

# MAFUNSO NDI MAYANKHO



Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Ambuye Yesu, ndife othokoza kwa Inu mmawa uno chifukwa cha mwayi kuti tabwera mu Kukhalapo Kwanu, ndi nthawi iyi ya chiyanjano, ndi kudzakhala pano mmalo ammwambamwamba mwa Khristu Yesu. Tsopano, Ambuye, ife tikupemphera kuti Inu mupitirize kukhala ndi ife pamene ife tiziyankhula za Inu. Mulole mitima yathu ikhale yodzaza ndi chimwemwe pamene ife tiziyang'ana pa Mawu Anu ndi malonjezo Anu kwa ife. Adalitseni abusa athu, othandizira athu, abale onse ndi alongo amene amabwera kuno kuti adzakomane ndi ife ndi kudzasonkhana kuno mu malo aang'ono awa amene ife tawakonzera kuti akhale malo okumaniranapo kwa Inu. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutidalitse ife mu chirichonse chimene ife titi tichite kudutsa mu tsikuli. Mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Amenii. (Mukhoza kukhala pansii.)

[M'bale Branham ayakhulana ndi winawake pa nsanja—Mkonzi.]

<sup>2</sup> Izi zakhala ngati kupepuzidwa kochepe kwa ine pang'ono pokha. Ine ndinali ndi misonkhano kumbuyo kuno, zokambirana; ine ndimayenera kuti ndikhale ndi zokambirana zapadera kapena mwina—k—kapena kuti nditenge ndi kuyankha mafunso. Pafupifupi chirichonse chimene chimabwera mmawa uno chinali masomphenya, ndipo ine ndinakhala ngati ndina...ine ndinamuza Billy, ngati M'bale Neville sanali wotangwanika kwambiri, ine ndikatenga mulu wa mafunso awa ndi kuwayendetsa apa, kukhala ngati kupeputsa malingaliro anga pang'ono. Izo...zimakhala ngati zimandiponyera ine pansii, kukhala...Iwo—masomphenya amenewo ndiwo...Koma anthuwo anathandizidwa; ndicho chinthu chachikulu. Chinthu chenicheni, iwo anathandizidwa; nd—ndiro gawo labwino. Ndipo kotero, ndiye ine ndidzawatenganso iwo molawirira pang'ono madzulo ano, kuti ine ndithe kuyamba madzulo ano pa zoyankhulana, zapadera.

<sup>3</sup> Tsopano, ndife okondwa mmawa uno kuwawona abwenzi athu ndi...Tsopano, izi...Musamutsutse nazo Billy izi. Kotero ndiye...Iye amayenera kuti awadziwitse anthu ngati ine ndinali woti ndipitirira kuyankha mafunso awa. Ine ndimaganiza izo zikanandipatsa ine, mwinamwake o—ora kapena chinachake kuti ndiyankhe mafunso amenewa. Zina zanga...ine ndimakonda...ine sindimakonda kuchokapo; ine ndimakonda kusesa mbale yanga mbee. Mukuona? Ndiye mafunso awa ndi zina zotero, i—ine ndimangofuna kunena kuti, i—i—ine ndafika pochita izi. Ine ndikakhala ndi zochuluka m...pa malingaliro anga; izo zimandipangitsa ine manjenje.

Ndipo ine sindikufuna kuti ndizikhala wamanjenje ndi china chirichonse; i—ine ndikupita Kwathu ku Ulemerero limodzi la masiku awa.

<sup>4</sup> Mzanga wakale wa ine ananena kwa ine masiku angapo apitawo, anati, “Ine ndikufika potopa kwambiri kukhala ndiri mu sutikesiyi.”

Ine ndinati, “M’bale wokondeka, ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe chinachake, ndipo ine ndifuna kuti ndikuuze iwe chinachake. Ine ndikupukwa kwathu. Ine ndakhala ndikupukwa kwathu kwa zaka makumi awiri, ndipo ine ndiribe kwathu koti ndizipitako.” Mukuona? Izo ndi zoono. Icho ndi chinthu choipa kuti uchinene. Ine ndimakhoza kukhala pansi ndi kumalira kuti ndipite kwinakwake kuli kwathu. Ine ndiribe kwathu koti ndizipitako. Kulikonse kumene ine ndimapita, ine sindimatha kukakhala kumeneko masiku pang’ono; ine ndimakhala wokonzeka kuti ndipite kwinakwake. Ine basi . . . ine ndakhala mwanjira imeneyo; i—ine ndinabadwa mwanjira imeneyo. Mkazi wanga amanditcha ine “Mphepo zosakhazikika.” Ine basi—ine ndimangokhala kuno ndi uko. Ndipo uwo ndi mpanipani woipa kuti uzikhala ulimo, koma ine ndikuganiza ine ndikuyenera kuti ndizikhala mwanjira imeneyo chifukwa cha utumiki wanga. Koma ambiri a inu mumasilira . . . Chabwino, ife timasilira kuchitira china chirichonse kwa Mulungu, koma inu musadzati konse . . .

<sup>5</sup> Tsopano, ife tangokhala kagulu ka anthu akwathu mmawa uno. Mukuona? Koma i—ine ndikupukwa kwathu. Ine ndikufuna kupita kwathu, ndipo ine sindikudziwa koti ndipite. Inu mukuti, “Nanga bwanji kupita ku Arizona, banja lanu liri kumeneko?” Ine ndimakakhalako bwino kwa masiku awiri kapena atatu, ndipo ine ndimayenera kuti ndipite kwinakwakenso. Ndipo ine ndikapita kumeneko, ndiyeno ine ndimakakhalako bwino kumeneko masiku awiri kapena atatu, ndipo ine ndimayenera kuti ndipite kwinakwakenso. Koteru palibe kwathu koti ndizipitako, ndipo ine ndikupukwa kwathu.

<sup>6</sup> Chabwino, kulipo Kwathu. I—ine ndidzapita kumeneko nthawiina, koma ine ndiyenera kuti ndikuthandizeni inu poyamba. Mukuona? Ndi chimene ine ndadzera pano, nkuti ndidzakuthandizeni inu. Ndipo mpakana nthawi imeneyo ifike, mpakana ine sindingathenso kukuthandizani inu, ndiye i—ine ndikufuna ndizipita Kwathu. Ine ndikufuna ndipite Kwathu kwenikweni ndiye. Koma alipo Malo kwinakwake amene ine nditi ndidzawakonde kwambiri, ine sindidzafuna kuti ndidzabwerere kuno.

<sup>7</sup> Ine ndimachoka ku Jeffersonville; ine ndimakhala nditachoka kwa masabata pang’ono; ine ndimafuna nditabwereranso kuno. Ine ndikapita ku Arizona; ine ndimaganza kuti ndi kodabwitsa; ine ndimafuna kubwereranso

kuno. Ine ndikapita kwinakwakenso; ine ndimafuna kubwereranso kuno. Ndipo ine kupita kuno, ndikapita uko, ndipo i...ndiye ine ndimaganiza kuti ndikufuna ndibwere kuno. Ine ndikafika kuno; ine ndimangokhala kuno masiku pang'ono, ndipo ine ndimakuwonani inu nonse; ine ndimafuna kuti ndipite kwinakwakenso. Mukuona, ine ndiri nawo ana anga amwazikana padziko lonse, ndi i—i...iwo amene ine ndawabalira kwa Khristu. Ndipo i...Ndiye ine ndiribe kwathu. Ine ndikufuna ndidzawatenge iwo onse palimodzi lina la masiku amenewa, mwawona, Atate adzatero, ndiyeno i—ife tidzakhala nako kwathu kumene ife sitimadzangozungulira aponso. Mukuona? Kutopa ndi kuyendayenda ndi wopanda malo oti uzikhalako.

<sup>8</sup> Ndipo ine ndingamulangize aliyense, kuti asadzakhale konse mwala wogudubuzika (mwawona?), kupatula ngati utakhala utumiki wa mtundu wina umene ukukuitanani inu mwanjira imeneyo, chifukwa...i—ine ndingati ndipereke chirichonse, mmawa uno, ngati ine ndikadakhala nawo malo kuno mdzikoli omwe ine ndikanatha kupitako, ndi kuti, “Kuno ndi kwathu!” I—ine...Ngati ine ndikadakhala nawo iwo, ine ndikadapereka madola milioni. Ngati ine ndikadakhala nawo malo omwe ine ndikanati, “Mnyamata, ine ndikuwakonda awa basi kwambiri; ine sindikufuna kuti ndiwasiye iwo kenanso,” i—ine ndikapereka chirichonse. Koma i—ine sindikutha kuwapeza iwo.

<sup>9</sup> Ine ndiri chinachake momwe Abrahamu analiri; ine ndikufunafuna Mzinda. Mukuona? Ine sindikutha kuwapeza iwo, koma ine ndikudziwa kuti ulipo. Koma ine ndithudi sindikutha kudziyanjanitsa ndi malo ena aliwonse pa dziko lino. Izo basi sizikuwoneka ngati...Anthu abwino, malo abwino, ndipo iwe ukapita uku, ndi konyowa kwambiri; ukapita kunja uko, ndi kouma kwambiri; ukapita kuntunda uko, ndi kozizira kwambiri; ukapita kumusi uko, ndi kotentha kwambiri. Mwawona? Ndipo iwe...Palibe malo; si Kwathu basi. Sindikufuna kuti nditenge nthawi yanga kulirira pa phewa lanu, koma ine... .

Chabwino, ife tiri othokoza kwambiri kwa Ambuye. Amenii! Khalani othokoza chifukwa cha zinthu zonse. Ine ndiri motero, chifukwa ndine wotero. Mulungu anandipanga ine chimene ine ndiri. Ndipo ine sindingathe kukhala chirichonse koma chimene Iye anandipanga ine, wozingwa, ndi zinthu za mtundu umenewo. Iwo akundiiza ine kuti ndizingokhala mwanjira imeneyo kuti ndikakhale thandizo limene Iye ananditumira ine kuno kuti ndidzakhale. Ndipo ine ndikufuna kuti ndikhale munthu wa mtundu umenewo. Ngati umo ndi mmene ine ndikuyenera kuti ndikhale ndiri, ndi chimene ine ndikufuna kuti ndikhale. Chirichonse chimene chiri chifuniro cha Ufumu wa Mulungu, kapena chifuniro cha Mulungu, ndi chimene ine ndikufuna ndikhale ndiri.

<sup>10</sup> Tsopano, tiyeni ife tipemphere kachiwiri. Ambuye Yesu, mafunso awa ayikidwa patsogolo pathu apa, Atate. Ine sindingathe kuwayankha iwo, Ambuye. I—ndine wosakwanira pa mafunso amenewa, koma ine ndikudziwa kuti Inu ndinu wokwanira mu zonse, chifukwa izo ziri pa mtima wa anthu. Ndigwiritseni ine ntchito, Ambuye, kuti ndikapepusitse kupsinjika kwawo, simutero Inu, Atate? Mu Dzina la Yesu Khristu ine ndikupempha izi. Ameni?

Tsopano, ife tiyambira pa...ine ndikuganiza iwo sakujambula izi, kotero izo zangokhala...Izo zonse ziribwino, ine ndikuganiza.

<sup>11</sup> Tsopano, chinthu chimodzi chimene...Chifukwa chimene ndimadandaula za mafunsowa, nthawizonse pamakhala chinthu chimodzi chokongola...chinthu chowawa, kani, chimene nthawizonse chimandisautsa ine: chimenecho ndicho kuyankha funso la chikwati ndi chilekano. O mai, kuitana kwa lamy, makalata, ndipo m'bale wina anazikulungiza yekha mu bulangeti ndi kudzakhala pakhonde langa kuyambira 12:00 koloko mpaka masana mmawa wotsatira. Atumiki akuitana kuchokera kulikonse, okwatira kawiri kapena katatu ndi onse. Utumiki...ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu chinthu chimodzi. Ine ndikadali nawo angapo a iwo apa, ine ndikudziwa. Ine sindinawayang'ane modutsa iwo, koma alipo ochulupa a iwo apabe mkati umu.

<sup>12</sup> Zikumbukira kokha ichi! Kwa inu anthu amene muli okwatira, ndipo munalekana, ndipo munakwatiranso, ndilonjezeni ine chinthu chimodzi. Mukuona? Inu mwaika chidaliro chanu mwa ine. (I—ine ndikulingalira kuti izi sizikujambulidwa. Ine sindiri...) I—i—inu muli...inu mukundikhulupirira ine ngati mneneri wanu wotumidwa kuchokera kwa Mulungu, wantchito wanu, ndiye inu mutenge mawu anga pa izi, kodi inu mutero? Kapitirizeni kumakhala basi momwe inu muliri. Inu musati mukayesere china chirichonsecho monga icho, koma kakhaleni, muzingopitirira, muzingokhala okondwa. Inu muli...Inu ndi opulumutsidwa. Ngati inu muli Akhristu, zingopitirirani kumakhalira moyo Khristu; Iye anali nacho chifukwa chokupulumutsirani inu.

<sup>13</sup> Tsopano, pamene ine ndidzabwereranso, Ambuye akalola, ine ndidzafotokoza zimenezo kwa inu mu Baibulo. Mwawona? Ndipo musati mukhale okhumudwa. Amuna ambiri andiua ine, anati, “Chabwino, ine ndimamukonda mkazi wanga, koma i...ine ndikuyenera basi kuti ndimusiye iye; i—ine sindikufuna kuti ndiuphonye mkwatulo.” Inu musati muchite zimenezo! Khalani basi momwe inu mulirimo mpakana inu mudzamve kuchokera kwa ine kachiwiri (mukuona?) pa phunziro ili. Ndiye pamene ine...ine sindingathe kufotokoza izo mu maminiti khumi kapena khumi ndi asanu; izo zidzatenga nthawi ina kuti ndizifotokoze zimenezo, chifukwa liyenera kukhala liri Lembu.

Ziyenera kukhala ziri PAKUTI ATERO AMBUYE. Ngati si choncho, si zolondola.

<sup>14</sup> Ine ndikudziwa mafunso awa amene Yesu ananena apa, “Ngati mwamuna amusiya mkazi wake ndi kukwatira wina kupatula pa chifukwa cha chiwerewere achita chigololo, aliyense amene akwatira iye wosiyidwayo, azikhala mu chigololo”. . . Zinthu izi, Iye anali ndi chifukwa choti anenere zimenezo. Iye anali Mulungu; amenewo ndiwo Mawu Ake.

<sup>15</sup> Tsopano, tiyeni tibwerere mmbuyo ku chiyambi ndi kukapeza chomwe zonsezi zikutanthauza, inu mukuona, ndiye ife tizitulutsa izo apo. Koma mpakana ife titachita zimenezo, zingopitirirani momwe inu muliri pakali pano, basi momwe inu mwakhala mukuchitira nthawizonse, ngati inu muli Akristu. Ngati inu muli banja la Chikhristu, ndipo inu munakwatirana, ndipo muli ndi ana, ndi zinthu monga izo, zilumikizano zina zazing’ono zimene zikukumangani inu, musati mumusiye mkazi wanu kapena mwamuna wanu tsopano. Musati muchite zimenezo. Mukuona? Dikirani mpaka inu mudzandimve ine kachiwiri pa phunzirolo. Kodi inu mundilonjeza ine zimenezo? Kwezani mmwamba dzanja lanu! Tsopano, inu mwandikalira ine kuti mundikhulupirire ine. Tsopano, i—inu mwandikhulupirira ine mpaka apa; tsopano, ndikhulupirireni ine mopitirira pang’ono basi pa phunziroli.

Ts—tsopano, tiyeni tiwone, ine ndiri nawo abwino kwenikweni apa mmawa uno, ena . . .

**325. Kodi onse amene akupita mwa Mkwatibwi afunika azikhala mkati mwa mailosi fiftini handiredi kwa kachisiyu** (ine ndikukhulupirira ine ndinali nalonso ilo Lamlungu lapitali. Ine ndiyenera kuti ndizingowatenga iwo ndi kuwagwiritsa iwo ntchito mmene ine ndingathere.)—**mailosi fiftini handiredi kwa kachisiyu, monga mmene zikumvekera ngati pa tepi yachiwiri ya “Kwawo Kwa Mtsogolo Kwa Mkwatibwi”?** Ine nthawizonse ndinkaganiza kuti Mkwatibwi adzabwera kuchokera ku zigawo zonse za mdziko pa nthawi ya mkwatulo. Kodi ine ndikulakwitsa?

<sup>16</sup> Ayi, mzanga wokondeka, inu simuli kulakwitsa, inu mukulondola. Tsopano, ngati ine ndinanena chirichonse pansu pa tepi chimene chingakutsogolereni inu kuti mukhulupirire . . .

Tsopano, ine ndiribe . . . Onse awa ndi atsopano kwa ine tsopano, ine sindinayambe ndayang’ana umu—mu awa apa. Inu mukuona? Awa ndi mulu watsopano umene ine ndinautenga Lamlungu lina lija, ndipo ndinawabwezeretsanso iwo mu envelopu iyi, ndipo ndinakaziyananso izo mmenemo.

<sup>17</sup> Tsopano, mu ili . . . Ayi, Mkwatibwi sakusowa kukhala pa malo ena ake. Ambiri a iwo adzakhala ali mu fumbi la dziko lapansi. Iwo adzakhala ali kuzungulira dziko lapansi; iwo

adzakhala atapanga chisanu mu—chisanu cha kumpoto, n—ndi fumbi la mu nkhalango zotentha, n—ndi konsekonse kuzungulira mdziko. Koma pamene Lipenga la Mulungu lidzawomba, akufa mwa Khristu adzauka, kuukitsidwa, ndipo adzatulukira kuchokera mu fumbi la dziko lapansi, ziribe kanthu komwe iwo ali. Ndipo tsopano, mu izi, chiukitsiro chidzakhala chiri cha konsekonse. Mwawona? Kulikonse cholengedwa chirichonse pa mpira wa dziko lapansili amene ali mwa Khristu adzatulukira apo limodzi ndi Iye pamene Iye akubwera (mukuona?), ziribe kanthu kumene inu muli.

<sup>18</sup> Tangoganizani za malo achiwonetsero mu masiku a ofera oyambirira, apo pamene Akhristu awo anali kuponyedwa mu khola la mikango, ndipo mikango iyo inkawapha Akhristu ndi kuwadya matupi awo. Mukuona? Komabe iwo anamwazikana, matupi awo anali mu ndowe za mkango pa nkhope ya dziko lapansili. Ziribe kanthu komwe iwo ali, inu simungathe... Onani, inu munapangidwa ndi zinthu zimene ziri zosawoneka kupangidwa zogwirika, ndipo Mulungu a—adzawapatsa awo—zipangizo zimenezo mobwezeretsa. Mukuona?

<sup>19</sup> Tsopano, monga ngati inu mukatenga k—khungu. Inu mukaliswa ilo kuchokera ku khungu, ndipo iko kamabwera ndiye ku—khungu mu khungu, ndipo mpaka mu atomu, ndi molekyulu, ndi kupitirira mmusi monga choncho; ndipo potsiriza izo zimatsirizira kukhala zosawoneka. Izo zimapita kuchokera ku chachirengedwe, chinachake chimene iwe ungaike manja ako apo, kupita ku mipweya; kuchokera ku mipweya kupita ku zidulo—zidulo kupita ku mipweya, ndi mipweya, kupitirira mobwera monga choncho, mpaka potsiriza zonsezo zimakathera ku chinthu chimodzi chaching'ono, ndipo chimenecho ndi mzimu. Ndipo mzimu uwu umene ukukhala mu mipweya iyi. . . Iyo ikhoza kusakhala mipweya yofanana, koma mapangidwe a chimene inu muli zidzakhala ndendende zimene izo ziri kachiwiri. Mukuona? Mzimu wazilamulira zimenezo.

<sup>20</sup> Ndipo tsopano, mwa kuyankhula kwina, pamene inu munakhala mwamuna wamng'ono kapena mkazi, ndi monga, Mulungu amatenga chithunzi cha inu... Tsopano, ziribe kanthu momwe inu muliri wokalamba ndi wamakwinya, ndi wosawoneka bwino, chirichonse chimene chiti chidzakhale chiri, zimenezo zidzapitirirabe mpaka pansu kudutsamo. Ndipo thupi limenelo likhoza kukhala litawonongedwa, kupundulidwa, kuwotchedwa, kudyedwa ndi mikango, chirichonse chimene chiri, koma ilo linapangidwa ndi mipweya, zipangizo sikisitini za dziko lapansi. Ameneyo anali kashiamu, ndi potashi, ndi mafuta, ndi kuwala kwa dziko, ndi zina zotero, zonsezo zimayendera palimodzi kuti zilipange thupilo. Tsopano, ziribe kanthu, izo. . . Dziko lonse ndi lodzaidwa nazo zimenezo.

<sup>21</sup> Koma tsopano, chithunzi ichi ndicho chinthu chachikulu. Ndiye mu chiukitsiro, mipweya imeneyo, ndi zidulo, ndi zinthu

zidzabwereranso kumene mu malo ndi kuchipanganso chithunzi ichi kachiwiri. Tsopano, chithunzi ichi sichinajambulidwe pamene inu munali usinkhu wa sikisitini, kapena eyitini, kapena zaka twente mwa ubwino wanu. Kodi icho chinajambulidwa liti? Kusanakhale maziko a dziko, icho chinakaikidwa mu kaundula wamkulu wa Mulungu. Ndiyeno, chinthu chokha chimene icho chinachita chinali kudziika chokha kuno kuti inu mupange kusankha kwanu. Mukuona? Ndiye inu munakhala wantchito wa Mulungu. Iye atadziwiratu zimenezo, zikumupanga Iye kukhala Wowombola, momwe ife takhala tikudutsira mu zimenezo.

<sup>22</sup> Ndiye chithunzi chimenecho chiri mwamtheradi. . . Ichi ndi chosatsukidwa. Gawo losatsukidwa la moyo ndi limene inu mukulikhalala moyo tsopano. Ndipo chirichonse, ngati pali chosatsukidwa, apo payenera kukhala chenicheni pasanakhale chosatsukidwachō. Chotero, ngati ichi ndi chosatsukidwa, payenera kukhala chenichenicho kwinawake. Ndipo ichi si chinthu chenichenicho; ichi ndi mthunzi wotsogolera chabe wa chinthu chenichenicho chimene chiri nkudza. Tsopano inu mwazimvetisa zimenezo?

<sup>23</sup> Kotero, ine sindikusamala zimene iwo angachite nanu; iwo sangathe kuwononga maonekedwe amenewo, chinthunzi chimenecho mu malo opachika zinthunzi a Mulungu kumwamba uko. Izo sizingathe kuchiwononga icho, icho chiri Kumwamba. Inu mukhoza kuliwotcha ilo, ndi kulidyetsa ilo kwa mikango, kuchita nalo ilo mulimonse momwe inu mukufunira kutero; ilo lidzatulukiranso apo kachiwiri motsimikiza basi monga ma thuu awiri ali foro. Motsimikiza basi monga Mulungu analiyankhulira ilo, ilo lidzatulukira apo. Kotero, ziribe kanthu kumene inu muli. . .

<sup>24</sup> Tsopano, ngati i. . . Ine ndikuganiza ngati inu mungaisewere tepiye. . . (ine sindikudziwa yemwe analilemba ilo; linalembedwapo, kachidutswa kakang'ono basi ka pepala ndi inki ya buluu, kolembedwa kuchokera mu kabukhu kolembamo. Kakuwoneka ngati kachita kung'ambidwa kuchokera pa ka—k—kabukhu kolembamo.) Koma kumbukirani, pa izi, m—mu funso ili tsopano, mu tepiye, ngati inu mungazindikire, ine ndinanena izi, chinachake pa izi (iwo mwina sangakhale mawu pa mawu tsopano, ngati mungafufuze tepi iyi ndi inayo): ine ndinati, “Mwa chitsanzo, ife tiri pano mmawa uno. Mzinda uwu umene ife tikukhumba kuti tiuwone udzakhala konsekonse mailosi fifitini handiredi.” Ine ndinati, “Kuti iwo ukanati ufikire kuchokera ku Maine mpaka ku Florida, ndi kuchokera ku Khoma la Nyanja la Kummawa mpaka mailosi eyiti handiredi kumadzulo kwa Mtsinje wa Mississippi, mailosi fifitini handiredi konse konse.” Ine ndinati, “Taganizani za zimenezo, pomwe pano mmawa uno, pali anthu omwe akhala pomwe pano a—amene abwera kwenikweni kuchokera ku mtunda wochuluka chotero, kuchokera ku mailosi fifitini handiredi konse konse, akhala

muno pano.” Tsopano, ine sindikudziwa kumene Kachisiyo ati adzakhale ali pa dziko lapansi, koma ine ndiri nalo lingaliro kuti Kachisiyo adzakakhala pafupi kumene kuli Palestina tsopano. Pamenepo mwinamwake padzakhala pali pamwamba pa phiri pomwe kumenekoko. Iwo uzidzafika konse. Ndithudi, uko sikudzakhalanso kuli nyanja apo. Mukuona, dziko ili liri mailosi 25,000 kulizungulira ilo, koma mailosi fifitini handiredi si ochulukwa kwambiri kuchokera pa awo. Koma Mzinda waukulu uwu udzakhala pa mailosi fifitini handiredi a konse konse awa pa phiri.

<sup>25</sup> Tsopano, chifukwa chimene ine ndikukhulupirira zimenezo ndi chifukwa cha mauneneri ndi zinthu zokhudza Phiri la Zioni mu Yerusalemu ndi mizinda imeneyo. Ndipo kumeneko ndi kumene Abrahamu mneneri anali kuufunafuna Mzinda umenewo, ndipo iwo unali umene Woumanga wake ndi Woupanga anali Mulungu. Iye anali kufunafuna Mzinda umenewo mu dziko limenelo. Ine ndikukhulupirira iwo udzakhala uli kumene dziko ilo liri.

<sup>26</sup> Dziko limenelo, inu simungalipeze nkomwe ilo pa mapu. Ilo ndi kadontho kakang’ono kwambiri. Ndipo kuyang’ana pa dziko ilo Russia, ndi United States, South America, ndi malo onse awo kumeneko. . . Nchifukwa chiyani Mulungu anali wokhudzidwa kwambiri nao malo amenewo (mwawona?), ndi malo amodzi amenewo? Limenelo ndiye funso. Ine sindingathe kutsimikizira izo, koma izo zikungowoneka motero kwa ine. Koma kulikose komwe kuli, ife talunjika njira imeneyo, koteri Ambuye alemekezeke chifukwa cha zimenezo.

<sup>27</sup> Tsopano, ngati inu muli ndi kukhudzidwa kuti i—kuti ine ndinanena kuti kudzakhala mwa. . .kuzungulira mailosi fifitini handiredi a ku kachisiyo, uko kunali kukhudzidwa kolakwika (inu mukuwona?), chifukwa izo sizidzatero. Kachisi uyu ali ndi. . .Ano ndi malo aang’ono chabe amene ati adzawonongedwe. N—ndipo dzikoli lidzawotchedwa, ndipo izi zonse zidzathetsedwa. Ndipo Indiana uyu, ndi United States, ndi chirichonse zidzangosungunuka ndi kunyembeterera kutali osakhalanso kanthu koma chiphalaphala chamoto. Mwawona? Tchimo lonse, matenda onse, majeremusi onse, chinthu chirichonse chidzawonongedwa. “Ndipo ine ndinawona Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano, pakuti loyamba. . .”

<sup>28</sup> Ganizani! Mulungu anali zaka sikisi sauzande akulimanga dziko limeneli, akuliyika ilo palimodzi, akulipanga ilo. Kodi Iye anachita motani izo? Baibulo linati, “Iye analipanga ilo kuchokera ku zinthu zomwe sizimawoneka”; ndiko kuti, Iye analilenga dzikoli. Tsopano zindikirani; izi ndi zokongola. Mlengi yemweyo amene analilenga dziko lapansili pa cholinga (Satana analidetsa ilo), Iye anabwera pansu kuti adzawombole zimene zinatsalirapo kuno. Ndipo Iye anapita kwinakwakwenso ndipo ali mu ntchito Yake panobe akulenga.



<sup>29</sup> Tsopano, izo zinamutengera Iye zaka sikisi sauzande kuti apange—dziko lapansi, ndipo Iye akuti atenge masiku awiri kuti alenge Mzinda umene ukupita pa dziko lapansili. Iye ali... “Mu Nyumba ya Atate Anga muli zinyumba zambiri: ngati zikanati zisakhale choncho, ine ndikanati ndikuuzeni inu. Ine ndikupita kuti ndikakukonzereni inu malo (kukamanga mzinda kuchokera mu golide wowonekera, misewu ya golide).” Malo okongola akewo.

Kodi Iye akazitenga kuti izo? Kodi kuli zipangizo zirizonse ku maiko ammwamba enawo, kapena miyezi, ndi nyenyezi, ndi zinthu? Iye sakusowa kuti achite kukhala nazo, Iye ndi Mlengi. Iye anapita kuti akaumange Mzindawo. Amen! Zimenezo ndi zokwanira bwino kwa ine, sichoncho kwa inu? Zimenezo ndi zabwino. Pakuti ngati Iye analimanga ili, ndipo ine ndikukomedwa nalo ili, zidzakhala bwanji pamene Iye ati adzamange latsopano ilo? O, mai, chinthu chodabwitsa chakecho. Ndipo kotero ine ndi wokondwa kuti ife tikupita ku Mzinda umenewo. Chabwino.

**326. M’bale Branham, ine ndimawakonda Ambuye, koma kwa chaka chapitachi ine ndakhala ndiri—ine ndakomana ndi vuto. Zimawoneka kuti nthawizina ndakhala ndiri pafupifupi kusokonezeka malingaliro anga. Kodi ndi chiyani icho? Chonde ndipempherereni ine ndi amuna anga.**

<sup>30</sup> Chabwino, ngati palibe... Ngati munthu uyu anali pa zokambirana zapadera, monga anthu inu mwakhala muli mmenemo mmawa uja, uko kukanakoka izo nkuzitulutsa chimene izo ziri, chirichonse chimene chiri. Mukuona? Ambuye akanati aulule chimene icho chiri. Koma tsopano, pakuti ine sindikudziwa yemwe inu muli, ndipo inu simuli pano; ilo langoti, “Mlongo mwa Khristu.”

<sup>31</sup> Tsopano, tsopano, ngati izo ziri... ngati pali chinachake chimene inu mwachita chimene chiri cholakwika, chimene chikukusautsani inu, ndiye chifufuzeni icho ndi Baibulo ndi kuwona chimene inu mukuyenera kuchita. Koma ngati inu simunapange chirichonse ndipo inu simuli kutsutsika ndi chirichonse, mwinamwake ndi misempha yanu. Mukuona? Izo zikhoza kukhala zinthu zambiri zimene zinachitika: mwinamwake vuto lina kale mmoyo wanu. Mwinamwake ndi—mkazi kuno akhoza kukhala kuti ali mu nthawi ya kusintha kwa thupi. Ndi pamene chirichonse chimakhala cholakwika ndi iye, ndipo apo palibe kanthu kolakwika ndi iye, komabe chirichonse ndi cholakwika kwa iye. Ndipo sikuti akungodzipangitsa, iye akumvereradi kwenikweni zimenezo; ziri basi ngati zenizeni. Munthu aliyense amene ali wamanjenje amakhala mwanjira imeneyo. Ndipo musati mumutsutse.

<sup>32</sup> Ndipo inu amuna kwa akazi anu, pamene iwo ali mu nthawi imeneyo ya moyo, ngati inu munayambapo. . . ngati iye anayamba wakhalapo wapamtima wokoma wanu, inu mumulole iye akhale apo pomwe, chifukwa iye akukusowani inu. Iye akusowa kwenikweni thandizo lanu; iye akusowa winawake woti amuthandize iye, ndi kumamumvetsa iye. Ziyankhulani naye iye, munyamuleni iye mu mikono yanu mo—monga—ngati kuti iye anali wapamtima wokoma wanu, ndipo iye azikhala ali. Ndipo—ndi kumamvetsa iye, chifukwa iye akudutsa mu nthawi imene mapangidwe ake onse ali kusintha, ndipo inu mukuyenera kumakhala wabwino kwa iye pa nthawi imeneyo.

<sup>33</sup> Ine ndikuganiza ndi chifukwa chake Bambo Rockefeller anapanga kulakwitsa koopsya. Iwo anakondedwa ndi fukoli, mwina akanakhala purezidenti wathu wotsatira. Koma pamene akazi awo anali kusintha mu thupi, nalowa mu kusintha kwa thupi, ndipo iwo anamusiya iye ndipo anakwatira mlembi wao, inu mukuwona zimene zinachitika? Izo zikusonyeza kuti akadalipo Achimereka oganiza bwino panobe.

Tsopano, ine ndimawakonda Bambo Goldwater, k—kapena Bambo. [M'bale Branham akukhwatchitsa zala zake—Mkonzi.] Rockefeller. Iye ndi. . . ine ndimawakonda Bambo Goldwater nawonso; ine ndimamukonda aliyense. Koma i—ine sindikufuna kuti. . . Ena a inu—ena a abale anga achi Republican akhala uko komwe akundimva ine ndikunena zimenezo, i. . .

<sup>34</sup> Zindikirani, koma ine si wa ndale, i—ine ndikufuna kuti ndikhale Mkhristu. Mukuona? Ndipo ano si malo a ndale. Mukuona? Chinthu chonsecho chapita mulimonse, mwanjira imeneyo, koma ichi chimene ife tikuchikambachi ndi Chamuyaya. Democrat kapena Republican. . . O, ndi chisokonezeko chotero; izo sizingakhoze kuwomboledwa konse. Izo zatha, kotero musati muzisutsana za zimenezo. Chinthu choyenera kuti muzichita ndi kukhalira moyo kwa Ufumu uwu. “Pakuti kuno ife tiribe mzinda wopitirira, koma ife tikufunafuna Wina uli nkudzawo.” Ameni! Uko nkulondola. Inde, bwana!

<sup>35</sup> Kotero ndale ziri kumbali imodzi ya mpanda, ndipo ine ndiri ku mbali inayo. Ine ndinati, “I—ine ndinavota kamodzi; kameneko kanali kwa Khristu; ine ndikutsimikiza kuti tipambana.” Uko nkulondola. Mukuona? Inu muli ndi voti imene ikubwera. Mukuona? Mulungu anakuvoterani inu, ndipo mdierekezi anavota mokutsutsani inu. Tsopano, kumbali imene inu muti muponyerereko voti ndi kumene inu muti mutulukireko.

<sup>36</sup> Kotero tsopano, ine ndikukhulupirira munthu uyu ali basi. . . Ine ndikuganiza kuti awo ndi manjenje chabe. Ngati palibe chirichonse chikukutsutsani inu, zipitirirani nazo ndi kungonena kuti, “Pita kutali ndi ine, Satana!” Zingosunthani

mtsogolo basi. Tengani kuyambitsako ndi kumamukhalira moyo Mulungu.

**327. Tsopano. Kodi pali chikhalidwe chirichonse chomwe chiri chovomerezeka kuti ukwatirenso pambuyo pa chilekano, molingana ndi** (Tsopano, ine ndiwona ngati ili liri... Ine ndikuganiza kuti pali mafunso awiri kapena atatu pa ili.)—**molingana ndi Malemba? Ngati ine sindikhala—ngati ine sindikhala ndikanali wokwatira mu ku... kuchokera ku nthawi za mmbuyo, ndi...kodi pali malo ena aliwonse a chilekano amene amakuloleza iwe ngakhale kuti ukwatirenso? Ine ndikhala—ine ndikhala (n-d-i-k-u... n...ndigula tepiye (Eya!) kuti ndipeze yankho ili. Zikomo inu mochuluka kwambiri. Ine ndidzaifunafuna iyo Lamlungu.**

<sup>37</sup> Chabwino tsopano, ine ndanenapo izi, inu mukuona. Musati—musati...i—i...Ndiroleni ine ndingozisiya izi zokha (inu mukuona?) mpaka ife tidzafike pa malo pamene... tsopano pamene ife tidza...izi zonse zidzakhala zitawongoledwa. Ndipo tsopano, inu mungokumbukira, zimenezo ndi Mulungu akalola, mwamsanga pamene ine ndidzabwerera kuno. Nthawi yotsatira ine ndikadzabwera, Ambuye akalola, ine ndidzalalikira pa phunziro limenelo. Mukuona? Ndipo tsopano...Ndiyeno, ife tidzazijambula izo mulimonse. Ndipo ngati—ngati izo ziti zidzapweteka, izo zidzapweteke; ngati izo zidzakonza zonse, izo zidzakonze zonse. Koma inu mungokhala olimbantima bwino. Mukuona?

**328. Okondeka M'bale Branham, kodi ndi zotheka kuti wina akhale nao ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kusakhala nazo zizindikiro zikumutsatira, b—bola osati mpakana ku... nthawi ina yamtsogolo ndi zifukwa zoikidwa ndi Mzimu?**

<sup>38</sup> Tsopano, ilo likhoza kumveka ngati funso losakanizika, koma ilo ndi labwino, labwino kwambiri. Mwawona? Tsopano, apa zikundipatsa ine mwayi pang'ono, kuti ine ndapeza kuti izo zikugwira ntchito ndi langa—banja langali pano tsopano (mukuona?), ine ndikutanthauza inuyo, banja langa, ndi banja kunja uko ku dziko kumene ife... kumene matepi athu amapita.

<sup>39</sup> Tsopano, gawo lalikulu la osonkhana anga ali opangidwa ndi anthu Achipentekosite, ndipo chifukwa Pentekosite ndi uthenga wa posachedwapa umene ife tiri nawo mu zigawo zazipembedzo. Ndipo kwa ine, ine ndithudi ndimagwirizana nawo iwo kwambiri kusiyana ndi mpingo waachipembedzo uliwonse. Ine ndimakangamira chaku Chipentekosite, chifukwa iwo n...ndiwo uthenga wa posachedwapa. Ndipo owatembenuza anga onse amene ine ndimawabweretsa kwa Khristu, ine ndimayesera kuti ndiziwalondolera iwo ku mpingo wina wa Chipentekosite. Koma ine ndawazuzula iwo mwanjira iliyonse yomwe ine ndimaidziwa kuchita kwake, kuti iwo anali

kulakwitsa mu Lemba pokhala achipembedzo ndi posalolera kuti aziyenda mu Kuwala pamene Kuwala kunaperekedwa kwa iwo. Komabe, ngati ine ndikanati nditenge kusankha kwanga lero kuti nditenge mpingo uliwonse mu dziko, ine ndikanatenga Chipentekosite pamene zifika ku achipembedzo. Koma zikafika kwa anthu pawokha, monga amuna ndi akazi, muli Akhristu enieni mu zipembezo zonsezo: Methodisti, Baptisti, Chipresibateria, Chilutera, ndi zina zotero. Koma ine ndikunena za kachitidwe komwe anthu amenewa alimo, osati konse munthu payekha, koma kachitidwe komwe anthu awa akodwera nako mu chipembedzo chawocho. Iwo amamvetsa izo bwino bwino tsopano (mwawona?), zimenezo i—ine ndikuganiza anthu... Ngati iwo ali a Chiroma Katolika, Mboni za Yehova, Ayuda achi Orthodox, aliwonse amene ali, zimenezo ziribe vuto kwa ine; koma ndi anthu pawokha amene Khristu anawafera kuti awapulumutse.

<sup>40</sup> Ndipo tsopano, i...Ndipo kugwirizana ndi kachitidwe kawo kamene iwo alimo...Ine ndikukhulupirira kuti alipo basi Akhristu ambiri kunjira uko mu Baptisti, monga amene alipo mu Methodisti, kapena Chipresibateria, kapena chinanso chirichonse. Iwo ndi Akhristu, okhulupirira enieni. Ndipo uko komwe mu mpingo wa Chiroma Katolika muli anthu enieni mmenemo amene ali amuna enieni ndi akazi amene amawakonda Ambuye. Ndipo iwo samajowina mpingo umenewo kuti akhale olakwitsa, iwo amaujowina iwo kuti akhale olondola. Koma ndi kachitidwe mmenemo kamene kamawalondolera malingaliro awo njira yolakwika. Ndipo ngati ingafike pa nthawi yoti ine ndipange chipembedzo, ine ndangamakunyengeni inu ndi kuti ine ndakubweretsani inu mu kachitidweko; izo zikhale kutali ndi ine. Ndipo Mulungu andisunge ine mu malingaliro anga olondola kuti ndizikulondolerani inu kwa Yesu Khristu, Mawu. Kumakhala muli ndi Amenewo. Mukuona?

<sup>41</sup> Koma tsopano, munthu uyu apa akufunsa funso la momwe zingathekere kuti ukhale ndi ubatizo wa Mzimu Woyera popanda zizindikiro zikuwatsatira iwo. Tsopano, izo zikanati... Ngati inu muli obadwa kachiwiri, inu muli...Ngati inu muli obadwa poyamba ngati munthu wokhalapo ndi munthu wokhalapo wabwinobwino...Tsopano, ine ndikuyankha izi mwa—m—mwanjira ya umwana weniweni yochitira izo. Koma ngati inu mwabadwa muli munthu wokhalapo wabwinobwino, inu makamaka muzichita zinthu zimene munthu wokhalapo wabwinobwino akanati azichita. Kodi uko ndi kulondola?

<sup>42</sup> Pamene inu mubadwa ngati munthu, zikhalidwe zachibadwa za munthu wokhalapo zizikutsatirani inu. Inu simumakhala mu mtengo, ndi kumayesera kuuluka ndi mapiko anu monga mbalame, k—k—kapena chinachake monga icho. Izo sindizo—uyo sakanakhala ali munthu wabwinobwino,

kachitidwe kabwinobwino ka munthu wokhalapo. Kachitidwe kabwinobwino ka munthu wokhalapo kangakhale kuti azigwira ntchito, akhale... akwatire, akhale ndi banja, ndi kumachita zinthu zimenezi. Zimenezo ndi zachibadwa, wabwino... munthu wabwinobwino, chifukwa inu munabadwa chimenecho. Ndiye pamene inu mubadwa Mkhristu, wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, inu mwachibadwa mumatenga zikhaliidwe za Khristu. Inu mukuona?

<sup>43</sup> Tsopano, ngati ife tikanatenga apa mmawa uno mwa osonkhana awa pamene anthu inu mwakhala pano ndi kumamvetsera tsiku ndi tsiku ndi zina zotero ku kuphunzitsa, inu mupezapo kuti inu mukanakhala muli osiyana wina kwa mzake, chifukwa inu—ndinu osiyana. Ndinu—mapangidwe anu ndi osiyana; zanu—zokonda zanu ndi zosiyana; i—inu mumadya mosiyana; koma inu nonse mumadya chakudya. Koma tsopano, basi kuyambira... Ndi munthu wokhalapo mmodzi aliyense monga ngati wina uyo, inu ndinu osiyana kwa winayo. Akhristu amachitanso chinthu chomwecho. Inu simunganene kuti, “Tsopano onse...” Kodi onse amayankhula ndi malirime, kodi onse amalosera, kodi onse...? Mukuona?

<sup>44</sup> Inu muyenera kumaziyang’ana zinthu zimenezi, chifukwa Mkhristu amatenga z—zizolowezi za Mkhristu; ndipo iwo amakhala moyo ngati Mkhristu. Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Zindikirani: “Mu Dzina Langa iwo azidzatulutsa ziwanda; iwo azidzatenga njoka kapena... kumwa zinthu zakupha; ndipo iwo azidzayankhula ndi malirime atsopano.” N—ndi zinthu zimenezo ndendende basi mochtika zikuwatsatira Akhristu.

<sup>45</sup> Tsopano, munthuyu ali ndi chinthu chabwino kwambiri apa: “...kapena kodi ife tiyembekezere mpakana nthawi yamtsoyolo kapena zofunikira zoikidwa ndi Mzimu Woyera?” Ine ndikuzikonda zimenezo. Mukuona? Tsopano kodi inu mwaligwira lingalirolo? Pamene ziti zidzaikidwe ndi Mzimu Woyera! Mulungu amaikiratu zinthu.

Ndipo pamenepo, ine ndikuganiza ngati anthu Achipentekosite akanati ayesere (amene akumvetsera kwa tepi iyi), inu mundimvetsa ine ngati inu mufika apa chifukwa chimene ine ndimasiyanira ndi inu mukamaumilira lingaliro lija loti iwo onse ayenera kuti aziyankhula ndi malirime. I—ine ndimalephera kuziwona izo bwinobwino, chifukwa izo zikanakhala... ine ndimakonda chitumbuwa cha nthuza, koma palibe chifukwa—ndipo ndine munthu wokhalapo—koma palibe chifukwa kuti ine ndiziyesera kumakuuzani inu, “Ngati inu simudya chitumbuwa cha nthuza, sindinu munthu wokhalapo.” Mukuona? Koma kudya chitumbuwa cha nthuza ndi chimodzi cha zizolowezi za munthu wokhalapo. Mukuona? Inu mukhoza kutsutsana nane pa zimenezo, k—koma izo—ndi

zoon. Tsopano, wina angamadye ichi, ndipo wina angamachite chinthu chinachakenso.

46 Tsopano, Mzimu Woyera umaika maudindo amenewa, koma pamene iwe uyesera kudzikakamizira wekha mu izo... Ngati ine ndikanati inu mukuyenera kuti muzidya chitumbuwa cha nthuza, nanga bwanji ngati chitumbuwa cha nthuzacho chimakupangitsani inu kusanza? Ndipo komabe, inu mungati musanze ndi kumayesera kuti mudye chitumbuwa cha nthuzacho ndi kusanza, ndipo...?.. Mukuona? I—inu—inu mukudzipweteka nokha, ndipo ndi mmene zimakhallira inu mukamayesera kuti muchite chinachake chimene chiri chosiyana kwa Mzimu. Iye ali ndi moyo wanu atauyika pa chinthu chinachake. Kodi inu mukumvetsa zimenezo? Mukuona?

47 Ndipo inu, pamene inu muli odzazidwa ndi Mzimu, apa pali chimodzi cha zizindikiro zopambana zimene ine ndikuzidziwa: inu mumakhala kwambiri mu chikondi ndi Khristu ndipo mumakhulupirira Mawu aliwonse amene Iye awanena kuti ali Choonadi. Mukuona? Umenewo ndi umboni woti inu muli nao Mzimu Woyera. Ndipo moyo wanu umakhala wodzaza ndi chimwemwe, n—ndipo o mai, chirichonse chimakhala chosiyana (mukuona?) kusiyana ndi momwe zinaliri. Umenewo ndiwo Mzimu Woyera.

48 Tsopano, mphatso zimenezi ziri mu Mzimu Woyera. Tsopano, ngati osonkhana awa mmawa uno, awa... tchalitchi chosaoneka bwino basi chodzaza ndi... (Zipinda zosefukira, ndithudi, zadzazadi.) Koma mu... Basi... (Popanda kulengeza kuti tikhala tikuyankha mafunso awa, koma anthu awa angobwera muno.) Zindikirani, ngati munthu aliyense mkati muno akanakhala mu mgwirizano wangwiro nao Mzimu Woyera, aliyense wa inu akanadzazidwa nao Mzimu Woyera ndipo ali mu chiyanjano nao Mzimu Woyera, zizindikiro izi zikanangokhala zikuchulukitsidwa pakati pa inu nthawi zonse (mukuona?); izo zikanakhala zikupitirira mosalekeza. Koma pamene pali chisokonezeko, pamene pali kusiyana, ndi pamene ife tikukhazikitsa, Mzimu Woyera sungathe kudzisuntha wokha. Inu mukuona? Iwo sungathe kugwira ntchito kudzera mwa anthuwo. Mukuona?

49 Ndipo apo, ngati ine ndikanati, “Tsopano inu, aliyense wa inu, kodi inu munayankhulapo mu malirime?”

“Eya.”

“Chabwino, inu muli nawo Iwo.” “Kodi inu munayankhula mu malirime?”

“Ayi.”

50 “Inu mulibe Iwo.” Tsopano, ine ndikudzipanga ndekha kukhala woweruza. Mulungu ali woweruza wa zinthu zimenezi.

51 Koma penyani, Yesu anati, “Zizindikiro izi zizidzawatsatira iwo.” Mukuona? Magulu amene amakhulupirira, chikhalidwe chonse cha Mzimu Woyera chimayenderera mwa iwo, ndipo iwo onse amakhala odzazidwa ndi chikondi, ndi chimwemwe, n—ndi kungokhala mtolo waukulu w—w—w—wa anthu odzazidwa ndi umulungu weniweni. Mwaona, umenewo ndiwo Mzimu Woyera. Ndipo mkati—mmenemo, iwo amayankhula ndi malirime pa nthawi yoti malirime awukapo (bwanji), kapena pakakhala kufunikira kwa iwo, iwo amayankhula ndi malirime. Ndipo ngati pali ulosi, iwo umayankhulapo. Ndipo o, izo zimangokhala ndendende zangwiwo nthawi iliyonse.

52 Afunseni anthu fifitini kapena twente awo amene anakalowa mkati umo mmawa uja pa kuyankhulana ngati panali mawu amodzi mulimonse, anasowa mwanjira iliyonse, ndi alendo mwangwiwo. Zimene... Mzimu Woyera unakumba kumene mpaka pansi mmenemo, ndi kuzipeza zinthu zimenezo, ndi kuzitulutsa izo kunja, ndi kuzinena izo kwa iwo. Mukuona, mwawona? Mulibe kulakwitsa mu zimenezo. Kuwauza iwo ndendende basi chimene *ichi*, ndi chimene *ichi* chinali, ndi chimene *icho* chiri, ndi chimene *ichi* chiri choti chichitidwe, ndi zinthu zonga izo, ndi zimene iwo anachita, ndi zimene iwo akuyenera kuti achite. Mukuona? Ndizo basi... Kuziyika izo basi mu dongosolo. Tsopano, iwo ayenera kuti achitepo pa zimenezo.

53 Usiku wina ine ndinali kuyankhula kwa banja, ndipo ine ndinali k—kunyumba kumene ife tinali ndi msonkhano, kapena basi—tinali titangokhala pozungulira tebulo tikuyankhula. Ndipo zonse mwakamodzi, Mzimu Woyera unatsikira pakati pathu, ndipo ine ndinanena kwa winawake pamenepo, “Ine ndinamuwona bambo *winawake*, ndipo iwo... iye anali atasokonezeka mu malingaliro mwake pokhudza zinthu zina,” ndipo ine ndinati, “monga mu chisokonezeko m—mu k—kuzindikira zamumtima.” Ine ndinati, “Tsopano, ziri pomwe pano tsopano.” Ine ndinati, “Ine ndikudziwa zimene inu mukuganiza.” Ndipo ine ndinapita mmbuyo momwe ndipo ndinangokatenga njira yozungulira apo ndipo ndinayankha funso lililonse limene mwamuna ameneyo anali nalo mu malingaliro ake kwa iye, kuti iye... Palibe aliyense amadziwa ngakhale zomwe ine ndinali kunena koma iyeyo. Mukuona? Koma iye anazigwira izo. Iye amadziwa kuti izo zinali za chiani. Inu mukuona? Ndipo zimenezo zinali chiani kwa iye? Kumusonyeza iye, kutsimikizira kwa iye kuti Mzimu Woyera unali kuululira kwa ine zimene zinali pa mtima wake. Inu mukuona? Ndipo ine sindinasowe kuti ndizinene izo kwa onse a iwo. Bamboyo akumvetsera kwa ine pakali pano. Tsopano, ndiko kulondola. Tsopano, inu mukuona momwe izo ziriri? Chimenecho ndicho chitsimikiziro.

54 Tsopano, ngati mpingo wonse ungagwire ntchito mogwirizana monga choncho, ndiye pakati pathu ife

tikanakhala tikutulutsa ziwanda, tikumatola njoka, kumwa zinthu zakupha, zinthu za mitundu yonse ziri kuchitika. Koma pamene inu muyesera kumakakamizira izo kwa payekha, ndiye iwe umadzipeza wekha... Chimenecho ndi Chipentekosite kachiwiri. Ndiye iwe umapeza Babeloni, chisokonezeko. Inu simungathe kuziweruza zimenezo. Mukuona? Mitima yathu ili yodzaza ndi chisangalalo ndi kukondwa, ndipo o, mai, mbalame zikuimba, c... Chirichonse chiri chodabwitsa, mai, tangodzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo ife tiri mu chikondi kwambiri ndi Yesu, ife tikufuna kuti tipemphere usiku wonse.

<sup>55</sup> Tsopano, ine sindikanati ndichititse manyazi gulu ili, kapena ngakhale inemwini kwa inu. Koma ine ndikudabwa, ngati ine ndikanati ndifunse mmawa uno ndi ndani mu gulu ili, kapena anthu awa amene anali nao Mzimu Woyera, mwina akanakhala magawo nainte-faifi pa zana a inu mukanakweza manja anu kuti munali nao Mzimu Woyera. Ndiye ine ndikanapotoloka apo ndi kukupatsani inu umboni wa Baibulo, umodzi wokha, umboni wa Baibulo; ndipo ine ndikukaika ngati pakanakhala dzanja limodzi kapena awiri akanapita mmwamba. Mwaona, mukuona? Zikanakhala basi... kungozimangiriza izo pa malo oterowo, koma pamene inu muchita zimenezo (mukuona?), iwe uli aponso kuwapweteka osonkhana anu. Koma iwe uyenera kuti uwachotse iwo mu ukhanda uwo ndi kuwafikitsa iwo mu ubambo. Mukuona?

<sup>56</sup> Monga winawake analemba funso tsiku lina, anali kuno, ananena za... ananena chinachake mokhudza M'bale Junior Jackson. Winawake anapita kumusi uko, ndipo iwo anati, "Inu mukumapita uko kwa 'nyemba zakufa,'" kapena chinachake kapena chimzake chonga icho, M'bale Jackson... Chifukwa osonkhana kwa M'bale Jackson, iwo amawaloleza iwo kumayankhula ndi malirime basi ali mu tchalitchi. Paliponse pamene iwo amverera Mzimu ndipo akufuna kuti ayankhule mu malirime, iwo amapitirira nazo nachita zimenezo. Chabwino, umenewo ndi mpingo wa M'bale Jackson. Zimenezo ndi zolondola mwangwiro. Ine ndiribe kanthu kotsutsana ndi zimenezo, palibe kanthu. Junior Jackson ndi mmodzi wa abwenzi anga opambana, ndi mwamuna waumulungu weniweni, wodzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo ndife abale. Tsopano, iye sakusowa kuti azichita kumadya chitumbuwa changa cha nthuza, ine nditha... Kapena ine sindikusowa kuti ndizidwa chitumbuwa chake cha maapulo (mukuona?), koma ife tonse tikudya chitumbuwa. Ife tonse tikuwukhulupirira Uthenga uwu ndendede. Ilo ndi dongosolo la mpingo. Ine ndinati, "Ine ndikufuna mpingo wanga kuti uziyesera kubwera palimodzi." Ine ndinati... Pamene ife tiyamba kuphwasukana kuno, Mzimu Woyera kuyankhula mu malirime ndi zina zotero, ine ndinati...



Winawake anandifunsa ine, ndipo anati, “Tsopano, M’bale Branham, kodi onse awo ndi enieni?”

<sup>57</sup> Ine ndinati, “Ine sindine woweruza.” Ine ndinati, “Ndikuuzeni inu chiani, tiyeni tizifikitse izo pa malo. Tizilole izo kuti zipitirire kwa kanthawi ndi kuzifikitsa izo pamalo mpaka Mawu akhale ataperekedwa pa icho. Ndiye muchiwone icho. Ngati Uwo uli Mzimu Woyera, Iwo uzigwirizana limodzi ndi Mawu; ngati izo sizitero, iwo sukhala uli.” Mukuona? Ndiyo njira yokha imene inu mungadziwire izo; ndiye i—izo zimadziweruza zokha. Inu mukuona? Chabwino, i—izo zimaulukira mmwamba ngati uwo uli Mzimu Woyera, izo zimachita mosokonezeka. Mukuona? Koma ngati Iwo uli Mzimu Woyera, Iwo uzingotsatira modzichepetsa mu mzere, chifukwa ndicho chimene Iwo uli; Iwo ndi Mzimu Woyera ukupita kumene mu dongosolo Lake lomwe.

<sup>58</sup> Tsopano, mu kuyankhula mu malirime uku ndi zina zotero, ine ndimakhumba aliyense wa inu akanamayankhula mu malirime. Ine ndithudi ndimatero. Ndipo nthawi zambiri, Akhristu abwino . . .

<sup>59</sup> Inu mukuwona, ngati ine ndikanakuuzani inu kuti izo zinali pa dongosolo . . . Ine ndinapeza winawake . . . Osati dongosolo, pepani ine, pa zoyankhulana mmawa uja. Munthuyo (ine ndikulingalira iwo akadali muno mu nyumbayi) kuti iwo . . . Za kuyankhula ndi malirime . . . Munthuyo ndi munthu woyenera, munthu weniweni, ndipo iwo akhala moyo wolondola. Ndipo iwo andimvapo ine ndikunena kuti umboni wa Mzimu Woyera sunali kuyankhula mu malirime, ndipo iwo siuli, koma ine ndinamulangiza munthu ameneyo kuti amufunse Mulungu kuti aziwalola iwo kuti mwina aziyankhula mu malirime kapena kunenera, chifukwa ndi chibadwa.

<sup>60</sup> Chinthu choyamba, ine ndinapita kwa munthu ameneyo ndipo ndinakapeza malo awo obadwirako, ndi chizindikiro chimene iwo anabadwira pansi pake, ndipo ndinatha kudziwa chomwe kubadwa kwawo kunali. Njira imene izo zinaikidwira mu chibadwa chawo chachirengedwe zimawaika iwo mu mzere winawake. Ndiye, pamene iwo abadwanso kachiwiri, iwo ali cha kuno mu chikhalidwe china. Ndiyeno, pamene inu mupeza mu chikhalidwe ichi, mmenemo ndi mkati, chikumbumtima, chikumbumtima cha mkati . . . Chikumbumtima chakunja chimakusunthirani inu ku njira imodzi; kumeneko ndi kubadwa kwanu kwachilengedwe. Ndiye, izo zimapanga chinachake ndipo icho chimawaika iwo chiani? Pansi pa zinai, ndi kuwaika iwo mu chikhalidwe chogawanika. Iwo samadziwa choti achite. Iwo angati, “Ambuye akufuna kuti ine ndizichita *ichi*.”

<sup>61</sup> Wamkatiyo, “O, i—ine ndikungodziwa kuti n—ndi—i—izo zikuyendera limodzi ndi Lemba.” Ndipo iwo ayamba kumachita zimenezo, ndipo chinthu choyambirira inu kuchidziwa, Satana ali kunjaku aziwaonetsa iwo mitundu yonse ya

zopindika mmenemo. Ndiyeno iwo nkumati, “Chabwino, ine ndikuganiza ine...” Mwawona, mukuona? Iwo akumvetsera kwa Satana. Mukuona? Inu muyenera kumatenga cha mkati chinachakecho, ndi chimene chiri mkati mwa inu chimene chiri cha Mwamalemba. Ndipo musati muzimulola Satana kuti aime pena paliponse. N...Ndiyo ntchito yake kuti aziima pamenepo ndi kumagogoda pa inu monga choncho. Koma musati muzimvetsera kwa iye.

<sup>62</sup> Koma, munthu ameneyo, ine ndinawauza iwo. Iwo anati, “Chabwino tsopano, ngati ine ndikanangokhala wotsimikiza za kuti ndiri nao Mzimu Woyera.” Mukuona? Munthu wabwino, munthu womvera kwenikweni ali nao Mzimu Woyera, koma izo zikanakhala zabwino kwa iye kunena kuti, “Atate, tangondipatsani ine ichi ngati chinachake choti ndiziimapo.”

<sup>63</sup> Tsopano, ngati ine ndikanaphunzitsa izo monga choncho, anthu akanamafika pomagwira izo popanda kukhala nacho chimene munthu uyo ali nacho. Mukuona? Mzimu Woyera umayankhula ndi malirime, koma iwe umayenera kukhala nao Mzimu Woyerawo poyamba Iwo usanati uyankhule ndi malirimewo. Tsopano inu mwazimva zimenezo? Kotero, ngati inu mufikira ndi kuigwira mphatso ya kuyankhula ndi malirime mulibe...

<sup>64</sup> Tsopano kumbukirani, imeneyo ikhoza kukhala ili mphatso yenyeni; umenewo ukhoza kukhala uli Mzimu Woyera ukuyankhula mwa inu ndi malirime osadziwika, ndipo inu mukhoza kutaika ndi kupita ku gehena. Baibulo linanena choncho. Inu mukukhulupirira zimenezo? Kodi inu mukufuna mutakhala ndi Lemba pa zimenezo? Inu mukufuna Lemba, kwezani dzanja lanu. “Ngakhale ine ndingamayankhule ndi malirime ngati amuna ndi Angelo...” Ndi kulondola uko? Onse, amene angathe kutanthauziridwa ndi iwo amene sangatheke kutanthauziridwa, malirime a Mzimu Woyera weniweni. “Ine sindiri kanthu,” mukuona, pokhapokha china icho chitamapita ndi izo. Inu mukhoza kukhala nacho *ichi* (mukuona?), kotero musati muzifikira kwa *icho* popanda *ichi*. Pezani *ichi* poyamba, ndiyeno, *icho* mochtika chitsatira kwa chimenecho.

<sup>65</sup> Tsopano, mvula imagwera pa olungama ndi osalungama. Dzuwa limawalira pa oyipa ndi abwino. Mvula imagwa kuti ikhwimitse mbewu; iyo imakhwimitsa maudzu nawonso, mvula yomweyo. Mzimu Woyera ukhoza kugwera mu gulu la anthu, ndi kuyankhula mu malirime, ndi kuzipanga izo kukhala ndendende zoono, kukwawira pakati pa anthu, ndi kuzipanga izo kulosera, ndi kukhala ndendende zoono. Ndizo ndendende kulondola!

<sup>66</sup> Nthawizina inu mukhoza kupita kwa—mfiti kapena wamaula, ndipo iwo akhoza kunena chinachake chimene chiri ndendende cholondola. Tayang’anani pa mfiti yaku Endori. Sauli...Izo zikanakhoza kukhala ndendende zoono; koma

izo sindizo. Awo ndi afiti. Kuyankhula mu malirime ine ndawawonapo adierezi akuyankhula mu malirime, ndi kulemba mmalirime osadziwika. Zimenezo sizimatanthauza kalikonse. Koma chinthu chenicheni ndi Mawu amenewo kachiwiri. Tibwerere ku Mawu amenewo!

<sup>67</sup> Chotero, inu mukhoza kuchita zinthu zimenezi popanda Mawu. Koma pamene inu mutenga Mawu, ndipo Iwo akamachita zimenezo, ndiye muwapenye iwo ndendende basi akukwaniritsidwa, ndendende chinthu cholondola. Mukuona? Ndiye inu muli ndendende mu mzere.

<sup>68</sup> Inde, Mzimu Woyera umawagwiritsa ntchito anthu awa monga zinaikidwa ndi nzeru Yake yomwe Yaumulungu. Koma chinthu choyamba . . .

<sup>69</sup> Tsopano chiyani? Ndiroleni ine ndingokupatsani inu kupinda pang'ono apa miniti yokha. Ine ndikanati, "Ndi angati ali ndi Mzimu Woyera?" Nonse inu kwezani mmwamba dzanja lanu. Ine ndikanati, "Chabwino, ine ndiwone ngati inu muli nawo." Baibulo limanena kuti iwo amene anali ndi Mzimu Woyera amasimidwa ndi kumalira usana ndi usiku chifukwa cha zoipa zomwe zikuchitidwa mu mzinda. Tsopano, ndi manja angati amene angakwezedwe mmwamba? Ndi angati a inu amene simungathe kupuma usiku, odzaza kwambiri ndi chisangalalo, mphamvu ya Mulungu, ndi achisoni kwambiri chifukwa cha anthu amene ataika, kuti usana ndi usiku inu mumalira ndi kumafuula chifukwa cha zoipa? Inu simungati . . . Mukuona? Angakhale ndani ameneyo mu mzindawu? Ndi angati ali, amene ali mu mpingo? Ndi chimene Baibulo limanena kuti chinali umboni wa Mzimu Woyera.

<sup>70</sup> Iye anamuza Mngelo wosindikiza (Ezekiele 9, ndiko kulondola), Iye anati, "Tenga . . . Dutsa mu mzindawo ndi kumaika chizindikiro pa iwo amene akusimidwa ndi kulira chifukwa cha zoipa zikuchitidwa mu mzindawo. Ena onse a iwo, musiye Mngelo wowononga awawononge iwo." Zilibe kanthu kaya mamembala angati amene analipo ndi zinthu zingati zimene iwo anzichita, anati, "Kaika . . ." Ndipo bambo ali ndi cholemba, atavala zoyera (zimene zimaimira Mzimu Woyera) anabwera apo ndipo anaika chizindikiro pa iwo onse amene ankasimidwa ndi kulira chifukwa cha zoipa zimene zinkachitidwa mu mzindawo. Tsopano, inu mukuti . . . Ndipo penyani zimene Iye ananena umo aponso. "Kaphe psyiti, ana aang'ono, akazi achikulire, makanda, kawaphe onse!" Ana aang'ono? Inde!

<sup>71</sup> Pamene Yoswa anakalowa mu dziko la Kenani, iye anati, "Usati ukasiye aliyense wa iwo akhale moyo. Ngati ali mwana wamng'ono wokongola, wa Chamaleki wamng'ono, kapena wa Chiamorai, kawaphe iwo! Inu muzikumbukira, iye adzakula kudzakhala wa Chamaleki; iye adaudetsa msasawo." Ndipo

pamene zinthu zazing'ono izo zikubwerera monga choncho kumatsutsana ndi Mawu a Mulungu, zichichotsanipo chinthu chimenecho. Ine sindikusamala kuti ndi wa chipembedzo chiti.

<sup>72</sup> Inu mukuti, “Chabwino, iwo ndi abwino...” Ine sindikusamala momwe iwo aliri anthu abwino! Ngati iwo ali motsutsana ndi Mawu amenewo, chichotsenipo chinthucho pakati panu. Ndi Wachiamalekai wamng'ono akukula. Akuwoneka wokongola, akawoneka wosalakwa; izo zimawoneka ngati ziri bwino, koma inu musati mukhale ndi chirichonse chochita nazo izo. Inu mukhale kutali kwa izo.

<sup>73</sup> “Chabwino, M'bale Branham, i—ine ndimapita kumusi uku, chifukwa...Chabwino, ine sindima...” Inu muzingokumbukira, wa Chiamaleki aliyense, chirichonse chimene chimawakana Mawu, muzikhala kutali kwa icho; mosakhale ndi kanthu kochita ndi icho nkomwe! Ndi angati akukhulupirira izo kuti ndi Choonadi? Ndithudi izo ziri. Mukuona? Khalani kutali ndi izo!

<sup>74</sup> Amene amasimidwa ndi kulira chifukwa cha zoipa zimene zimachitidwa mu mzinda...Kodi zimenezo inu mumaziwona kuti? Ine ndikhoza kukusonyezani inu zikwi khumi oyankhula mu malirime kwa wina amene ali wolemedwa kwenikweni nalo tchimo...amene sangathe ngakhale kupemphera ora. Koma kodi inu mumadziwa kuti Baibulo limanena kuti... muwasindikize awo okha amene akusimidwa ndi kulira chifukwa cha zoipa zomwe ziri mu mzinda? Ndi angati anayamba awerengapo izo? Zedi! Umenewo unali Mzimu Woyera ukubwera apo kudzasindikiza anthu, ndipo anati kwa Mngelo wowonongayo, “Pita uko ndi kukawononga chirichonse chimene chilibe chizindikiro chimenecho pa iwo.” Ndipo chizindikiro cha Mulungu ndi Mzimu Woyera, ndi Chisindikizo cha Mulungu.

<sup>75</sup> Tsopano, alikuti anthu amene ali kusangalatsidwa? Ine ndikhoza kukumvani anthu inu amene mumalumpha mmwamba—ndi—pansi ndi kumalira mu tchalitchi; ine ndikhoza kukusonyezani inu anthu amene amafuula ndi kumathamanga mu chipinda chonse; ine ndikhoza kukusonyezani inu anthu amene amalosera, ndipo izo zimafika pochitika; ine ndikhoza kukusonyezani inu iwo amene amayankhula mu malirime, n—ndi kumathamanga paliponse ndi mu zinyumba, ndi kumanana zinthu zimene amazitanthauzira kumene ndipo izo zimafika pochitika; koma alikuti munthu uyo amene amasimidwa ndi kumalira chifukwa cha zoipa zimene zimachitidwa mu mzinda? Ulikuti moyo wolemedwa uwo? Inu mukanati mutembenuze masamba ena atsopano pa izo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>76</sup> Tsopano, ine ndayesa mwa kupambana kwanga k—k—kuti ndikuuzeni anthu inu ndi kukutsogolerani inu monga

bambo angawatsogolere ana ake. Inu ndinu ana anga; ine ndakubalirani inu kwa Khristu kudzera mu Uthenga uwu umene ine ndikuulalikira. Mukuona? Ndipo i—i—ine ndikufuna inu kuti mukule kwathunthu kukhala ana okhwima, k—kapena ana. Ndipo ine ndikufuna kuti ndidzakuperekeni inu kwa Khristu tsiku limenelo, monga Paulo anati, “Namwali wangwiro.” Mulibe chinthu china mu Mawu amenewo koma chimene mtima wanu ungavomereze kuti “ameni” kwa icho.

<sup>77</sup> Tchimo liribe. . . Ndithudi inu muzichita zinthu molakwitsa, koma pamene chinacho, chinthu choyamba chomwe chizikutsutsani inu, “Atate, ndikhulukireni ine.”

<sup>78</sup> Ine ndikuti ndinene ichi. Ndinangoyang’ana pa munthu maminisi pang’ono apitawo. Iye anali akundifunsa ine za mnyamata wabwino tsiku lina. Ife tinali tikusaka agologolo. Mmawa umenewo ine ndinapha asanu; ine ndinasiya mmodzi wa iwo kuti akhale wa madzulo akewo. Iwe umangopeza sikisi mu dziko la Kentucky; ndiwo malire ake. Kotero munthu *wina* uyu anati, “Ine ndinapeza naini.” Mnyamata wa Chikhristu, mwana wabwino.

Ine ndinati, “Iwe wachita molakwitsa. Iwe wachita zolakwa!”

Iye anati, “Chabwino. . .”

<sup>79</sup> Ine ndinati, “Ine ndinapeza asanu mmawa umenewo, ndinasiya mmodzi kuti akhale wamadzulo akewo. Ndipo pamene ine ndinapeza gologolo mmodzi ameneyo, ndinayang’ana mu mtengo, ndipo ine ndinawerenga faifi kapena sikisi atakhala apo pomwe pamene ine ndikanatha kuyang’ana pa iwo, ndinayenda kuchokapo ndipo ndinawasiya iwo.” Ine ndinati, “ine ndinayenda chokwera kudutsa pamenepo si kale litali, ndipo apo panali pafupi fifitini kapena twente ali pamenepo. Ine ndinangotenga polekezera panga, ndipo ndinayenda nkuchokapo, ndipo ndinawasiya ena onsewo pamenepo.” Ine ndinati, “Ngati ine ndidzabwera ku dziko lino, kudzalalikira kwa anyamata inu ndi anthu inu kuno chinthu chimene chiri cholondola, ine ndikuyenera kumakhala chitsanzo chimenecho.” Chikhristu si chimene iwe umanena, ndi chimene iwe umakhala moyo, chimene iwe umachita; ndicho chitsanzo. Inu ndinu mchere wa padziko lapansi. Ine ndinati, “Ndiye, lamulo limati. . . Yesu anati, ‘Inu muzimupatsa Kaisara zinthu zimene ziri za Kaisara.’ Inu mukamaswa lamulo la liwiro ilo kunja uko, kodi inu mukuchita chiani? Inu mukuchita cholakwitsa; inu mukuchimwa. Zimupatsani Kaisara zimene ziri za Kaisara, ndicho Mulungu zimene ziri za Mulungu.”

<sup>80</sup> Kutu, “Chabwino, lamulolo ndi lolakwika.” Ine sindikusamala kulakwa kuti komwe kuli; ndi kulakwa kuswa lamulo la Yesu. Ndipo ngati inu simumamupatsa Kaisara zinthu zimene ziri za Kaisara, ndiye inu mwachita zimene Yesu

anakuuzani inu kuti musamazichite, ndi kulakwira kwa lamulo ndi tchimo. Kodi uko nkulondola?

<sup>81</sup> Ife tonse tiri olakwa; ife timachita zimenezo. Koma pamene iwe uziwona wekha utalakwa, siya izo! Anthu akukuyang'ana iwe; anthu sangamapite ku tchalitchi, koma iwo azikuwerenga iwe, kuwona zimene iwe ukuchita.

<sup>82</sup> Kotero, tengerani Khristu mu mtima mwanu; ndicho chenicheni... Khristu ndi Mzimu Woyera ali chinthu chomwecho. Mzimu Woyera, *Khristu* amatanthauza “Iye wodzozedwayo.” Ndipo Mzimu Woyera ndiwo Kudzoza kumeneko, ndipo inu ndi amene mwadzozedwa. Mukuona? Ndipo ali Khristu mwa inu akukudzozani inuyo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>83</sup> Mukatero inu muli ndi chinthu cholondola. Ndiye Iye akhoza kukugwiritsani inu ntchito kwa chirichonse chimene Iye akufuna kuti akugwiritseniko inu ntchito, chifukwa inu muli mu Thupi ndi ovomereza kwa iliyonse ya mphatso zimenezo. Koma inu mukuona, kuti ukhale nayo iliyonse ya mphatsozo kunja kwa Thupi, izo sizingamakuchitireni inu ubwino uliwonse. “Ngakhale ine ndingamayankhule ndi malirime a anthu ndi Angelo, ndiri wopanda chikondi, izo sizimandipindulira ine kanthu. Ngakhale ine nditakhala nacho chikhulupiro ndi kumamvetsa zinsinsi zonse za Mulungu, sizingandipindulire ine kanthu. Ngakhale ine nditapereka thupi langa kuti liwotchedwe ngati nsembe, kupereka katundu wanga yense kwa osauka, ngakhale ine nditakhala ndi chikhulupiro chosuntha nacho mapiri, sindiri kanthu.” Mukuona? Musati muzidalira pa zinthu zimenezo. Mzimu Woyera ndi Chokhalapo; Iwo ndi Mulungu, Mulungu mwa inu, Umunthu, Mulungu, umene wawunikira thupi lako lonse. Iwe uli wosinthidwa; iwe uli cholengedwa chatsopano. Kanthu kakang'ono kalikonse kamene kali kolakwika, Iye angati akuuze iwe uko ndi kulakwa, ndiye siya; usati uchite zimenezo. “Atate, ine sindimatanthauza kuti ndichite zimenezo, Inu ndikhululukireni ine.” Mukuona? Ndipo ndi—ndiwo Mzimu Woyera.

<sup>84</sup> Ine sindisamala mochuluka kwa momwe unayankhula ndi malirime, kuchuluka kwa momwe inu mumathamangira, kuchuluka kwa momwe inu munalumphira, kuchuluka kwa momwe inu munachitira *izi, izo*, kapena *zinazo*. Mukuona? Chirichonse chimene inu muchita, icho sichingatanthauze kanthu ngati Mzimu Woyera sunali mmenemo kuti uzikutsutsani inu pa zinthu zomwe ziri zabwino ndi zoipa.

<sup>85</sup> Tsopano, icho ndi chifukwa chake munthu uyu apa ali kulondola. Uloleni Mzimu Woyera uzichita zimenezo. Koma tsopano (inu mukuona?), tsopano, chimene chikupangitsa izi... Ndiroleni ine ndinene izi ndi chikondi, zitakonkhedwa ndi chikondi n—ndipo zitadzozedwa ndi Mawu. Mukuona?

Ngati Mzimu Woyera weniweni ukanakhala uli mwa inu, inu simukanati mukaikire zimenezo. Inu mukudziwa izo inueni, icho ndi chinthu cha payekha pakati pa inu ndi Mulungu. Mukuona? Inu mukudziwa kuti chinachake chinachitika. Inu mukudziwa kuti pali kusintha, kaya pali china—chinthu china chirichonse, inu mwiniwanu, inu ndinu kusinthako. Mukuona? Inu ndi yemwe mukuchita kusinthako, mkati mwa inu, ndipo inu mukudziwa kuti muli nawo Iwo. Kaya inu munayankhula ndi malirime, kaya inu munalumpha, munafuula, kapena china chirichonse, inu mukudziwa kuti Mulungu akukhala mkati mwa inu, kuti simukumayenda ndi malingaliro anu anu, ndi malingaliro a Khristu amene akukutsogolerani inu ndi Mawu amenewo, ndendende basi kumene Iwo upita.

<sup>86</sup> Tsopano! Koma ine ndikanati... Ngati anthu ati, “Chabwino ndiye, M’bale Branham, inu simumakhulupirira kuti ife tikuyenera kumayankhula ndi malirime?” Mukuona? Ndiye inu mukutenga ndendende cha mmbuyo pa zimene ine ndangozina kumene. Ndithudi, ine ndikukhulupirira kuti inu mumayenera kumayankhula ndi malirime. Ndipo ena a anthu inu... Mukuona? Koma inu mumapeza izi, ndi... ine ndimapeza izi, monga mmbuyo umu mailosi fifitini handiredi awa (inu mukuona?), kukhala pali pano pa kachisi. Basi, ngati inu simukuzimvetisa izo, ndiye muzindifunsa ine. Mukuona? Zindilemberani mobwereza kwa ine ngati inu simukuzimvetisa. Muzingonena zimene ine ndanena pano. Mukuona? Ndipo i... Ndipo inu... Monga Paulo anati, “Inu muzinditsatira ine monga ine ndikumutsatira Khristu.” Inu mukuona? Ndiye inu mukaona kuti ine ndikulakwitsa, ndiye muzichokako kwa ine, mwaona, ndizo zonse, chifukwa i—ine ndingakhale munthu wolakwitsa. Mukuona?

**329. Chonde fotokozani. Anthu akumati M’bale Branham ndi woposa munthu, iye akhoza kulenga, ndipo Yesu akhoza kuwoneka monga ngati M’bale Branham.**

<sup>87</sup> Tsopano, ndiroleni ine... Munthu yemwe wanena izi. Aliyense amene angakhale ali, ine sindikudziwa. Koma ine ndine m’bale wanu. Mukuona? Yesu ndi Mpulumutsi wanu. Ine sindingathe kukhala Mpulumutsi wanu, chifukwa Iye anakupulumutsani kale inu. Tsopano, inu mwayandikira kwambiri kuti mukhale mu Choonadi pamenepo, ndipo komabe motalikira kwambiri kwa Choonadi, munthu amene anamuuza munthu uyu izi. Tsopano, ali basi... Zikuwoneka kwa ine ngati ndi zolemba za mkazi, zolemba zokongola kwambiri. Ndipo ine nditha kunena kuti zimenezo zinali zolemba za mkazi sichonchonso inu? Mbale Capps, kodi inu simukanaganiza kuti izo zinali zolemba za mkazi? Kulemba kokongola. Ndipo ine sindikudziwa yemwe ali. Mukuona?

<sup>88</sup> Tsopano, “M’bale Branham, kodi Yesu angamawoneke ngati inu, kapena inu mungakhale Yesu, kapena chinachake chonga

icho?” Kulingalira kumodzi kwa mawu, izo ziri ndendende Choonadi; kulingalira kwina kwa mawu ndi motsutsakhristu. Ndiko kusiyana kwake pakati pa chabwino ndi choipa. Kuti mundipange ine kukhala Umunthu wa Ambuye Yesu Khristu, ndingakhale ndiri wotsutsakhristu (mukuona?), pakuti Munthu uja wa Ambuye Yesu akukhala pa dzanja lamanja wa Ufumu mmwamba mwamba, ndipo adzabwera kachiwiri mu mphamvu yaikulu ndi ulemmerero. Koma pa za Moyo Wake umene unali mwa Iye kukhala uli pa ine, ndi pa inu amene muli naye Iye, izo ziri ndendende Choonadi; ndipo inu mumakhala Khristu.

<sup>89</sup> Mukukumbukira uthenga wanga wa Tiamesiya? Mukuona? Inu ndinu... Mawu okuti *Mesiya* amathanthauza... “Iye wodzodzedwayo.” Tsopano, inu muli, ngati inu muli nawo Mzimu Woyera, inu mumakhala iye wodzodzedwayo. Mukuona? Ndiye pali mitundu yonse ya iwo odzodzedwawo.

<sup>90</sup> Tsopano penyani, ngati ali iwo odzodzedwawo a Baibulo. Ambiri a iwo ndi odzodzedwa... Mukuona? Chinthu chonsecho chiri mu chisokonezeko chachikulu chotero cha... mtundu uliwonse wa kusokonezeka; n—ndi za... Satana ndi machenjerero ake onse kubwera umo ndi kusanzira izo mpaka pa dontho, pafupifupi mpaka pa dontho. Pali njira imodzi yokha yomwe inu mungakhale nayo chitsimikizo mwamtheradi; mufufuze mawu ndi mawu, mawu ndi mawu! Ndi njira yokha imene inu mungathere.

<sup>91</sup> Koma kwa ine ngati—munthu, William Branham, k—kapena mwamuna wina aliyene kapena mkazi kuti angakhale ali Ambuye Yesu Khristu, Mpulumutsi wathu, uko ndi kulakwitsa. Koma kuti ukhale wodzodzedwa ndi Mzimu Wake, chimene chimabweretsa Munthu Wake yemwe wa Moyo Wake mwa iwe...

<sup>92</sup> Izo zinaimiridwa mokongola kwambiri mwa Eliya ndi Elisha, pamene Elisha anatengedwera mmwamba, Eliya, mneneri wakale, akupita Kwawo. Ndipo iye anali atatopa ndi wolema; ndipo uko kunali galeta litakolowedwa patsidya pa mtsinje kumeneko, ndipo iye... kuti amutengere iye mmwamba Kwawo ndi akavalo amoto. Ndipo kodi inu munazindikira ndiye, pamene Eliya ndi Elisha ankawoloka mtsinje? Sukulu ya aneneri inali pamtunda apo akuwayang’ana iwo. Ndipo Eliya anatenga chovala chake ndipo... kapena anaukantha mtsinje. Ndipo pamene izo zinatero, izo zinagawaniza, ndipo iye anapita patsidya. Ndipo iye anati kwa mneneri wamng’onyo, “K—kodi ukundilondoleranji ine? K—kodi—iwe ukufunapo chiani?”

<sup>93</sup> Iye anati, “Kuti magawo awiri a mzimu wanu ubwere pa ine.” Magawo awiri a mneneri wopambana uja abwere pa ine?

Iye anati, “Iwe wapempha chinthu chovuta; koma ngati iwe uti undiwone ine pamene ine ndizichokapo, ndiye Iwo



ubwera pa iwe.” Kotero inu mukhoza kulingalira momwe iye ankamuyang’anira mneneriyo.

<sup>94</sup> Tsopano, mu tsiku limenelo, mneneri uyo anali Mawu, pakuti iye anali kuwonetseredwa kwa Mawu kwa dziko. Mukuona? Ndipo iye ankadziwa kuti panayenera kukhala utumiki waukulu umadza, chifukwa apo pankasoweka chinthu chachikulupo. Ndipo pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, Iye anali Eliya. “Zinthu izi zimene ine ndikuzichita inu muzidzazichita apo; zazikulu kuposa zinthu izi inu muzidzazichita, chifukwa ine ndikupita kwa Atate Anga.” Tsopano, inu muzichita motani zimenezo? Zimuyang’anani Iye! Ndi ndani Iye? Mawu! Mukuona? Zimuyang’anani Iye!

<sup>95</sup> Tsopano, pamene zifika ku kulenga kwa zinthu, izo ndi zoonu. Yesu sanalenge konse mwachindunji chirichonse ndi kuchibweretsa icho nkukhalapo. Iye ankatenga chinthu poyamba. Iye anatenga madzi, anapanga vinyo. Iye anatenga mkate ndipo anapanga mikate yochulukirapo. Iye anatenga nsomba ndipo anapanga nsomba zochulukirapo. Koma Iye analonjeza kuti zinthu zazikulupo zoposa izi zikanati zizidzachitidwa. Mukuona? Inu mukuona? Tsopano, bwanji? Izo ziri mu tsiku loipa kwambiri kuposa momwe izo zinaliri pamene Iye anali kuno. Mukuona? Uyo akadali Iye apabe, koma akugwiritsa ntchito kachisi wanu. Mukuona?

<sup>96</sup> Ndipo munthu uyu amene ali mkati mwa inu, kumene kuli kubadwa kwanu. . . Inu ndinu John Doe; inu munabadwa mu mwezi *winawake*, ndipo inu munabadwira pansu pa nyenyezi *inayake*; inu munabadwa pansu pa chinthu *chinachake*, ndipo chimenecho chiri ndi chinthu china chochita ndi inu. Ndithudi chimatero!

<sup>97</sup> Ine ndikudziwa ine ndinka. . . Bambo anga anakonda kumanena kuti, “Ine sindingati ndikabzale mbatata izo pa nthawi ino, chifukwa mwezi sulipo yenera. Iwe sungati ubzale mbatata zimenezo, Billy.”

<sup>98</sup> Ndipo ine ndinati, “Ine sindikuzibzala izo pa mwezi, ine ndikuzibzala izo kuno mu nthaka!”

Ankati, “Chabwino, wokumva zawekha, pitirira nazo! Iwe ukapeza motupa mungapo pa mutu wako ndiye iwe udzaphunzira chinachake.” Ine ndinatero. Ine ndinatero.

<sup>99</sup> Ine ndikukuuzani inu: mudzatenge bolodi ndi kuligoneka ilo pansu uko pa maudzu mu mdima wa mwezi ndi kudzawona zimene zimachitika. Maudzu amenewo afa pompano. Ligonekeni ilo pa kuwala kwa mwezi; inu mukhoza kulisiya ligone pamenepo kwa sabata; ilo silingawononge iwo npang’ono pomwe.

<sup>100</sup> Dzaiyang’anani nyanja iyo pamene mwezi uwo ukusintha kutaliko. Pamene mafunde. . . Pamene mwezi ukuchoka nusowa, mafunde amaatsatira iwo nachoka, ndipo iwo uli mamilioni

a mailosi kuchokera pa dziko lapansi. Osati izo zokhazi, mudzapite uko ku dziko la Kentucky ndipo mudzakazike chitsulo pansi mu nthaka mpaka kufika mu madzi amchere; ndipo mudzaiyang'ane paipi imeneyo, kuya kwake pamene mwezi...pamene mafunde abweramo ndipo mudzawone mmene iwo akupita nachoka, kutali pansi pa dziko lapansi. Ndithudi!

<sup>101</sup> Inu mukadzala chinachake chimene chimayanga pamwamba pa dziko. Mu mdima wa mwezi muchiwone icho chikutsikira pansi pomwe ndi kuchipanga icho monga chikasu kapena mpiru angachitire. Inu muzale izo mobwereza njira inayo ndipo muziwone izo zikuyanga pamwamba ponse pa nthaka. Zedi, izo ziri ndi chinachake chochititsa.

<sup>102</sup> Nchifukwa chiyani Aroni ankavala cha pachifuwa cha mwala wamabadwidwe wa aliyense wa mbadwa zija? Yang'anani pa azimayi awo pamene iwo anali nkubala mayankhulidwe. Pamene azimayi awo ndi akazi a Chihebri aja mu kubala ankayankhulira pa ana aja ali nkubalidwa, izo zinkakhalitsa dzina lawo; izo zinkanena za mabadwidwe awo; izo zinkawaika iwo mu dziko la kwawo; izo zinkawaika iwo uko ku umuyaya.

<sup>103</sup> Limodzi la masiku awa pamene ine ndidzabwera muno ndi kudzakhala kanthawi pang'ono, ine ndikufuna kuti ndidzatenge phunziro limenelo. Ndendende! Ndiye muwoneni Yakobo, pamene iye anali akufa uko, pamene iye anaika manja ake pa mbadwazo ndi kuzidalitsa izo, iye anali kuwauza iwo ndendende kumene iwo akanati adzakakhale. Ndipo izo ziri ndendende molingana ndi dzina lawo, ndi ndendende molingana ndi kubadwa kwawo. Ndipo zedi, izo ziri nacho chinachake chochita ndi inu.

<sup>104</sup> Tsopano, imeneyo ndi njira yanu ya mabadwidwe; icho ndi chimene inu muli, mwamuna wachibadwa kapena mkazi wachibadwa. Koma pamene inu mubadwanso kachiwiri, chimenecho si chikumbumtima chakunja. Chakunja ndi chimene inu mumawona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva, koma chamkati mwa chimenecho ndi chomwe inu muli kwenikweni. Tsopano, izi kunja kuno, Satana amakuyesani inu basi ndi kumakukhomani inu pamenepo mbali iliyonse apa; koma pansi apa iye sangathe kuchita zimenezo kupatula inu mutamulola iye kuti azichita zimenezo. Pakuti mkati umu inu muli nacho chikhulupiro, ndipo chikhulupiro sichimachokera ku chikumbumtima chakunja, icho chimalingalira. Koma mu chikhulupiro mulibe kulingalira. Inu mumakhala nacho icho kuchokera kwa Mulungu, ndipo inu mumadziwa kuti chiri mmenemo. Ine sindikusamala momwe izo zikuwonekera zolakwika, inu mumadziwabe kuti izo ndi zolondola; ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Ndipo palibe chinthu chingati chisokoneze zimenezo. Palibe kanthu kangavutitse zimenezo; izo

zikudutsa kumene molunjika patsogolo. Chovuta sichitanthauza kanthu kwa icho; chimasambira chamtsogolo kumene kupyola mu zimenezo, chifukwa Icho ndi Mawu. Ndipo Mawu ndi Lupanga, ndipo Mawu amacheka... Lupanga limadzidula Lokha momasuka kwa chinthu china chirichonse. Inu mukuona? Zimatengera dzanja la chikhulupiroro kuti liwagwire Mawu amenewo. Chikhulupiroro chimenecho chiyenera kukhala chiri...

<sup>105</sup> Tsopano onani, pamene chikumbumtima chamkati icho... Umu ndi mkati mwake; uku ndi kunjwa kwake. Izo zimaaululidwa mkati umu, Choonadi chimenecho; kunjwa kuno, ndi kulingalira. Tsopano, kodi izo sizikuwoneka zomveka ngati ife tikanati, “Ife tonse tingopita ndi kukalumikizana ndi Assemblies?” Tsopano, ine ndimawakonda a Assemblies of God, ine ndimawakonda aumodzi, ine ndimakonda yonse ya mipingo imeneyo. “Bwanji ife tonse sitikungopita ndi kumakachita limodzi ndi iwo, mwinamwake kukachita zabwino zina.” Uko ndi kulingalira, kunjako. Koma pansi mkatimo, penyani izo. Pamene inu muwona kunjwa kuno, izi zima—izi zimatsutsana, ndiye... Yang’anani pa Assemblies. Zinthu zambiri zimene iwo amachita zimene ine sindimakhulupirira kuti ziri—ziri Mwamalemba, ndipo ndikhoza kutsimikizira izo kwa iwo kuti siziri Mwamalemba. Koma pali malingaliro ochuluka kwambiri adzazana mmenemo. Pali zikwi za abale a Assembly amenewo ndi alongo amene amakhulupirira awa, Mawu, ndipo samakhulupirira zimene a Assemblies amaphunzitsa kuti ndi zolondola. Koma iwo ali mu ukonde.

<sup>106</sup> Abaptisti, Apresibateria, aumodzi, ndi ena onse a iwo, iwo ali mu ukonde umenewo kumene gulu la anthu limasonkhana palimodzi ndipo iwo amazilingalira izo. Ndipo kumakhala kutchuka kochuluka kwambiri kwa munthu. Apa pali bishopu wakhala apayu, woyang’anira zonse wamkulu; iye amanena chirichonse, kodi kamunthu kakang’onoko kanganene chiani? Iye amawopa kuti anene chirichonse. “Ine ndikugwirizana ndi inu. Eya, uko nkulondola! A-nha! Inde, Bishopu, k—kapena Mkulu, ndinu... izo ndi ndendende kulondola.” Iye amagwirizana naye iye.

<sup>107</sup> Apa, tiyeni titenge chidakhwa kunjwa kuno pa msewu, mbadwa wamba ija ikudutsa kutsika ndi msewu nati, “Wopempha wachikulire, palibe kalikonse kwa iye.” Mutengereni iye kumusi kuno, kamuikeni iye pa gulu la apolisi, ndi kuika batchi pa iye, ndi mfuti pa iye. “Mmawa wabwino, John, ziri zabwino kwambiri kukuwonani inu kachiwiri!” Mukuona? Ulemu kwa wina ndi mzake.

<sup>108</sup> Yesu anati, “Inu mungakhale nacho bwanji chikhulupiroro pamene inu muli nako kulemekeza?” Kwa mtundu woterowo, inu mukudziwa, kutifunsa ife, kulemekeza wina... ine sindikukumbukira basi momwe mawu akupitira pamene.

Koma, pamene chokhumba chanu nkulemekezana wina ndi mzake. Mukuona? Simungati muzichita zimenezo.

109 Ndipo pamene anthu abwera palimodzi mu bungwe, iwo amakhala pansu; ndipo mwamuna wachichepereyo amachita mantha kuti anene chirichonse, chifukwa abishopu anena choncho, mkulu wanena chomwecho. Koma musamunyozetse mwamunayo, mukhulupirireni iye kuti ndi mwamuna wabwino; koma nthawizonse muzikumbukira, Mawu a Mulungu ali olondola ndipo zina zonse zosiyana ziri zolakwika. “Mulole Mawu Anga akhale owona, ndi mawu a munthu aliyense akhale bodza.” Mukuona zimenezo? Ndi zimene ife tikufuna kuti tizichita, ndiko kukhulupirira zimenezo.

110 Tsopano kumbukirani, ife sitiri Mawu, koma ife ndife Mawu. U nhu! Tsopano inu mwazimva zimenezo? Yesu sanali Mulungu, koma Iye anali Mulungu. Iye anali Munthu, komabe Iye anali Mulungu. Iye ankakhoza kulira, ndipo komabe Iye ankakhoza kudzutsa wakufa. Iye ankakhoza kulira chifukwa choti munthu wafa ndi kumudzutsanso iye kachiwiri. Iye anali Yehova-yire, Yehova rafa, Yehova-Manase; Iye anali Yehova, zonse kwathunthu. Iye anali Yehova, ndipo komabe Iye anali Munthu. Iye anali mwini wa dziko lapansi, ndipo analipanga dziko lapansi, ndipo analibe malo oti agonekepo mutu Wake. Iye anati, “Mbalame zimene Ine ndinazipanga ziri nawo zisa, ndipo Ine ndiribe malo oti ndingagonekepo mutu wanga. Ankhandwe, amene ine ndinawarenga, ali nawo mauna mu nthaka, ndipo Ine ndiribe ngakhale amodzi Mwiniwanga, ngakhale okuti ndidzaikidwemo.” Ndiko kulondola. Iye anachita kubwerekera manda a winawake kuti aikidwemo.

111 Iye analenga chiberekero chirichonse chimene chinali mwa mkazi. Iye analibe chiberekero choti abadwiremo; iye anachita kubwereka chiberekero. Iye analenga dziko lapansi ndipo analibe malo oti aikidwemo; Iye anachita kubwereka- . . . una mu nthaka, kuti aikidwemo, Yosefe waku Arimatea. Mukuona? I—iwo anachita k—anachita kubwereka malo, komabe Iye anali Mulungu, zinatsimikizira kuti Iye anali Mulungu.

112 Tsopano, inu mukumvetsa? Ife si tiri. . . Iye ndife Tiamesiya, koma osati Yesu uyo. Iye ndi Atate wathu; ife timangodzozedwa ndi Mzimu Wake, ndipo ndicho chifukwa Moyo Wake. . . Ndipo zimenezo zimawatenga anthu. Mukuona, ngati inu simungati mukhale ndi kuganizira izo kwathunthu, izo zimawafikitsa anthu pokhulupirira, “Chabwino, mwamuna uyu angakhale ali Mesiya. Zedi iye ali.

“Uyu cha kuno akhoza kukhala ali.” Iwo onse ali. Mukuona? “Chabwino, angakhalepo bwanji apo awiri a iwo?” Pali zikwi za iwo. Mukuona?

113 Koma inu onani, Moyo Wake unagawanidwa pa Tsiku la Pentekoste. Pamene Lawi la Moto lija linabwera pansu, Ilo

linagawanika ngati malirime ndipo linakhala pa aliyense wa iwo, Mulungu akuzigawaniza Iyemwini pakati pa anthu Ake, chifukwa Mpingo ndi Khristu ali Amodzi, monga momwe mwamuna ndi mkazake ali mmodzi.

**330. M'bale Branham, kodi ine ndikuyenera kumamusonyeza chotani mkazi wanga kuti ine ndimasamala kwenikweni za iye ndipo komabe nkumasewera . . . kapena nkumakhala limodzi nao Mawu (Ndiko)—kukha—kumakhalabe limodzi nao Mawu, komabe nkumakhala ndi funso monga ili lakuti: “Chifukwa chiani iwe sumachita zimene iwe umalalikirira kapena kukhulupirira?”**

<sup>114</sup> Chabwino ndiye, ngati mkazanu, ngati mkazanu akunena izi kwa inu pamene iye. . . ali nawo ufulu woti azinena izo, inu kulibwino muyambe kuchita bwino. Mwawona, mukuona? Ndiye ngati i—ngati iye akunena zimenezo pongofuna kuti akhale woipa, kumbukirani, Baibulo linati, “Kukanakhala bwinoko kuti mwala wamphero ukanati upachikidwe pa khosi lako ndi kumizidwa mu kuya kwa nyanja kuposa kuti mukhumudwitse ngakhale wochepesetsa wa awa, aang’ono anga.” Tsopano, limenelo ndi lanu basi. . . ? . . .

<sup>115</sup> Ndipo mwinamwake mkazi uyu sali mtundu umenewo wa munthu. Mwinamwake iye ndi wosiyana. Mwina iye ndi munthu wabwino. Mwina iye akungokuyesani inu kuti awone zimene inu mungati muchite.

<sup>116</sup> Tsopano, khalani mu chikondi ndi iye ndipo muloleni iye kuti aziwona Yesu mwa inu. Inu zichitani zimenezo. Mukuona? Inu musingopitirira nazo. Ena. . . Ine ndinapereka kulungosola kwakung’ono mmawa uno za munthu amene. . . Nthawi ina mkazi wamng’ono uyu a—anali atalandira Mzimu Woyera. Iye anali munthu wamng’ono wokoma kwambiri. Iwo. . . Iye anati. . . Chabwino, iye anakhala ndi moyo wovuta, ndipo mwamuna wake anali chidakhwa. Ndipo kotero, iye anali kumangopitirira naye; iye amapirira naye iye. Iye amati, “Iwe ukufuna kuti uzipita ku tchalitchi, Wokonedwa, zipita!” Koma tsopano, iye ankapita uko komwera mowa, kumusi uko ku Brown Derby achikulire, kumusi uku. Amapitirira nazo. Chotero iwo amakhala ali kumeneko nthawi zonse, kale anakutchira kwa Bonifers. Ambiri a inu a nthawi zakale kuno mukukumbukira pamene a Bonifer anali nayo uko pangodya ya. . . Iko kumatchedwa Brown Derby tsopano, ine ndikukhulupirira iwo ali.

<sup>117</sup> Kotero, kumakhala ali kumusi kumeneko, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, usiku wina panabwera funso lokhudza tchalitchi ndi lokhudza Akhristu. Mmodzi wa oledzera wachikulire atakhala pamenepo anati, “Kulibe chinthu chotero ngati Akhristu panonso. Ndipo palibe konse chinthu choterocho. Gulu lonse ili la achinyengo,” anati, “inu mumawawona iwo

kuno akusuta, akumwa, akuchita chinthu chomwecho chimene ife timachita, ndipo,” anati, “amadzitcha okha Akhristu. Palibe zoterozo.”

<sup>118</sup> Wina uyu woledzera anaimirira ndipo anati, “Miniti yokha! Pali mmodzi amene ine ndikumudziwa.”

Anati, “Nndani ameneyo.”

Anati, “Ameneyo ndi mkazi wanga.” Mwawona? Iye anali atakhala wamchere. Iye anali akuchigwira icho nthawi yonseyo.

Iye anati, “Ine ndikukaikira ngati iye anayikidwa pofinyidwa. . .”

Iye anati, “Ayi, iye ndi Mkhristu basibe; ine nditsimikizira izo kwa inu.” Anati, “Ine ndikuuuzani choti ife tichite; tiyeni tipite kunyumba, ndipo ine ndikakusonyezani inu ngati iye ali Mkhristu kapena ayi.” Anati, “Tiyeni tipite kunyumba, ndipo tsopano, tiyeni tiledzere kwenikweni. Ife tizikachita ngati taledzera kwenikweni.” Anagogoda pa khomo, analowa akudzandimira pa chirichonse n—ndi. . . “Bwanji iwe sunawakhazike apa mwanjira iyi,” ndi chirichonse. Ndipo iye anali atawakhazika iwo onse mu mipando imeneyo ndipo (alendo ake, inu mukudziwa)—ndipo ankayesera kuwapangitsa iwo kukhala olandiridwa basi monga akanathera. Anati, “Ine ndikufuna kuti iwe utikonzere ife chakudya china.” Ndipo kotero iwo. . . Iye anatuluka ndipo anakakonzika china. Anati, “Ife tikufuna nyama ndi mazira.” Iye amadziwa kuti iwo anali nazo izo, kotero iwo anakonzika nyama ndi mazira. Pamene iye anafika pa tebulo apo, iye anaziyang’ana izo monga choncho, anainyamula mbale yake, ndipo anataira zinthuzo pansi, anati, “Iwe ukudziwa, ine sindimakonda mazira anga monga choncho. Tiyeni anyamata tiyeni tichokeko kuno mulimonse,” monga ch—monga choncho.

<sup>119</sup> Iwo anapita panja ndipo anakakhala pansi monga choncho, inu mukudziwa. Ndipo mkaziyo anabwera panjapo; iye anati, “Wokonedwa, i—ine ndikupepesa kuti ine sindinawakonzika bwino iwo; ine ndikukonzikanira inu ena.”

<sup>120</sup> “O, zachabechabe, iwe umadziwa kuti ine sindimawafuna iwo mwanjira imeneyo pakuyamba pomwe,” basi kumangopitirira nazo monga choncho. Iwo anapita panja apo, ndipo anakakhala pansi, ndi kumachita ngati iwo anali ataledzera. Iwo anamumva mkaziyo mkati umo akudandaula kwa iyemwini, akuimba ndi mawu otsika kwenikweni:

Kodi Yesu anyamule mtanda yekha,  
Ndi dziko lonse lizipita mwaufulu?  
Pali mtanda wa aliyense,  
Ndipo pali mtanda wa ine.

Mtanda opatulika uwu ine ndiunyamula,  
Mpaka imfa idzandimasule ine.

Woledzera mmodzi anayang'ana pa mzake wina, anati, “Uyo ndi Mkhristu; iye ali nacho icho!” Ndipo mkazi wamng'ono uyo anamutsogolera mwamuna wake, palimodzi ndi ena awa kwa Khristu usiku umenewo. Mukuona? Bwanji? Mukuona? Kungokhala muli okoma kwenikweni. Muzikumbukira basi, Iye amadziwa zonse za izo.

<sup>121</sup> Kotero, mlongo, kapena m'bale, aliyense amene angakhale ali, kapena m'bale, izo ziri pano, chifukwa iye anafunsa za mkazi wake, inu mungokhala amchere basi; iye anayamba kukhala waludzu ngati muli chirichonse mkati mwa iye choti achitire ludzu. Ngati umo mulibe, kumbukirani, ngati inu mwatenga munthu wolakwika, inu mudzapeza woyenerayo mu Zakachikwi. Inu mungopitirira naye; zolakwika zonse zidzakonzedwa bwino kumeneko.

**331. M'bale Branham, kodi inu mumaphunzitsa kuti Mkwatibwi asamapite ku mpingo wina uliwonse kupatula ngati inu muli kumeneko mukulalikira, kapena ku kachisi, mwakuyankhula kwina, kachisi?** (Pali “mwina,” izo zikutanthauza “mwakuyankhula kwina.”)

**332. Ndiponso, kodi inu mumaphunzitsa kuti ife sitikusowa kumasunga 1—Lamlungu kapena masiku a tchuthi, monga kugwira ntchito, kuwedza, ndi zina zotero? Kapena . . .** (ine ndinganene kuti limenelo linali Lamlungu. Ilo limawoneka ngati Lamlungu kwa ine. Kapena mpaka pansi izo zikuwoneka ngati . . . kapena Lamlungu, ine ndikulingalira ilo liri, masiku atchuthi kapena Malamlungu. Eya, Malamlungu, ndi momwe apa zikuwonekera? [M'bale Branham ayankhula ndi winawake—Mkonzi.] Masiku opatulika—masiku opatulika, Lamlungu ndi masiku opatulika.)

<sup>122</sup> Ayi! Inu mwalakwitsapo. Mukuona? Ndiroleni ine ndidutsemo mobwereza ndi kungoyankha izo momwe ine ndikubwerera pa izo.

“Kodi inu mumaphunzitsa kuti Mkwatibwi asamapite ku mpingo wina uliwonse kupatula ngati inu mukulalikira—kulalikira kapena ngati ayi, mwinamwake, pa kachisi?” Ayi! Ine sindimaphunzitsa zimenezo. Ine sindikhulupirira zimenezo; ine sindimakhulupirira zimenezo. Ife tiri ndi atumiki amene akhala pano amene amwazikana konsekonse kuzungulira mu dzikoli, ndipo ine ndikukhulupirira kuti iwo ali gawo la Mkwatibwi ameneyo. Ine ndikukhulupirira kuti mwamuna kapena mkazi akhoza kupita ku mpingo uliwonse kumene iwo akufuna kuti azipitako kumene amaphunzitsako Mawu. Ndipo ine ndikukhulupirira, ngati iwo samaphunzitsa Mawu onse, ndipo inu simukutha kupita ku mpingo ku malo ena aliwonse kumene iwo amaphunzitsa Mawu onse, zipitani kumene iwo amaphunzitsa Mawu atheka mpaka inu mutapeza kumene

iwo amaphunzitsa Mawu amphumphu. Zipitani ku mpingo chirichonse chimene inu mungachite. Zichitani zimenezo.

<sup>123</sup> “Ndiponso kodi inu mumaphunzitsa kuti ife tiy—ife tiyenera. . . sitikusowa kumasunga Lamlungu, kapena tsiku lopatulika lirilonse, k—kapena kugwira ntchito, kapena monga kugwira ntchito, kapena kuwedza Lamlungu?”

<sup>124</sup> Ine ndimakhulupirira kuti ndi tchimo kukawedza, ndi kusaka, ndi kugwira ntchito Lamlungu pamene inu mukanakhoza kupita ku mpingo. Tsopano, ine ndikukhulupirira inu mukulakwira malamulo a Mulungu. “Kodi liripo lamulo ku zoterozo?” Inde, bwana! Tsopano, mu Chipangano Chakale ife tinali ndi choimira cha tsiku la Sabata. Ilo linali zonse. . . Ndipo Yesu sanabwere kuti inu muzisunga masiku a Sabata. Tsiku lakale la Sabata linali Loweruka, limene linali kutha kwa sabata. Lamlungu ndi tsiku lachisanu ndi chitatu, kapena tsiku loyamba la sabata, limene Yesu anawuka pa ilo.

<sup>125</sup> Ine sindimakhulupirira kuti ndi zolondola kuti. . . Tsopano, ngati inu muli kutali komwe mu nkhalango kwinakwake, ndipo inu muli kumeneko pa ulendo wosaka, kulibe mpingo pozungulira, chirichonse monga choncho, ndipo palibe chirichonse chimene inu mungathe kuchita; ndipo ngati inu mumawedza, ine ndikukhulupirira kuti zimenezo zikanakhala bwino bwino. Koma ngati inu muli pafupi ndi mzinda, kapena pafupi kumene mpingo uli kupitirira nazo, inu muyenera kukakhala nao mpingo mwanjira iliyonse, kwinakwake.

<sup>126</sup> Ndipo ine ndikukhulupirira, ponena za kugwira ntchito, ine ndimakhulupirira ngati ng’ombe ili mu dzenje, kapena chinachake chimene chikuyenera kuti chichitidwe Lamlungu, inu pitirirani nazo ndi kukachita izo, ngati icho chiri chinachake chimene inu simukanatha kuchitira mwina, icho chimayenera kuti chichitidwe mwanjira imeneyo. Koma ngati inu mukungochita zimenezo, ndipo mwachita kudikirira mpakana Lamlungu kuti muchite icho, kapena kungozichita izo monga choncho, inu mukulakwa. Mukuona? Ife tisamachite zimenezo, ife tiyenera kuti tizililemekeza tsiku lopatulika limenelo.

<sup>127</sup> Ndipo tsopano, kumbukirani, muzipita ku mpingo kwinakwake, malo ena. Ngati. . . i—ine ndikhoza kutchula mpingo wachipembedzo winawake, koma ine sindingati ndichite zimenezo, chifukwa mpingo uno, chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa nkuti iwo amaphunzitsa chimene ine ndimakhulupirira ndicho, iwo amanena kuti iwo amakhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu. Chabwino, ine ndimatero zimenezo. Kuphunzitsa kwawo kwina konse n. . . Iwo amakhulupirira mu. . . ndi kuchotsedwa kwa machimo kuli mwa madzi. Tsopano, awo si aumodzi; iwo amachita chinthu chomwecho, koma ine sindikuyankhula za



iwo. Iwo amakhulupirira k—kuti kusinthidwa kumachitidwa ndi madzi, ndi zina zotero. Ndipo ine sindimakhulupirira zimenezo. Ndipo iwo, o, iwo amakhulupirira kuti ngati chirichonse chiri ndi machiritso Auzimu mwa icho ndi cha mdierekezi. Ndipo iwo amakhulupirira mu zonse... Iwo ndi okhawa—iwo ndi chinthu chokha chimene chiripo, ndipo chinthu chokha chimene inu mumayenera kuchita ndi kungoika dzina lanu pa bukhu limenelo. Ndipo ngati inu mulibe ilo umo, inu mwataika. Tsopano, ine sindimakhulupirira zimenezo. Koma ngati kulibe mpingo uliwonse woti muzipitako (ine sindikanapita kumeneko motsutsa), ine ndikanapita kumeneko ndi cholinga cha kukhalapo kwanga, ndipo ine nkukakhala pafupi ndi winawake, kuti Khristu amene anali mu mtima wanga akakhoze kumukopa winawake kumeneko. Zipitani pakati pa iwo, koma musati mukhale ochita nawo za kusakhulupirira kwawo.

**333. M'bale Branham, ine ndikufuna kuti ndilandire Mzimu Woyera. Ine ndikufuna kuti ndidziwe choti nkuchita. Ine ndikulemedwa kuti banja langa lipulumutsidwe.** Ndipo mlongoyo walembedo dzina lake.

<sup>128</sup> Ngati inu mukufuna kuti mulandire Mzimu Woyera, ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, Mlongo wanga wokonedwa, ngati inu muli pano. Nd—ndipo—ine... M'bale Neville, kodi ameneyo ndi membala wa mpingo pano? [Mbale Branham ayankhulana ndi M'bale Neville—Mkonzi.] ine si—ine sindiri kuwakumbukira iwo ngakhalenso. Koma n—ngati inu muli pano, Mlongo B-o-u-g-h, ngati inu muli pano, ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Baibulo limati, “Odala ali iwo amene amamva njala ndi ludzu lofuna chilungamo...” Inu ndinu odala kwambiri ngakhale pakuwufuna Iwo. Mukuona? Tsopano, kumbukirani, osati kuti i—inu—muli nawo Iwo, koma odala ali iwo amene achita njala ndi ludzu pofuna Iwo, “pakuti iwo adzadzazitsidwa.” Ingokhalani basi ndi iwo.

<sup>129</sup> “Kodi ine ndilichitire chiyani banja langa?” Gwiritsani ntchito chikhulupiriro chomwecho chimene inu mukuchigwiritsira ntchito kwa inumwini, kwa banja lanu. Aperekeni iwo kwa Ambuye ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse kuti inu mufike populumutsidwa. Lolani izo... Musalole kuti izo zizingobwera mwa kulingalira kwanu kwachibadwa apa, lolani izo zigwere mmusi momwe mkatimo, chikumbumtima icho, ndiye iwo ndi anu. Mulungu awapereka iwo kwa inu pamene inu mukhala nacho icho pansu pamenepo.

<sup>130</sup> Chirichonse chimene inu muli nacho mu mtima mwanu apa ndipo mukapempha pofuna icho, pamene inu muzipemphera, zikhulupirirani kuti inu mulandira chimene inu mumachipempha. Tsopano, inu simungati mukayikire izo panonso. Inu simungakhulupirire izo ndi kukayikira izo pa nthawi yomweyo. Ndi angati akudziwa zimenezo? Inu simungati muzikhulupirira ndi kukaikira pa nthawi yomweyo. Inu

muyenera kumakhulupirira kuti chimene inu mwachipempha, inu muchilandira icho, ndiye iye anati izo ziperekedwa kwa inu. Chotero inu mungokhulupirira kwa banja lanu, ndipo iwo awulandira iwo.

**334. M'bale Branham, nanga bwanji mwana wathu wamwamuna p—pakuti inu simuli pa—simuli kulalikira pa Malipenga? Kumbukirani lonjezo limene inu munandipatsa ine pa lamya lomukhudza iye ndi Malipenga Asanu ndi awiri?**

<sup>131</sup> Ine sindiri kukumbukira izo. Ine sindiri kukumbukira zomwe izo zinali. Koma chirichonse chimene icho chiri, inu mumulole Billy Paul adziwe chimene icho chiri. Chirichonse chimene ine ndinalonjeza, chimenecho ine ndichichita. Ine sindikumubukira. Inu mukudziwa, ine...Nthawizina ine ndimapeza, mwinamwake mu nthawi yausiku, ndimayankha mafoni makumi atatu, makumi anai pa nthawi imodzi, inu mukuona, chotero ine sindimakumbukira usiku pambuyo pa usiku, nthawizina pamene ine ndiripo, chotero ine sindikumva chirichonse chimene icho chiri.

**Nanga bwanji mlongo wanga wa Chikatolika ndi m'bale? Zikomo inu.**

<sup>132</sup> O, munthu uyu ndi wochokera kunjira konse kwa mzinda, kutali komwe muli mu Texas. Ine...Chabwino, mlongo, ngati i—ngati inu muli ochokera ku Texas ndipo mukaipeza tepi iyi, kapena ngati pali tepi (ine ndikuganiza sipadzakhala pali tepi pa izi), koma ngati ilipo...[M'bale Branham afunsa za kujambula utumikiwu—Mkonzi.] Kodi iwo akupanga tepi? Inu mukupanga iyo? Chabwino, ngati iwo ali...Tepiyo...Ndiye ine ndikuuzeni inu chochita. Ngati inu...Pa tepi iyi, pamene inu mupeza iyo, kumbukirani, “Nanga bwanji mwana wathu wamwamuna pamene...zokhudza Malipenga Asanu ndi awiri?” Ine sindiri kukumbukira za izo, kupatula ngati ine ndinalonjeza kuti ndikomana naye iye kapena chinachake pa nthawi ya Malipenga Asanu ndi awiri. Ngati ine ndinatero, ine ndidzamuwona iye; chifukwa ine sindinalalikire Malipenga Asanu ndi awiri, ine ndinalalikira *Phwando la Malipenga*. Inu munamvetsa za zimenezo.

<sup>133</sup> “Ndipo nanga bwanji mlongo wanga wa Chikatolika ndi m'bale? Zikomo inu!” Ine ndikuuzeni inu, Akazi a C-o-r-n-i-l-s-e-n... Ngati donayo ali pano, amuwone Billy Paul mmawa uno. N—ndipo ngati sichoncho, chabwino, ine ndi—ine ndidza—i—ine sindikumvetsa kuti izo ndi chiani (inu mukuona?); ndi funso chabe. I—ine sindikutha kuzimvetsa izo (mukuona?), chimene icho chiri, chifukwa ine ndinalonjeza chinachake chokhudza mwana wawo wamwamuna ndi Malipenga ndi za mlongo wa Chikatolika; ndipo i—ine si—izo siziri mmalingaliro anga tsopano kuti ndizikumubukire. Mungomuwona Billy.

Ili liyenera . . . Ilo langokhala pempho la pemphero. Apereka dzina la munthuyo ndipo akuti, “kupweteka kwa mutu ndi nkusani.” Kotero izo zinangokhala . . . Kungoti tiwapempherere iwo, ine ndikulingalira. Chabwino.

**335. Chonde talongosolani chikwati ndi chilekano.** (Ine ndinali nalo kale ilo. Awa ndi mafunso asanu ndi awiri, mafunso asanu ndi atatu pa pepala limodzi.) **Chonde talongosolani chikwati ndi chilekano.**

Ine ndatero.

**336. Mose n—ndi Eliya ali pa dziko lapansi tsopano? Kodi Mose ndi Eliya ali pa dziko lapansi tsopano? Kodi iwo ali mu Amereka?**

<sup>134</sup> Ayi! Mukuona? Ayi, iwo siali kuno; iwo sadzakhala alipo mpakana Mpingo utatengedwa nuchotsedwapo, ndiye Mose ndi Eliya . . . Ndi angati akumvetsa zimenezo? Chabwino. Ndipo tiyeni tiwone. Iwo alibe dzina lililonse lalembedwa kwa ili, kotero . . . Chabwino. Ngati aliyense amene anafunsa mafunso awa . . . Ine ndikukhulupirira pali asanu ndi awiri a iwo; ine ndinapereka . . . ndinalemba seveni. Chabwino!

**337. Talongosolani kusiyana pakati pa “Dzina la Yesu,” ndi “Dzina la Yesu.”** (Dikirani miniti.) **Longosolani kusiyana pakati pa dzina “Yesu” ndi “Dzina la Yesu.”**

<sup>135</sup> Chabwino, iwo onsewo akhala ali ofanana ngati iwo agwiritsidwa ntchito mwanjira yofanana (mukuona?), kugwiritsidwa pa Munthu yemweyo, dzina *Yesu*, ndi *Dzina la Yesu*. *Dzina la Yesu* ndi dzina—dzina *Yesu* ndi Yemwe Iye ali. *Dzina la Yesu* likukamba za Munthuyo, kotero izo zingakhale ziri zofanana . . . ine ndikuganiza izo zikanati . . . Kodi izo sizikumveka mwanzeru? Mukuona? *Dzina Yesu* ndi Munthu Mwiniwakeyo, ndipo *Dzina la Yesu* ndi inuyo kulozera kwa Munthu ameneyo. Mukuona?

<sup>136</sup> Kuti, dzina langa ndine *William*. Ameneyo ndi ineyo. Chabwino. Tsopano, inu mukuti . . . ine ndikuyankhula . . . *Dzina la William*, ndiye inu mukulozera kwa ineyo. Limenelo ndi dzina langa. Mukuona? Tsopano.

**338. Kodi Dzina la Ambuye lasintha mu nyengo zosiyanazi?**

<sup>137</sup> Inde, inde! Ilo nthawiina linkatchedwa—Iye ankatchedwa INE NDINE. Iye ankatchedwa Yehova, ndipo Iye wasintha nthawi zambiri. Nthawi yotsiriza imene ilo linasinthidwa panali pamene Mulungu anadzakhala thupi ndipo anatenga dzina la umunthu.

<sup>138</sup> Yehova, INE NDINE, ndi onse awo, ndi maudingo kwa Dzinalo. Mukuona? Inu mukanabatizidwa mu dzina la Yehova, ilo likanakhala liri Dzina la Yesu Khristu. Inu mukanabatizidwa mu dzina la Yehova-rapha, Yehova Manase, ndi Yehova-yire,

onse amenewo, akanakhala ali Yesu Khristu. INE NDINE ndiye Yesu Khristu.

<sup>139</sup> Kumbukirani, ataima pajapa tsiku lijali, ndipo Iye anati, “Inu mukuti munkadya manna mu chipululu . . .”

“Makolo athu ankadya manna”

Ndipo anafa!” Iye anatero.

<sup>140</sup> Iwo anati, “Chabwino, ife tikudziwa tsopano Inu ndinu wopenga, chifukwa Ndinu munthu chabe ndipo simunapitirire usinkhu wa zaka fifite, ndipo Inu mukuti munamuwona Abrahamu.”

Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.” Mukuona? Iye anali INE NDINE. Ndipo maudingo onse ndi maina amene anayamba akhala ali a Mulungu anapangidwa Dzina limodzi la umunthu, Ambuye Yesu Khristu. Chabwino.

**339. Tsopano: Ngati nthawi ikutha pamene Zisindikizo zinatsegulidwa, ndi . . . Ngati nthawi inatha (pepani ine) pamene Zisindikizo zinatsegulidwa, ndiye Zakachikwi nazonso—ndiye Zakachikwi nazonso zinatha, si choncho izo?**

<sup>141</sup> Ayi, ayi! Nthawi sinathe pamene Zisindikizo zinatsegulidwa. Simunazimvetse izo. Chimene chinachitika, zinsinsi zinaululidwa, osati nthawi inatha. Mukuona? Tangoyang’anani. Penyani mwacheru kwenikweni tsopano, ndipo mukasewere tepi yanu ngati inu munapeza izo kuchokera pa tepi. Mukuona?

<sup>142</sup> Nthawi sinathe mpakana . . . Uyu ayenera kukhala kuti ndi wa zakazikwi zamtsogolo kapena chinachake, amene anafunsa funsoli. Chifukwa mukuona? Ife tiri nazo zaka chikwi Mpingo utapita kale Kwawo ndi kubwereranso pa dziko lapansi. Ndiye nthawi ikutha mu Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano.

<sup>143</sup> Tsopano, Zakachikwi si Miyamba Yatsopano ndi Dziko Latsopano. Uko kudzakhala kudakali tchimo zikadzatha Zakachikwi. Zakachikwi ndi choimira cha Nowa kukalowa mu chombo, ndi kutengedwera kwinako, ndipo anamubweretsa Hamu ndi iwo ku mbali inayo. Ndipo tchimo linatuluka ngakhale kuchokera mu chombo. Mukuona?

<sup>144</sup> Koma Enoki, wosinthidwayo, anali woimira wa Mkwatibwi amene anapita mmwambayo, osati amene anatengedwera kumbali inayo. Chotero tchimo lidzakhala liripobe ku mbali inayo ya Zakachikwi, koma osati mu nthawi ya Zakachikwi. Mukuona? Mu nthawi ya Zakachikwi kuli mtendere. Mukuona? Koma tchimo lidzathetsedwa ku mbali inayo ya Zakachikwi, ndiyeno nthawi ikuziralapo.

<sup>145</sup> Ndipo tsopano, kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri kumene kunaperekedwa ndi Mzimu Woyera, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinali kokha kuti zipangitse kudziwika zimene zinali zitasiyidwapo mu nyengo zambuyo mwathu.

<sup>146</sup> Tsopano, monga wafioloje wina wamkulu anayesera kuti andipanikize ine pa zimenezo, iye anati, “M’bale Branham, inu... Mulungu tsiku lina adzakupatsani inu chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo. Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zimenezo zidzakhala ziri chinachake chimene ife sitinayambe tachiphunzira panobe, kuti izo zidzakhala ziri chinachake chimene sichiri ngakhale mu Baibulo.” Ayi, ayi! Izo sizidzakhala ziri zimenezo, chifukwa ngati inu mutero, izo zidzapangitsa izo kukhala... Ngati ine ndikanakuuzani inu zimenezo, ine ndikanakhala mneneri wabodza, chifukwa (inu mukuona?) Mawu awa... Apo... Chirichonse ch—chimene... Vumbulutso lonse la Yesu Khristu liri lonse kuthera mu Mawu awa. Mukuona? Ndipo ngati Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinali za kwa mipingo isanu ndi iwiri, izo zinayenera kukhala kuti zinadutsa kale, chifukwa ife tiri mu M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinali kokha kuulula zimene iwo anali atazisiyapo mmbuyo umo, ndipo izo zinatsegulapo zimene iwo anali atazisiya; zimene Lutera anazisiya; zimene Wesile anazisiya; ndi onse okonzanso, ndi Achipentekoste, ndi kutsika mpaka ku nthawi ya pakali pano.

<sup>147</sup> Tsopano, chinthu chotsatira chimene chatsalira ndi kusinthidwa kwa Mpingo, kubwerera kwa Mose ndi Eliya, ulamuliro wa Zakachikwi pa dziko lapansi limodzi naye Mkwatibwi ndi Mkwati kwa zaka chikwi, ndiyeno pa malo achiweruzo, ndipo kenako kuthetsedwa kwathunthu kwa tchimo. Silidzakhala liripo aponso pa nthawi imeneyo.

<sup>148</sup> Tsopano, osati z... Kutha... Zisindikizo sizinathetse konse nthawi. Nthawi kapena nyengo ziri mpaka zitatha Zakachikwi. Ayi! Idzakhala ilipobe nthawi mpaka zikadzatha Zakachikwi.

### **340. Kodi Zakachikwi ziri ndi chochita ndi zaka wani sauzande? Kodi izo zizingakhale kali kam’badwo?**

<sup>149</sup> Ayi! Kam’badwo kamene kanawerengeredwa mu Baibulo ndi zaka forte. Koma Baibulo linati, “Ndipo iwo anakhala ndi kulamulira naye Khristu zaka chikwi.” Izo zidzakhala ziri zaka chikwi pa dziko lapansi, chifukwa zaka chikwi pa dziko ziri kungowerengedwa ngati nthawi, monga fanizo kwa Mulungu, ngati tsiku limodzi. Zaka chikwi pa dziko lapansi ziri tsiku limodzi lokha ndi Mulungu, monga kuwerengera nthawi kwa Mulungu. Ndi angati akumvetsa zimenezo tsopano?

<sup>150</sup> Kotero, ndi tsiku la Sabata lija pamene Mpingo sudzamavutika aponso ndi tchimo. Ndipo Satana wamangidwa kwa kanthawi pang’ono, zaka chikwi, chifukwa omumvera ake onse ali mu hade, ndipo ake... Mpingo umene uli pa dziko uli wowomboledwa ndipo uli mu Kukhalapo komwe kwa Khristu, kotero iye alibe chirichonse choti angagwirirepo ntchito. Kotero, si unyolo ayi, monga ine ndinanenera, unyolo wa chipika, ndi unyolo wa zochitika; iye alibe chirichonse choti

angathe kuchita. Iye ali wopanda chomathandiza ndi wopanda chiyembekezo, akungodikira chiukitsiro cha omumvera; ndiye iwo ali kulekanitsidwa ngati nkhosa kwa mbuzi.

**341. Kodi Mfumukazi yaku Sheba siinabwere kwa Solomoni kuti idzamuyese iye—kumuyesa iye kuti akadzifufuzire yekha ng—ngati dzina la Ambuye linali moona Solomoni kapena ayi?** (I—ine sindikukhulupirira ndikulimva ilo. Dikirani chabe.) **Kodi Mfumukazi yaku Sheba siinabwere kwa Solomoni kuti idzamuyese iye kuti adzifufuzire yekha ngati dzina la Ambuye linali moona Solomoni kapena ayi?** (I—ine mwinamwake sindili kumvetsa limeneli. Basi...Ndikhululukireni ine miniti yokha. Mundirole ine ndiwerenge izo mobwereza.) **Kodi Mfumukazi yaku Sheba siinabwere kwa Solomoni kuti idzamuyese iye kuti idzifufuzire yokha ngati dzina la Ambuye linali moona Solomoni kapena ayi?**

<sup>151</sup> Ayi! Iye sanamuyese konse kuti afufuze ng—ngati dzina la Mulungu linali Solomoni. Solomoni anali mfumu. Iye anabwera, ndipo iye anati, i—iye anati, “Zoonadi Mulungu ali ndi mfumu Yake ndi anthu Ake.” Mwaona? Iye anabwera ndipo anayesedwa...Iye anamuyesa Solomoni pa za mphatso yake, chifukwa iye anali ndi zinthu mu mtima mwake zimene Solomoni anaziululira kwa iye, izo zinasonyeza kuti iye anali mfumu ya Mulungu pa dziko lapansi.

<sup>152</sup> Inu mukukumbukira uko mu, ine ndikukhulupirira, uko m—m—m...Kumene iye anachokera, uko mu dziko l—l—l—la Sheba kumene iye anachokera, anthu anali kubwera nadzerako, inu mukudziwa, n—ndi kumanena za zinthu zazikulu zimene zinali kuchitika, kuti iwo anali ndi Mulungu kumeneko amene wamudzoza mfumu yawo, ndi...momwe mfumu inadzozedwera ndi Mulungu. Ine sindikukhulupirira kuti iye ankaganiza kuti dzina la Solomoni...kapena dzina la Mulungu linali Solomoni, chifukwa ngati iye akanatero, izo zikanamupanga iye kukhala wachikunja mobwereza. Mukuona? Koteri, i—iye akanati achite zimenezo. Mu mtima mwake anakati aganize kuti Mulungu anali Solomoni, Solomoni anali Mulungu, chifukwa iye anali wachikunja pa kuyamba pomwe. Koma pamene Solomoni anaululira kwa iye chinsinsi cha mu mtima mwake mw—mwa mphatso ya kudziwa za mumtima; imene inkatchedwa, pamenepo, nzeru. Iye anazindikira izo. Iye anadziwa kuti Mulungu anali naye Solomoni, chifukwa pamenepo...Iwo anali...Iye anapeza kuti...Ngati iye akanabwera ndi zimenezo mu malingaliro mwake...

<sup>153</sup> Ng—ngati munthuyu apa, wofunsayu, ali kufunsa, “Kodi iye ankadziwa moona ndiye kuti zoonadi Solomoni...dzina la Ambuye linali moona Solomoni?” Mukuona, Solomoni sanali Ambuye; iye anali atazipeza zimenezo kuchokera mwa anthu, chifukwa iwo ankapembedza Yehova, ndipo uko kunali likasa

lalikulu, ndi pangano lalikulu, l—likasa limene malamulo a Ambuye anali umo. Ndipo iwo anamuza iye za pa Phiri la Sinai ndi malo osiyana kumene iwo anakhala aliko. Ndiyeno, iye ankakhoza kuwona kuti Mulungu—Mulungu uyo wa pangano limenelo anali mwa munthu uyu, chifukwa iye anali i—iye anali nako kuzindikira za mumtima kumene kunali kwa Mulungu yekha. Mukuona? Kotero iye anadziwa zimenezo kuti Mulungu anali mwa Solomoni. Koma tsopano, izo zikhoza kuwerengeka mwanjira imeneyo momwe wofunsayu anafunsira izo. Koma, “Kodi iye ankadziwa kuti dzina la Ambuye linali moona Solomoni?” Mwinamwake iwo sanalilembe ilo basi momwe iwo amaganizira. Inu mukuona? Kotero ine ndikuganiza mwinamwake iwo akanati—akananena izi: “Kuti Ambuye anali mwa Solomoni.” Inde, zedi anali. Chifukwa ngati ilo liri funsolo, zedi! Iye ankamudziwa Mulungu, chifukwa iye anapanga ndemanga imeneyo. Ndipo iye sakanati apembedze mulungu winawake. Ndipo ine ndikukhulupirira i—iye anati iye akanati nthawizonse. . . Iye anawona chifukwa. . . Iye analibe mpweya unatsalira mwa iye; iye analibe mafunso anatsalira mwa iye. Solomoni anangoulula chinthu chonsecho, ndipo iye ankadziwa kuti Mulungu anali naye iye.

**342. I—ife tinakwatirana zaka twente-wani zapitazo mwa chilungamo cha mtendere. K—kodi izo zinali zolakwika?**

<sup>154</sup> Inde, izo zinali zolakwika kuti inu muchite zimenezo. Chikwati ndi cha mu nyumba ya Mulungu. Koma pokhala kuti inu munakwatirana, pano ndi pamene inu mwakwatirana kwenikweni: inu mumakwatirana pamene inu mulumbirira wina kwa mzake, pamene inu mulonjezana wina ndi mzake kuti inu. . . kuti inu mutengana wina ndi mzake. Chilungamo cha mtendere chikhoza kukupatsani inu chilolezo, uko ndi kuchita kwa mwalamulo, kwa kukhalira palimodzi ngati mwamuna ndi mkazake popanda kukhala lamulo wamba la mwamuna ndi mkazake. Koma pamene inu mumulonjeza msungwana uyu ndipo uyu. . . inu mukamulonjeza mwamuna uyo kuti inu muzikhala moona kwa iye, ndipo inu nkumutenga iye kuti akhale mwamuna wanu, inu mwakwatirana pamenepo. Inu mukukumbukira, ine ndinafotokoza zimenezo sabata latha, ine ndikukhulupirira ilo linali. Mukuona? Pamene inu mumulonjeza iye. Mukuona?

<sup>155</sup> Ngakhale mu chakale—mu Baibulo lakale, ngati mwamuna anali atatomera kwa msungwana, ndipo (inu mukudziwa malamulo pa zimenezo. Bwanji, izo zinkangokhala basi chimodzimodzi ngati chigololo. Ndithudi icho chinali!) pamene iye alonjeza, izo zinali zimenezo.

<sup>156</sup> Funso linafunsidwa tsiku lina, “Kodi kulepheretsa—kulepheretsa—kulepheretsa nkofanana monga chilekano?” Mukuona? Pamene inu mundifunsa ine mafunso amenewo, mzanga, inu simukudziwa chimene izo zinkachita kwa ine.

Ine ndiri nawo amzanga ambiri akhala pano amene akwatira kawiri kapena katatu. Kodi inu mukuzindikira kuti ine ndikuyankhula kwa mwana wanga yemwe, Billy Paul? Kodi ine ndingamukondere Billy Paul? Ayi ndithudi! Billy Paul anakwatira kwa msungwana wina wamng'ono, ndipo anabwera, ndipo anati, "Adadi, ine ndikuti ndikakwatire."

<sup>157</sup> Ine ndinali kutsuka galimoto yanga; ine ndinati, "Kamenyetse mutu wako ku khoma ilo," ndinapitirira basi kutsuka galimoto langa monga choncho.

Iye anati, "Ine ndikuti ndikakwatire."

Ine ndinati, "O, pitirira nazo," ndinangopitirira nazo monga choncho. Iye anapita ndipo anakawauza amayi ake, ndipo amayi ake anamuseka iye. Inu mukudziwa zimene iye anachita? Anathawitsana ndi mwana wina wamng'ono waku sukulu wamba ndipo anakakwatirana. Ife tinalepheretsa ukwatiwo, bambo ake a msungwanayo ndi inemwini. Ife tinalepheretsa ukwatiwo, koma iye anali atakwatira chimodzimodzi basi. Iye ndi mwana wanga wakhala apa akumvetsera kwa ine tsopano. Tsopano, zimenezi ziri ndendende.

<sup>158</sup> Iye anabwera kwa ine ndi msungwana amene akukhala naye tsopano, mpongozi wanga wamkazi. Mdzukulu wanga wamwamuna wamng'ono. . . Iye anati, "Adadi kodi inu mungati mundikwatitse ine?"

<sup>159</sup> Ine ndinati, "palibe njira iliyonse." Uyo ndi mwana wanga yemwe. Kodi inu mukuganiza kuti zimenezi sizimandicheka ine mpaka mchirikati pamene ine ndinkamunyamula iye mu mikono mwanga ndipo ndinkachita chirichonse chimene ine ndikanatha kuchichita, ndipo ine ndakhala zonse bambo ndi make kwa iye? Inu mukuganiza kuti zimenezi sizimandipha ine kuti ndizinena zimenezi? Koma ndi Choonadi. Ndithudi! Mwana wanga wakhala apa akumvetsera kwa. . . Mpongozi wanga wamkazi ndi mdzukulu wanga wamwamuna wamng'ono atakhala pano pomwe tsopano. . . Koma ine ndinamuuza iye kuti ndi zolakwika (mukuona?), chifukwa ine ndikuyenera kutero. Ndine wokakamizikira kwa Mawu amenewo.

<sup>160</sup> Ndipo ine ndikuti, inu munakwatitsidwa ndi majestireti? Inu mukanati mukwatitsidwe ndi mpingo, ndi mtumiki. Ichu ndi chinthu chabwino kuti uchite pamene uli Mkristu. Koma pokhala kuti inu mwapanga kale lonjezo limenelo, ndi lumbiriro, ndipo mwakhala mutakwatirana kwa zaka twentewani zapitapo, ine ndikuganiza ziri bwino.

Inu mukuti, "Chabwino i . . ."

<sup>161</sup> Funso likhoza kukhala kuti, "Kodi ine ndibwere ndi kudzakwatitsidwa mobwereza?" Ngati inu mukukhumba kutero. Musati mukhale ndi kalikonse mu mtima wanu kamene kazivutitsa chikhulupiriro chanu, chifukwa ngati muli chirichonse mmenemo, inu simungathe kupita patsogolo kuposa



apo pomwe; inu imani apo pomwe. Pamene funso ilo libwera, ndi pamene inu mukathere, apo pomwe. Koma tsopano, kwa ine izo zikanakhala ziri zabwino.

162 Munthu amene anandibatiza ine mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu potsiriza anandithamangitsa ine ndichoke mu mpingowo, chifukwa ine sindikanatha kugwirizana naye iye pa alaliki aakazi. Zimenezo sizinandipangitse ine kuti ndibatizidwe mobwereza. Mukuona? Ayi ndithu. Mukuona? Izo zonse ziri bwino?

163 Koma ingokumbukirani, zinthu izi ndi zocheka kwa ine. Ine ndiri nawo abwenzi apamtima akhala pano, amuna ndi akazi amene angatenge zao. . . kuika zawo. . . kukolowola diso lawo ndi kulipereka ilo kwa ine ngati ine nditawapempha iwo polifuna ilo (inde, bwana!), ndipo iwo anakwatira mobwereza kawiri, nthawizina katatu, akhala pomwe pano tsopano. Ndi mwana wanga yemwe, mdzukulu wanga wamwamuna, mdzukulu wanga. . . ndi mpongozi wanga wamkazi amene ine ndimamukonda. . . Tayang'anani pa Billy, momwe ine ndaimira pafupi ndi iye ndi momwe iye waimira pafupi ndi ine, koma kuti ndinene choonadi kapena choonadi, choonadi ndi choonadi.

164 Ndiri naye. . . ine ndikanakhoza kutuluka pano lero ndi kukawaitana ena a Assemblies of God awa kapena ena a anthu awa ndi kuwauza iwo, "Ine. . . ndine. . . ndinali kulakwitsa mu zonse, ine sindikhala ndi Mawu amenewo, ine ndikhala ndi inuyo." Ine mwinamwake ndikanati ndikhale munthu wotchuka kwambiri posakhalitsa ndi mphatso ya Mulungu iyi. Kuti ndiponyere kukopa kwanga konse kwa limodzi la mabungwe amenewo, ine mwinamwake ndikanakhoza kukhala ndi dzina lalikulu pakati pa iwo. Ine sindiri kusamala za dzina langa pakati pa iwo. Ine ndimawakonda iwo, icho ndi choonadi. Koma ine ndiyenera kukhala wootsetseta. I—i—ine ndingakhale ndiri wachinyengo ngati ine ndikanachita zimenezo.

165 Ndipo ine ndikanakhala wachinyengo ngati ine ndikanaima pano chifukwa cha mwana wanga yemwe wakhala apoyo amene analonjeza kwa msungwana, ndipo ine ndikanati. . . Nga—ngati iye akanapanda kukhala nao konse ngakhale mwambo utanenedwera pa iye, ziribe kanthu ngakhale iye sanakhale naye konse mkaziyo, kapena kugona naye iye, msungwanayo, kapena chirichonse chimene chinali, pamene iye anapanga lumbiro limenelo, iye anakwatira, Billy Paul kapena asali Billy Paul. Izo ziri ndendende choonadi! Iye anakwatira pamene iye anapanga lonjezo limenelo. Ngati ndiri ine, izo ziri chimodzimodzi.

166 Ife tiyenera kukhala tiri owona mtima. Ngati ine sindingati ndikhale woonamtima kwa mnyamata wanga, ine sindingati ndikhale woonamtima kwa inu. Ngati ine sindingakhale woonamtima ndi inu, ine sindingakhale woonamtima ndi Mulungu. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzikhulupirira

zimene ine ndikukuuzani inu kuti ndi lingaliro loona mtima labwino. Musati muzipanga china chirichonse kuchokera mwa icho, muzingonena izo momwe ine ndanenera izo (mukuona?), chifukwa ine ndikuti ndizikuuzani inu Choonadi.

<sup>167</sup> Tsopano, ine sindimayankhula kwa inu nonse monga choncho mowirikiza, chifukwa inu ndinu ana anga, ine ndimakutchani inu. Ine ndakubalilani inu kwa Khristu kudzera mu Uthenga. Ndipo pamene ife tiri pano palimodzi, basi gulu lathu lomwe lomwe liri pano, i—ine ndimakumetani inu pang'ono pokha. Koma ine ndikufuna kumakuuzani inu: koma pamene inu mubwera kwa ine ndi kundifunsa ine chinthu chirichonse, ine ndikuti ndizikuuzani inu mwa kupambana kumene ine ndikukudziwa! Ngati izo ziri mu Mawu, ine sindikusamala ngati izo zikunditsutsa ine, ine ndiri ndi mfundo zambiri zoti zimetedwe kuzichotsa pa ine. Ndendende!

<sup>168</sup> Koma pamene inu mundifunsa ine chirichonse, ine ndikuti ndizikuuzani inu. Ngati ine ndizikuuzani inu chirichonse, ndizikuuzani inu Choonadi. Ine nthawizonse ndayesera kumakhala moyo mwanjira imeneyo. Umo ndi momwe ine ndikufuna kumakhala moyo ndi kudzafa mwanjira imeneyo, kuti ndizikhala woonamtima naye aliyense.

<sup>169</sup> Msungwana wamng'ono anabwera kwa ine si kale litali; mkaziyo sali pano tsopano. Tom Simpson, ambiri a inu mukumudziwa iye. Tom ndi munthu wabwino; palibe abale ake ali pano. Ine ndikuganiza anthu awo onse anabwerera mmbuyo, kupatula ngati Fred akadali kuno. Ine... Fred Sothmann, ine sindikudziwa ngati iye ali pano kapena ayi, koma i—iwo ndikuganiza iwo ali. Koma Tom Simpson, iwo... iye anabwera kuno kuchokera ku Canada n—ndi Fred. Ndipo iwo... Inu mukumudziwa M'bale Fred, trastii wathu.

<sup>170</sup> Ndipo M'bale Tom, ambiri a inu mukumudziwa iye kuno. Ndipo Tom ndi munthu wabwino; iye ndi mwamuna wabwino zedi; ndi momwense aliri Akazi a Simpson. Ngati iye angamvetsere kokha ku zimene ine ndikumuuza iye, iye angati ayendenso kachiwiri. Ndipo iye wakhala ali mu chikuku icho wolumala choncho. Iye adzayenda ngati iye angochita zimene zinanenedwa kuti achite. Ndipo inu mungopenya ndi kuwona ngati izo si zoono. Mukuona? Tsopano. Koma iye akuyenera kuti achite zimene iye anauzidwa kuti achite ngati iye akuyembekeza kuti achite izo.

<sup>171</sup> Ndipo mmodzi wa asungwana ang'ono, asungwana aang'ono okoma... i... Pamene iwo anali tinthu tating'ono, ine ndinkakhoza kuwatenga iwo pa chilolo changa ndi kumasewera nawo iwo. Iwo akula kwambiri tsopano; iwo ndi azimayi pafupifupi, khumi, usinkhu wa zaka khumi ndi ziwiri. Ndipo chotero, mmodzi wa iwo anabwera kwa ine ndipo anati, "M'bale

Branham, ine ndinali ndi loto.” Ndipo iye anandiuza ine lotolo. Ndipo iye anati, “Kodi zimenezo zikutanthauza chiani?”

Ine ndinati, “Sindiri kudziwa, Wokondedwa. Ine ndipemphera, ndipo ngati Ambuye azipereka izo kwa ine, ine ndidzakuuza iwe.”

<sup>172</sup> Iye anati, “Chabwino!” Masiku pang’ono iye anabwerera, anati, “Mwalipeza loto lija?”

Ine ndinati, “Ayi, Wokondedwa, ine sindinalipeze; Iye sanaululire ilo kwa ine.”

<sup>173</sup> Pafupi sabata kapena awiri kenako iye anabwereranso, anati, “M’bale Branham, nanga bwanji loto lija?”

Ine ndinati, “Ine sindiri kudziwa.” Chabwino, ankawoneka ngati iye anali monga wokhumudwa. I . . .

<sup>174</sup> Inu muzikumbukira, pamene inu mundifunsa ine chirichonse kuti ndikuuzeni inu, ndipo ine ndikapanda kuchipeza icho kuchokera kwa Ambuye, ine ndimakhumudwa nanenso. Koma ine sinditi ndikhale wachinyengo, kapena wabodza, ine ndidzakuuzani inu choonadi. Ngati Iye ati andiuze ine, ine ndizikuuzani inu; ngati Iye satero, ine sinditero. Ndizo zonse zimene ine ndingathe kuchita. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikhulupirira ine mwanjira imeneyo.

<sup>175</sup> Ndipo tsopano, ine ndinkaganiza kuti ine ndinkadziwa chimene loto limenelo linkatanthauza mu malingaliro anga, koma ine ndingadziwe bwanji. Ine ndimayenera kuti ndichiwoneso chinthucho kachiwiri. Ndipo palibe mmodzi wa inu amene angalozе chala chake pa nthawi iliyonse kapena malo aliwonse, pamene ine ndinayamba ndakuuzanipo inu kutanthauzira kwa loto mu Dzina la Ambuye kupatula pamene zinali ndendende mwanjira imeneyo. Inde, bwana! Ine sindinayambe ndakuuzani inu chirichonse mu Dzina la Ambuye kupatula chimene chinafika pochitika nachonso, basi mwanjira imeneyo basi, chifukwa ndine—i . . . Ndi Iyeyo. Ndiyeno si udindo wanga pamenepo, ndi Iyeyo; ndi udindo Wake.

<sup>176</sup> Ine ndinati, “Taona, Trudy, bwanji ngati ife timapita ku Arizona. Ndipo bwanji ng—ngati ine nditabwera kudzakuuza iwe kuti pamene iwe ukafika uko, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE, mchimwene wako wamng’ono akachita . . .’ Johnny wamng’ono, amene ine ndimamutanza kuti amakhala ndi mimba yake yotsegula nthawi zonse.” Ine ndinati, “Bwanji ngati iye atagundidwa pa msewu? Ndipo ine nkuti, ‘Iwe ukudziwa chimene chiti chikachitike? Iye akagundidwa pa msewuwo.’ Ndipo iwe ukabwera kwa ine, n . . . ndipo iwe udzanena, ‘M’bale Branham . . .’ ‘Pitani mumutengere iye kwa M’bale Branham,’ maka. Ndiyeno iwe ukafunafuna konseko, ndipo iwe ukandipeza ine nditaima pa masitepe, ndikuyankhula kwa bambo atavala suti yoyera. Ndiyeno ine ndidzangoika manja

anga pa Johnny wamng'ono; iye adzabwerera ku moyo aponso ndi kumathamangathamanga.”

Tsopano, ndinati, “Ndiye iwe nkupita kwina Kumadzulo, ndipo chinthu choyamba iwe ukudziwa, tsiku lina iwe ukuwamva amayi ako akufuula, adadi ako akufuula, ndipo kuyang'ana, ndi Johnny wamng'ono amene wagundidwa. Kodi iwe ukanachita chiyani?” Ukuona? Iwe ukundikhulupirira ine. Ukuona? Ndipo ine ndikufuna kuti ukhale nacho chidaliro mwa ine. Ine sinditi ndikuuze kanthu mwa kungopenekera; ine ndizikuuza iwe zoono, kapena osakuuza iwe kalikonse. Ndipo ine ndinati, “Ndiye iwe nkubwera kwa ine ndi kuti, ‘O, Johnny wamng'ono. . .’ Kapena, kubwera kwa amayi ako, ‘O, Johnny wamng'ono wagundidwa. Iye wafa! Iye wafa!’”

<sup>177</sup> “Adokotala kubwera, kukokera maso ake mmbuyo, kufufuza mtima wake, kupuma kwake. ‘Iye wafa. Kumutengera iye kosungira mitembo.’”

“Kodi iwe ukanachita chiani? Iwe ukananena kuti, ‘Dikirani miniti yokha! Dikira miniti yokha! Muikeni iye mu mikono yanga; tiyeni tiyambe kuyenda.’” Ameni!

“Kodi iwe ukupita kuti, Trudy?”

“Ine sindikudziwa.”

“Iwe uli ndi chiani?” Iwe uli ndi mchimwene wako wamng'ono mu mikono yako. Kumangopitirira kuyenda kutsika ndi msewu. Anthu kumati, ‘Kodi msungwana ameneyo wapenga?’ Ayi, bwana!” Ali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Chiti chichitike ndi chiani?

<sup>178</sup> “Chinthu choyamba iwe kuchidziwa, iwe unena kwa bambo ako ndi amako, ‘Dikirani, ife timupeza M'bale Branham. Iye akhala ataima pa masitepe akuyankhula kwa mwamuna atavala suti yoyera. Ndi uyo waima apo pomwepoyo. Penyani zimene ziti zichitike.’ Wopanda kukaikira mu malingaliro ako. Kuyenda nkubwera pamenepo ndi kuti, ‘M'bale Branham, inu mukudziwa zimene inu munandiuza ine?’”

“Inde, Trudy. ‘Johnny, dzuka!’ Kulumphapo ndi kumapita ku msewu.”

<sup>179</sup> “Koma bwanji ngati ine nditakuuza iwe mopenekera zinthu zina zimene ine ndikungoganiza kuti ndi zolondola, ndi kukuuza iwe kachitidwe kameneko, PAKUTI ATERO AMBUYE, ndipo izo zisali zoono, ndipo izo nkusachitika, izo nkusafika pa kuchitika; ndiye iwe ukanakhala woopsyetsedwa mwa imfa pa za mnyamata wamng'onoyo. Iwe sukanati udziwe kaya kuti umubweretse iye kapena ayi.”

<sup>180</sup> Mulungu anandituma ine kuno kuti ndizikuthandizani inu, ndipo ine ndikufuna kuti ndikhale thandizo kwa inu. Ndipo ziribe kanthu ngati izo zikucheka, kupweteka kapena

chirichonse chimene chiri, ine ndiyenera kuti ndizizina izo mulimonse.

<sup>181</sup> Koma tsopano pa nkhani ya chikwati ndi chilekano, ine ndakupemphani inu ngati m'bale, sungani mtendere wanu mpaka inu mumve kuchokera kwa ine. Mukumva? Basi zipitirirani nazo momwe inu munali kukhalira. (Ine ndikutenga nthawi yochuluka kwambiri pamenepo.)

<sup>182</sup> “Ife tinakwatirana zaka twente wani zapitazo (eya)... chilungamo cha mtendere.” Mlongo Wokonedwa, M'bale wokonedwa, nthawi ina bambo wamalonda anali kundiuza kuti iye anayenda nalowa mu tchalitchi (iye anali Mkhirsitu) uko ku Connecticut kapena kwinakwake kumtunda uko, tchalitchi chachikulu kwambiri, anangolowa mkatimo kuti apemphere. Icho sichinali...Iye anali Wachipentekoste koma iye analowa mmenemo kuti akapemphere. Ndipo anati pamene iye analowa mkati umo ndipo anagwada pansu mu tchalitchimo kuti apemphere...anati iye anali akuyendetsa mopitirira, anali atatopa, anali ngati atapukwa, iye bambo wamalonda, ndipo iye akugulitsa zinthu, ndipo anati iye...ku mafakitare. Ndipo iye anapita mkati umo ku—kuti akapange zogula zina kapena chinachake, ndiyeno iye anadzera pa tchalitchicho, anaganiza, “Ine ndipite...Ine ndikukhulupirira kuti ine ndipite mkati umo ndi kukapemphera.” Chitseko ndi chotsegula; anati iye analowa. Sanamumve wina aliynse, chotero iye anagwada pansu ndipo anayamba kupemphera. Atha kupemphera mmenemo, anakhala pafupi ora, anati, molunjika iye anamva zitseko zina zikumenyetsedwa kapena chinachake; iye anaganiza kuti anali woyang'anira kapena chinachake cha pa tchalitchipo. Anati, patapita kanthawi iye anazindikira, apa panabwera... Iye anamumva winawake akuyankhula. Iye anasuzumira pamwamba apo ndi kuyang'ana, ndipo anayang'ana pozungulira kuti awone ngati anali woyang'anira pa malopo. Anali mwamuna ndi mkazi ataimirira patsogolo pa guwa atagwirana manja awo, anati, “Ine ndikukutenga iwe, wokonedwa, kuti ukhale mkazi wanga wokwatirana naye movomerezeka.” Mukuona?

Iye anati, “Ine ndikukutenga iwe, wokonedwa, kuti ukhale mwamuna wanga wokwatirana naye movomerezeka.”

“Bwanji,” iye anati, “ichi ndi chinthu chachirendo,” anati, Wachipentekoste uyu, iye anati, “mwamuna uyu ndi mkaziyu akukwatitsidwa popanda mlaliki.” Mukuona? Ndipo chotero iye anangokhala pansu ndipo anadikirira; ndipo iwo atatha kupanga malumbiriro awo kuti azikhala owona kwa wina ndi mzake, imfa yokha ikanati idzawalekanitse iwo, iwo anaika mikono yawo mokumbatirana wina ndi mzake, anapsyopsyonana wina ndi mzake, anapotoloka apo ndipo anayenda natuluka akumwetulira. Iye anati, “Mphindi yokha!”

Iye anati, “Ine ndiri ndi chidwi; Ine ndine mlendo.” Anati, “Inu nonse mukukwatirana?”

Anati, “Inde!”

“Popanda mlaliki?”

Iye anati, “Ayi!” Anati, “Ife takhala titakwatirana zaka forte.” Iye anati, “Ife tinakwatitsidwa pano pomwe pa guwa ili zaka forte zapitazo, ndipo chaka chirichonse ife timabwera ndi kudzapanga mwatsopano malumbiro athu.” Limenelo ndi lingaliro labwino. Mukuona?

<sup>183</sup> Koma kunena za kukwatira, pamene iwe umulonjeza iye, iye amatenga mawu ako; iwe umatenga mawu ake; ndipo Mulungu amatenga mawu anu nonse. Mukuona? Koma musamati muzingolonjeza kupatula... [Gawo loyamba la tepi litha—Mkonzi.]

**343. Pamene iwo alidulira ilo mkati...Kodi lalitali—kodi tsitsi lalitali liri pamene iwo alidula patsogolo?** (Tsopano, dikirani miniti, ndiroleni ine nditenge ili apa.) **Kodi tsitsi lalitali liri pamene iwo...**

<sup>184</sup> Chabwino, i—ine...Mwinamwake iwo akutanthauza ichi: “Kodi ilo ndi tsitsi lalitali aponso pamene iwo alidula ilo patsogolopa?” Silikhala aponso lalitali, iwo alidulapo ilo. Mukuona? Koma monga mwamuna amene anali atadula tharauza lake katatu ndipo nkukhalabe ili yaifupi. Mukuti chiani? Mukuti chiani? [M’bale Branham akukambirana ndi winawake mwa omvetsera—Mkonzi.] O, izo ndi zimene iwo akunena. Monga momwe ine ndimamutonzero msungwana wanga wamng’ono, iye anati... “Mabumu” ine ndimazitcha izo, inu mukudziwa, mabang’i, kapena chirichonse chimene izo ziri, inu mukudziwa, chopingasa patsogolo apa.

<sup>185</sup> Chabwino, ine ndikulingalira ana awo amene akumadula tsitsi lawo patsogolopa...Inu, mwina amayi anu akanakhoza kukuuzani inu za zimenezo, mukuona, ngati iwo akufuna kuti inu muzichita mwanjira imeneyo. Ine ndikuganiza izo zikanati ziziwoneka ng—ngati pang’ono pokha monga mkazi amayang’ana kudzera pa galasi loyang’anira mmbuyo ngati iye atadutsa pafupi usinkhu wa zaka twente faifi ndipo nkumafunabe kuti azidulira ilo kutsogoloku monga choncho, kuwoneka ngati mwana wina wamng’ono. Ziyang’anani patsogolo uku kumene inu mukupita, mlongo, osati kumene munakhala muli. Mukuona?

<sup>186</sup> Ndipo tsopano, koma kudula tsitsi, i—i—i—ine ndikuuuzani inu ichi. Ine sindingathe—i—ine ndiribe—palibe Lemba lonena kuti inu mukhoza kudula mochulukha chonchi la ilo ndipo simungati muchite mwinamo. I—ine ndiribe Lemba la zimenezo, i—ine sindikanati ndikuuuzeni inu zimenezo, mlongo, kapena m’bale, aliyense amene ali.

187 Ine ndimanena chinthu chimodzi. Ine ndimakhumba... Tsopano, ine ndikudziwa ana anga nawonso achitapo zimenezo, Rebekah ndi Sarah, ine ndinawona pamene iwo anadula tsitsi lawo patsogolo apa, ndi kulilukira ilo kumbuyo apa mmbuyomu, ndi kupangitsa zinthu izi kudutsa kutsogoloku, monga chonchi. I—ine sindi, i—ine... Tsopano, osati kuwagwira iwo. Mukuona? Ayi, bwana! Kwa ine, ine ndimakhumba iwo akanati asaike ngakhale lumo pa tsitsi lawo konse. Koma pamene iwo ali nalo lonse lalitali, likulendewera pansu monga chonchi, ndi kungodula kutsogolo kwa ilo kulichotsa pamaso awo, ana aang'ono mwinamwake... i—ine sindingati ndidziwe ngati uko kukanakhala... ine sindikanati ndiganize chotero. Mukuona? Koma pamene inu mutenga... Ngati inu mungathe, i... kwa inu alongo, ine ndingangolisiya momwe Ambuye analipangira ilo. Mukuona?

188 Ndipo ndithudi, ine ndikudziwa akazi amafuna kuti aziwoneka okongola; chimenecho ndi chibadwa, ndipo iz—izo ndi zimene iwo ayenera kumakhala ali. Mukuona? Iwo ayenera kumakhala mwanjira imeneyo. Ndipo chotero, zimenezo ziri bwino, koma basi musati—musati... mwanjira ina monga chonchi, musati muziwoneka ngati dziko (mukuona?); musati muzitengera za mdziko. Zinthu zolakwika... Inu mukufuna kulidulapo ilo, monga choncho, koma musati muzidula tsitsi lanu tsopano. Ngati inu muli ndi mangongo akulendewera pansu, k—kapena chirichonse chimene chiri mu tsitsi lanu, inu muzilisiya ilo lalitali. Musati muzilidula ilo kuti lizichita kuwoneka ngati dziko. Ngati inu muli chabe asungwana aang'ono awo...

189 Amalume anga anali ndi msungwana wamng'ono kumtunda uko m—mu New York. Iye anali ndi tsitsi lokongola kwambiri. Ilo ndi lokhala ngati la bulawuni woderapo ndipo iye amavala mangongo ake... Amayi anga ankakhoza kukwanitsaku... Mangongo awo ankagunda pansu apa kumbuyo kwa mawondo awo. Ndipo msungwana wamng'ono uyu anali ndi mangongo ngati amenewo nayenso; dzina lake linali Jacqueline. Ndipo iye anali atalipesera gawo la ilo pansu monga chonchi ndi kulidulapo ilo monga chonchi. Ndipo ine ndinali... Izo zakhala ziri pafupi zaka fiftini, eyitini, twente zapitapo. Ndipo ine ndinkadabwa, chifukwa chiani iye sanangopesera chinthu chonsecho kumbuyo, izo zikanawoneka mokongolerapo kusiyana ndi kungokhala nalo ilo monga basi, kulichotsa apa ngati Mabitolo amakono awa ali nalo masiku ano, inu mukudziwa. Ndipo... O, uko nkulondola, ine sindikuhulupirira kuti ine ndikanachita zimenezo. Chirichonse chowoneka ngati Mabitolo awo, zimenezo zimawoneka ngati zochokera mdziko, chotero siyani... mungolisiya ilo lokha. Eya!

**344. Amuna anga ndi ine sitimawona mofanana pa Baibulo, Zoonadi, monga Choonadi ichi chimene inu**

**mukuchilalikira. Iye samamvetsa. Kodi inu ndizipita naye iye ku mipingo pamene ine sindiri kukhulupirira kaphunzitsidwe kawo? Ine ndikusautsika nazo izi.**

<sup>190</sup> Inde! Ngati inu muli mkazake kwa mwamuna uyu, ndipo iye samakutsutsani inu, inu musati—inu musamamutsutse iye (mukuona?), chifukwa mwamuna amayeretsedwa ndi mkazake. Mukuona? Ndipo ine ndikukhulupirira, ngati iye akupita ku mpingo wina wachipembedzo kapena chinachake chonga chimenecho, iye akufuna inu kuti muzipita kumeneko ndi iye... Inu mukuona? Ngati inu simukhala... Onani, palibe kalikonse kumeneko kamene kangakakupwetekeni inu, chifukwa inu simukupita kuti mukamvetsere kwa zimene iwo akunena mulimonse, chifukwa inu mwanena kale apa kuti inuyo simumakhulupirira malalikidwe awo. Mukuona? Kotero izo siziti zikakupwetekeni inu, koma inu mukungosonyeza malemekezo kwa mwamuna wanu. Inu mukudzipereka nokha kwa iye, ndipo mwinamwake pakutero, i—inu mudza... Ngati iwo aziphunzitsa ndi kumachita zinthu kumeneko... Inu mwaphunzitsidwa zinthu zapamwamba kwambiri kuposa zimenezo; inu mukakhale amchere; iye adzawona ndi kubwera kwa Ambuye. Ine ndikukhulupirira ine ndikanati ndipitirire nazo. Ubwino wanga, taonani apa nthawi imene ili!

**345. Kodi Zakariya 4 ndi Chivumbulutso 11:3-12, amayankhula za chinthu chofanana? Tiwone Zakariya 4:12-14 ndi Chivumbulutso 11:4. Iwo analembapo dzina lawo kwa ilo, m'bale ndi mlongo wa pa mpingo pano.**

<sup>191</sup> Tiyeni tiwone, Zakariya 4. O, eya, iyo ndi mitengo iwiri ya azitona. Eya, mitengo iwiri ya azitona ndi Chivumbulutso 11 ziri... O, eya, ndi zimenezo. Chinthu chofanana. Ndi iyo yonse. Awo—amenewo—ali Mose ndi Eliya, mitengo iwiri ya azitona.

Mumupempherere wathu... Ilo ndi pempho la pemphero.

Ine ndikupepesa, izi ine sindingawerenge izo pamaso... Izo ndi za ubale wa m'banja. Eya, ndiziyika izo limodzi ndi ichi apo. Sindingati ndiwerenge izo pa gulu. Iwo ali pa kuyankhulana kwa padera mulimonse, k—kotero...

**346. M'bale Branham, kodi ndi kulakwa k—ku... [M'bale Branham akuyankhula ndi winawake pa nsanja—Mkonzi.] Kodi ndi kulakwa kugwira ntchito Lamlungu?**

<sup>192</sup> Ine ndafotokoza kumene zimenezo. Ngati ng'ombe ili mu dzenje, itulutsenimo iyo, koma musati muikankhire iyo mu dzenjelo basi kuti mudzaitulutsemo iyo Lamlungu!

**M'bale Branham, kodi inu mudzalalikira kuno Lamlungu likubwerali?**

<sup>193</sup> Limenelo ndi funso chabe. Ayi, Mlongo, M'bale, aliynse amene ali. Tsopano, awa ali ena amene anali basi panja apa.



Ndiyenera kuti ndinawaika—ndinawaika iwo, kapena winawake anawaika iwo mu kathumbaka.

M'bale...Izi ndi za inu, M'bale Capps. “Kodi inu mungaimbe, *Ife Sitidzakalamba konse?*” Ine ndiyenera kuti ndinaika mu... Ine ndinaika ena a onsewo mosakaniza.

**347. M'bale Branham, winawake akufuna kuti adziwe chifukwa chimene inu simu (s-i-m-u-...) simunatchulidwe mu Baibulo. Ine ndikukhulupirira kuti inu ndinu Habakuku 2:1-4. (Pezani pamenepo, M'bale Neville, Habakuku 2:1-4) Aloleni iwo awerenge izi ndi kuziphunzira izo, mutu wa 3...ganizani dzina ndi zoimira za mitu inayiyo, kukhulupirira—ine ndikukhulupirira ndi inuyo.**

<sup>194</sup> Tsopano, pamene iye akupafuna pamenepo, ndi pa Habakuku 2:1-4. M'bale kapena Mlongo, aliyense amene wafunsa funsoli (apa palibe dzina) izo ziri bwino, i—ine ndikukonda kuti inu muzifunsa zinthu zimenezo. Ine ndimadziwa zimene ziri pa mtima wanu (mukuona?), ndiyeno ine ndikuuzani inu. Ayi. Mukuona? Inu simukanati mufunikire kukhala ndi dzina lanu mu Baibulo, mwaona. Koma, inu onani, bola ngati inu muli mu Baibulo, umo... Bola ngati inu muli mwa Khristu, inu muli mu Baibulo; inu muli mwa Iye, inu mukuona, mu Baibulo. Mukuona? Bola ngati inu muli mwa Khristu, ndiye inu muli mu chidzalo cha Baibulo. Mukuona? Inu muli pa malo anu amphumphu pamene inu muli mwa Khristu. Nonse mukumvetsa zimenezo?

<sup>195</sup> Kodi inu muli napo apo, M'bale Neville? Chiani? Eya. Habakuku—Habakuku... Ine sindinapawerenge apo. Ili linangoikidwa mkati umu, ine ndikulingalira, mmawa uno. Habakuku 2:1-4. Ndi pamenepo. Habakuku 2—Habakuku 2, ndipo 1 mpaka 4:

*Ine ndidzayima pa ulonda, ndi kudziika ine pa nsanja, ndipo ndidzayang'anira ndi kuwona zimene iye ati anene kwa ine, ndi chimene ine nditi ndiyankhe i—ine ndiri... pamene ine nditsutsidwa.*

*Ndipo AMBUYE anandiyankha ine, ndipo anati, Lemba masomphenyawo, ndi kuwapangitsa kumveka pa magome, kuti iye akhoza kuthamanga amene awawerenge iwo.*

*Pakuti masomphenyawa ali apabe a kwa nthawi yoikidwiratu, koma pa mapeto iwo adzayankhula, ndipo sadzanama: ngakhale iwo angachedwe, adikirire iwo; chifukwa ine ndidzabwera ndithu, ndipo ine sindichedwa.*

*Taonani, moyo wake umene wakwezedwa pamwamba suli wolungama mwa iye: koma olungama azikhala moyo mwa chikhulupiro chake.*

<sup>196</sup> Chabwino, tsopano, i—ine ndikulingalira munthu wokondedwa uyu amene wafunsa izi. . . Inu mukuona? Ndi winawake amene amandikonda ine, kapena iwo sakanati alembe izo. Mukuona? Tsopano, ine sindikanati ndinene kuti. . . Baibulo silimatchula dzina—dzina langa, *William Branham*, kapena kutchula dzina lanu aliyense yemwe ali, koma ife tiri mwa Iye mulimonse. Ndipo izi. . .

<sup>197</sup> Ndipo tsopano, inu mumawona malo odziwika amene amalozera, mu Baibulo, amene amanena zinthu zinazake. Inu mukuona? Tsopano, ngati inu mungapenye, mbiriyakale imadzibwereza yokha mu Baibulo. Mukuona? Tsopano, tiyeni tingokupatsani inu Lemba la imodzi tsopano. (Ine ndikuwona ambiri a inu mukuzilemba izo apo.) Tsopano, mu mutu wachitatu wa Mateyu Woyera, Apo anati, “Ndipo pamene Mulungu anamuitana Mwana Wake atuluke mu Igupto kuti chikakwaniritsidwe chimene chinanedwa, ‘Kuchokera mu Igupto Ine ndimuitana Mwana Wanga’ . . .” Tsopano, ngati inu muli nalo—la Scofield kapena Baibulo lirilonse lokhala ndi lolozera, ngati inu mungatsatire kulozera uko pamenepo, kuwerenga kwa mmphepete, iko kukubweretsani inu mmbuyo kumene Iye anamuitana Yakobo, Israeli, atuluke mu Igupto. Mukuona? Koma Yakobo anali Mwana Wake amene Iye anamuitana kuchokera mu Igupto; ndiponso Yesu anali Mwana Wake amene Iye anamuitana kuchokera mu Igupto. Chotero (mukuona?) Mawu a Mulungu ali osatha konse. Mwaona, ife timadzizindikiritsa tokha mu Baibulo ndi zosiyana. . . Ndi angati akukumbukira uthenga wanga wa kudzizindikiritsa wekha ndi makhalidwe a Chikhristu, Phoenix, Arizona, kumene ine ndinaulalikira iwo? Eya, ambiri a inu muli nawo iwo pa tepi. Mukuona? *Kuzindikiritsidwa ndi Khalidwe la Chikhristu*. Mukuona? Inu mukhoza kudzizindikiritsa nokha kulikonse kumene inu mukufuna kutero mu Lemba limenelo ngati inu muli Mkhristu, ndipo ngati inu simuli Mkhristu, inu mukhoza kudzizindikiritsa nokha mu Baibulo. Mukuona? Kotero ine ndikuganiza mwinamwake zimenezo zikhoza kuthandiza. Ine ndikufuna kuti nditenge ochuluka a awa momwe ine ndingathere.

**348. M’bale Branham, ena akumanena kuti chifundo chatha ndipo palibe wina amene angati apulumutsidwe. Tsopano, kodi izi ndi zooni? (Ine ndiri wokondwa ine ndiri nalo ili.) Ife tikupenyenera ndi kupemphera. . . Ife tikupenya mizere ya pemphero, ndipo zikuwoneka kuti ena ali kupezabe chifundo.**

Tsopano, limenelo ndi funso loyamba, inu muli nawo awiri.

<sup>198</sup> “Kodi chifundo chatha?” Musati muziganiza zimenezo konse! Mukuona? Zipitirirani nazo basi kumachita chirichonse chimene inu mungathe mpaka inu mudzatengedwere kwinako. Mukuona?

199 “Ife tikuzindikira mu mzere wa pemphero ena akumapeza chifundo.” Ndithu! Zifundo, zitseko ziri zotseguka. Mukuona? Ine ndikuganiza pamene inu mukupeza, ilo, lingaliro ili likhoza kukhala pakati. . . Onani, ine ndiribe nthawi yoti ndipereke aliwonse a Malemba awa malo awo oyenera, (inu mukuona?), chirichonse cha zinthu izi malo awo oyenera. Iwo. . . Mu mzere wa pemphero inu mukupezamo chifundo, ndithudi.

200 Ngati ine ndikanadziwa kuti Yesu anali kubwera madzulo ano, ine ndikanakhala ndikuchita basi chinthu chimene ine ndikuchita pakali pano (mukuona?), kumapitirira nazo basi. Chifundo chiri nthawizonse chotseguka. Mukuona?

201 Ndipo tsopano, pamene ine ndikuganiza kuti inu munazitenga izo, ndi pa kutsirizitsa kwa Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri kukhala zitamasulidwa. Mukuona? Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, zawonetsera zimene zinachitika. . . zimene zakhala zitachitika. M’badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri, ife tiri pa mapeto a M’badwo wa Mpingo wa Chisanu ndi chiwiri. Pamene ine ndikuti *mapeto*, zimenezo sizikutanthauza ora lomwe lino, miniti yomwe ino. Inu kumbukirani, Baibulo linati, mmbuyo mu masiku a—a Ambuye Yesu, Paulo anati, “Pakuti nthawi ili pafupi.” Kodi inu mukuzindikira kutalika kwake komwe kunali mu nthawi ya Mulungu? Limenelo linali dzulo. Nthawi yanga, izo zakhala ziri zaka zikwi ziwiri. Mukuona? Nthawi ili pafupi. Mukuona? Chimene Mulungu akuchittha *pafupi* si zimene ife tikutchi *pafupi*. Mukuona?

202 Kotero zikhulupirirani mopitirira basi, pitirirani nako kupemphera, pitirirani nazo. . . Mulungu akadali nacho chifundo chotseguka; pitirirani kupita mu icho mwamsanga momwe inu mungathere. Mulungu achita kuimitsako pamene ili nthawi yoti aimitse. Mukuona?

**349. Tsopano. M’bale Branham, kodi ndi zowona kuti palibe wina angati azilalikira kupatula inu? Ife taona anu— ife takuanani inu mukuwadzoza amuna. Ife tiri—sitiri kukhulupirira kuti inu mukanati muchite zimenezo ngati iwo akanati asama. . . ngati iwo akanati asalalikire.**

203 Chifundo! M’bale, mlongo, aliyense amene anakuuzani inu zimenezo kuti palibe wina woti azilalikira kupatula ine, ine zedi ndingakhale chinthu chosauka kwa Mulungu ndi zonse zimenezo. Ayi! Mwamuna aliyense kapena. . . amene akumverera kuitana kwa Mulungu pa moyo wake, alowe mu utumiki ndi kuyamba kulalikira; ife tikuwasowa iwo.

204 Amuna a Mulungu ali odzozedwa konsekonse mu dziko kuti azilalikira Uthenga. Mukuona? Ine ndine nsangalabwi imodzi yokha yaing’ono pa gombe pakati pa miyala yambiri yaikulu. Mukuona? Kotero ine. . . Alipo ambiri amene ali okhoza kwambiri, oyenera kwambiri, ochuluka mu chirichonse

kuti azilalikira kuposa ine; ine ndine basi munthu mmodzi wamng'ono, wonyozeka amene ndiri kunjja kuno. Ine ndine njere imodzi ya tirigu mu nkhekwe yonseyi. Mukuona? Chotero izo zangokhala. . . Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza!

<sup>205</sup> Mwamuna aliyense amene ali wotanidwa ndi Mulungu ali woti azilalikira Uthenga.

**350. Kodi Mkhristu angazame bwanji mu chikondi cha Mulungu?**

<sup>206</sup> Ziwerengani Mawu ndi kupemphera. Ziwerenga Mawu a Mulungu ndi kumapemphera. Ine ndikuti ndifulumire, ndingotenga ambiri momwe ine ndingathere.

**Ine ndinapereka umu funso limodzi, koma ndinafunsa ilo (m-o-s-a-. . .) mosalondola. Ine ndikufuna kudziwa ngati inu muti mukhale ndi msonkhano wa machiritso musanachoke mu mzindawu. Ngati si choncho. . . ndiyenera kuchita. . .ine ndikhale nako kukambirana kwandekha ndi inu?**

<sup>207</sup> Tsopano, tiri chiyankhulire, ine ndikuganiza munthu uyu anali pa zoyankhulana mmawa uwu. Chifukwa, ife tinali ndi msonkhano wamachiritso; ife tinali nawo msonkhano wa machiritso aponso.

**351. M'bale Branham, chonde talongosolani Akorinto Woyamba—Akorinto Woyamba 11—11, ndi ndime ya 4 mpakana 6. Kodi izi sizikutanthauza (c-h-o-. . .) Chophimba chapadera kwa tsitsi, kapena kodi tsitsi lalitali ndilo chophimba chokha chimene ife timachisowa?**

<sup>208</sup> Ndipezereni ine Akorinto Woyamba 11. Tiyeni tiwone, Akorinto Woyamba 11:4. Akunena kuti, Pamene mukupemphera. . ." O eya, iye. . .Iwo anazitenga izo pamenepo. Iwo akuti, "Pamene mukupemphera kapena kunenera, kodi ife tingamachotse tsitsi lathu—kodi ife. . ." Tiyeni tiwone, iwo alemba mzere modutsa chinachake apa.

**Pamene tikunenera—pamene tikunenera, kodi ife tingatenge tsitsi lathu pamene ife. . .Inu munati: Kodi ife tingamavale tsitsi lathu kapena kulivula pamene ife tikunenera?**

<sup>209</sup> Ngati i—ngati inu muli ndi chidutswa cha tsitsi, inu mukhoza, koma i—ine ndingati. . .kapena kuvala imodzi ya mawigi a Mabitolo iyi, kapena chinachake, koma. . .Ngati ine ndikanati ndiziwoneka bwino mu imodzi, ine mwinamwake ndikanati ndizivala imodzi inemwini, koma iyo. . .osati wigi ya Mabitolo, koma ch—chidutswa cha tsitsi.

<sup>210</sup> Koma izo zonse nzabwino. Ngati inu mulibe tsitsi ndipo inu mukufuna ina. Ngati inu mungathe kuchita izo, zimenezo ziri zabwino mwangwiro. Inde, bwana! Ngati mkazi, tsitsi lake

siliri lalitali mokwanira, iye akufuna tsitsi lophimba bwino mmenemo, ine ndingati, zilivalani ilo, Mlongo.

<sup>211</sup> Ngati mwamuna amatenga chimfine choipa ndi zinthu, ndipo akufuna . . . njira ina . . . ngakhale mwa mawonekedwe ake kwa mkazi wake, ngati iye amafuna kuti azivala chidutswa cha tsitsi, zichitani izo. Inde ndithudi. Palibe kanthu kolakwika ndi zimenezo (ayi, bwana!) mopanda kuposa momwe inu mukadachitira ndi mano anu, kapena mkono woyikirira, kapena chinthu china chirichonse. Ngati chibadwa chiri ndi zina—anachotsa chinachake kwa inu ndipo icho chiri chothandiza kwambiri inu pitirirani, zimenezo ndi zabwino mwangwiro.

Koma ilo likuti apa, “Kodi ife tingamavale kapena kuvula tsitsi lathu pamene ife tikupemphera kapena kunenera? Kodi izi makamaka zikutanthauza chiani?”

<sup>212</sup> Chabwino, werengani, M’bale Neville . . . zinali 4—4 mpaka 6, chabwino, chabwino.

*Munthu aliyense akamapemphera kapena kunenera, . . . mutu wake utaphimbidwa, amanyozetsa mutu wake.* (Izo ndizo, ngati iye ali ndi tsitsi lalitali. Chabwino.)

*Koma mkazi aliyense amene amapemphera kapena kunenera ali ndi mutu wosaphimbidwa amanyozetsa mutu wake: . . . (Ameneyo ndiye mwamuna wake.) . . . pakuti zimenezo ziri ngakhale zonse monga wina ngati iye akanakhala wometedwa.*

*Pakuti ngati mkazi akhala ali wosaphimbidwa, msiyeni iye aponso kuti ametedwe: . . . (Ngati iye akufuna kuti adule tsitsi lake, mumpangitse iye alimete ilo mpala. Mukuona? Ngati iye sangati akhale nalo . . .) . . . koma ngati icho chisali chamanyazi kuti mkazi akhale—zikhala zamanyazi kuti mkazi akhale atamededwa kapena kusengedwa, musiyeni azikhala ataphimbidwa.*

<sup>213</sup> Ine sindikuwona kalikonse ka kuvala kapena kuvula tsitsi pamenepo, kupatula ngati mkazi akufuna . . . Iye akuti, ngati iye anena kuti iye akuyenera kuti alidule ilo, ndiye musiyeni iye alimete ilo lonse mpala. Mukuona? Chifukwa ngati iye satero, musiyeni iye azikhala nalo tsitsi lakelo; chifukwa tsitsi lake ndilo chophimba chake. Koma kuti mwamuna kukhala ali ndi mutu wake utaphimbidwa, tsitsi lalitali ngati mkazi, nkumaima pa nsanja, iye angamawoneke ngati mkazi pamenepo. Mukuona? Kotero iye asamakhale nalo ilo monga choncho. Mukuona?

<sup>214</sup> Ndizo—izo zikutanthauza kuti iwo avala kapena avula tsitsi . . . Ine ndikuganiza kuti munthuyo ayenera kuti analakwitsa pa kuganiza pamenepo kuti amatanthauza m—mwamuna kumanenera ali ndi mutu wake utaphimbidwa, ndiye nkuchotsa chophimba chachecho apo. Mukuona? Ayi. Izo sindizo

kuti iye anali ndi tsitsi lalitali, izo zikutanthauza, ngati iye ali wophimbidwa. . . Tsopano, inu werengani mopitirira mmusi patsogolo pang’ono chabe, inu amene munafunsa funsolo, ndipo inu mupeza kuti mutu wa mkaziyo ndi mwamuna wake. Ndi angati akudziwa zimenezo? Ndipo mutu wa mwamuna ndiye Khristu, chotero, mwamuna azimeta tsitsi lake chifukwa cha Khristu, pakuti mwa Iye muli zonse mwamuna, mkazi, ndi zonse. Iye ali zonse tate, mayi, mlongo, m’bale, zonse. Koma mwa mwamuna muli wamphongo yekha. Chotero, iye azilimeta ilo lonse chifukwa cha Khristu; koma mwa mkazi muli chachikazi chokha, kotero iye akhoza kumakhala nalo lake litaphimba; chifukwa mwamuna wake ali pamwamba pa iye. Iye ndi mbuye wake, womulamulira wake; choncho chotero, iye azikhala nalo tsitsi lalitali.

<sup>215</sup> Ndiyeno ngati iye anena kuti iye ayenera, iye ndi woti azilidula ilo, ndiye msiyeni iye azikhala atalipalamo ilo. Ndipo anati, ngati chiri chamanyazi kapena chochotsa ulemu kwa mkazi, amene akuyenera kuti aziwoneka wokongola, ndipo kukhala nalo tsitsi lake lonse litametedwa, ndiye musiyeni iye akhale nacho chophimba chake pa mutu wake; musiyeni iye azikhala nalo tsitsi lalitali. Mukuona? Chotero ndizo. . . Aliyense. . . Zonsezi zikufotokoza icho? Ine ndikutanthauza, kodi izo zikumveka bwino? Nenani, “Ameni!” ngati izo zikutero, ngati inu mwazimvetsa izo. Mukuona? [Osonkhana ayankha, “Ameni!”—Mkonzi.] Chabwino.

**352. M’bale Branham** (Ife tatsala nao maminiti khumi okha tsopano.)—**M’bale Branham, ife tiribe mlaliki kumene ife timakhala, koma ife timakhala ndi utumiki wa tepi Lamlungu usiku wokha. Kodi ife tiziwatengera ana athu ku mpingo wina kukakhala nayo Sande sukulu? Kodi mautumiki a tepi ali okwanira?**

<sup>216</sup> Chabwino, lolani izo zikhale molingana ndi momwe ana anu akupitira. Mukuona? Tsopano, ngati inu muwatenga ana anu, iwo ali aang’ono; ndipo inu mukawatengera iwo mu mtundu wina wa gulu kunjira uko, amene ati angokhomerera zinthu mkati mwawo zimene iwo—zimene i—iwo sayenera kuzidziwa; ine sindikanati ndichite zimenezo. Ngati iwo—ngati iwo akuwoneka kuti akuphuzira mokwanira kuchokera pa matepi ndi zinthu. . . Ndipo inu titi, titi, inu mukukawaika iwo uko mu mpingo wa Katolika, kuwatengera uko mu mpingo wa Katolika, kuwatengera iwo uko ku chinachake chonga izo; ine sindikanati ndikulangizeni zimenezo. Mukuona? Ngati iwo. . .

<sup>217</sup> Koma tsopano, ngati inu muli ndi mpingo wabwino waung’ono kumeneko umene mwina umatsutsana nanu zinthu ziwiri kapena zitatatu, ndipo ana anu akufuna kuti azipita ku Sande sukulu, iwo ndi anthu a Uthenga wathunthu, kapena chinachake, chabwino, zimenezo ndi zabwino mwangwiwo. Koma onani, koma pamene inu mubwera pa malo pamene. . .

Zimatengera momwe ana anu akuzitengera izo. Mukuona? Muziwona zimene ana anu akuchita, zimene, momwe iwo akuchitira kwa izo.

**353. Tiyeni tiwone. Ngati inu mulibe mpingo woti muzipitako, kodi inu muzingomvera matepi?**

Eya! Ndizo...ine ndikanati—ine...Zimenezo zikanakhala zabwino

**354. Kodi ana anu ayenera kukhala ndi chowachitikira kuti akhale nao Mzimu Woyera? Ng—ng—ngati iwo awuwona Uthenga wa nthawi-yotsiriza, kodi iwo ali nao Mzimu Woyera?**

<sup>218</sup> Wina aliyense ayenera kukhala nacho chomuchitikira! Ana anu sangalowemo mwanjira ina yake koma njira yomweyo imene inu mukuchitira. Mukuona? Iwo ayenera kuti abadwe kachiwiri. Mulibe zidzukulumu mu Ufumu wa Mulungu; iwo onse ndi ana. Iwo ayenera kukhala nawo, ayenera akhale nacho chowachitikira ndi Mulungu kuti alowemo, mofanana basi monga inu. Tsopano ine ndikuyembekeza ine ndingathe kulitenga ili. Ndilo...

**355. Wonedwa kwambiri: (Tiyeni tiwone.) Zokhudza Lemba la Aefeso 4:11 mpaka 13, kodi ife tonse (Tiyeni tiwone.)—kodi ife tonse timapeza ungwiro wonse wa oyera kupyolera mu matepi, kapena kodi ife tizikhala tiri kuno, kumene mphhatso za Mzimu zikugwira ntchito ndi maudindo osiyanasiyana a mpingo, kuti zithandizire kutipanga ife angwiro? Mitima yathu yakhulupirira Mawu onse a Ambuye.**

<sup>219</sup> Tsopano munthu uyu ndi wochokera ku Oregon. Tsopano, wokondeka wanga...ine ndikukhulupirira ine ndikumudziwa yemwe ali. Mwawona? Ndi...O, inde, ine ndiri, ine ndithudi ndiri. M—mnyamata wanu...Ngati munthuyu ali pano, ine ndikudziwa ndinu...Ngati inu palibe, ilo liyenera kukhala kuti linali Lamlungu latha. Mukuona? Izi mwina zabwera umu kuchokera ku Lamlungu lapita. Koma m—mwana wanu amawuluka motetezera, onani, ziri, ndipo... iye amayang'anira...Iye ali...Ine ndikuganiza iye ndi amene anandiitanira ine uko kuti tipite tikasake mphalapala ndi inu ku Oregon uko, kumene...Ndipo ine ndikuganiza izi ndi zolondola. Tsopano, ine ndikumudziwa munthu uyu mwa malembedwe mwa...ndipo chotero...

Ayi! Iwo akufuna kuti azibwera kuno ku mpingo kuti akhale angwiro. Mukuona? Kutu i—ife timapeza chiyanjano wina ndi mzake kuno ku mpingo, koma ungwiro umabwera mwa pakati pa ife ndi Mulungu. Magazi a Khristu ndi amene amatipanga ife angwiro mwa Mzimu Woyera.

<sup>220</sup> Tsopano, mu mpingo akuti, "...muli mphatso zikugwira ntchito." Tsopano, ife tiribe mphatso zochuluka kwambiri zikugwira ntchito pano, koma ife tiri nazo zina za izo. Ife tiri

nazo mphatso za malirime, n—ndi mphatso ya kulosera (ziwiri kapena zitatu za izo).

<sup>221</sup> Ine ndikuganiza M'bale wathu Higginbotham pano, kulikonse kumene iye ali, iye ali nayo mphatso ya kuyankhula mu malirime. Ndipo ife tiri naye M'bale wathu Junior Jackson limodzi nafe, ndipo iye amayankhula ndi malirime. Ndiyeno ife tiri nawo awiri kapena atatu a iwo amamasulira. M'bale Neville pano nayenso, m'busa wathu, amayankhula ndi malirime ndipo nthawizina kulosera, ndipo Ambuye amabweretsa pa iye. . .

<sup>222</sup> Kungoti tsiku lina iye ananena chinachake. Iye anaitana pa foni mu nyumba kumene ine ndinali, kuti iye analosera pa munthu, anawauza iwo kuti munthu woledzera akanati—pakanati pakhale kusintha kwakukuru mwa iye nthawi yomweyo kapena chinthu chinachake chotero. Ndipo bamboyo wabwera kuchokera kwa Othandizira Zidakhwa, akadali chidakhwabe, ndipo kwa masiku sikisite-eyiti sanakhudze nkomwe mowa, kapena popanda mankhwala a izo, kapena chirichonse. Ameneyo anali M'bale Neville kunenera pa iwo.

<sup>223</sup> Kotero ife tiri. . . Ife tiri nazo zina mwa mphatsozo zikugwira ntchito pakati pathu, ndipo ife tikhala okondwa kwambiri kuchita chiyanjano ndi aliyense wa inu, amene ali nayo njira, imene inu mukugwirira ntchito, kapena mukufuna kuti mubwere ndi kumadzayanjana ndi ife, chirichonse chimene ife tingathe kuchita, ife ndife okondwa kwambiri pa izo. Mukuona? Koma tsopano kupangidwa wangwiro ndi za kwa Khristu.

Tsopano, tiyeni tiwone, pafupi limodzi lina kapena awiri owonjezerapo.

**356. M'bale Branham, kodi inu mungakhale achifundo mokwanira kuti mulongosole chithunzi chimene chinajambulidwa ndi M'bale Arganbright? Funso loyamba: lachiwiri pa—chithunzi chachiwiri pa khoma, kuwala kokuzungulirani inu, chomangira lamba, ndi zina zotero.**

<sup>224</sup> Chabwino tsopano, ine ndikukuuzani ziripo. Iwo analembo dzina lawo, ndipo iwo sali pano tsopano. Ife tikumvetsa izo. Ndi M'bale ndi Mlongo Jackson ochokera ku South Afrika; iwo abwerera kwao. Chotero ife tikumvetsa zimenezo; ife tinalongosola izo.

**357. Ndi liti pamene mpingo umene. . . Ndi liti pamene mpingo umene unachita. . . ndani (a-n-a-. . .) anafa pa nthawi ya chisautso ndi. . . kuuki-. . . kukhala ataukitsidwa? Kodi iwonso adzayembekezera kufikira chiukitsiro cha opandaumulungu? Kodi iwo adzakhalanso moyo mu nthawi ya Zakachikwi?**

<sup>225</sup> Tsopano, limenelo ndi funso labwino. Likuyenera nthawi yochuluka kuposa yomwe ine ndikhoza kulipatsa ilo, koma kungoti ine ndithe kutenga. . . Mukuona? Ine ndiribe. . . Ine ndatsala ndi mosachepera magawo awiri a atatu a amene



ine ndinayamba nazo mmawa uno, akhala ali maora awiri. Basi ochuluka kwambiri iwe sungathe kufikira kwa iwo. Inu mukuona? Ndipo ine ndikungofuna kuti nditenge ochuluka amene ine ndingathe, kungoti sindikuwona pamene iwo ali. Ine ndikudziwa muli ena abwino kwenikweni mkati umu naonso amene ayenera kuti adziwidwe, monga mbewu ya serpenti kuti ilongosoledwe, ndi zinthu; koma ine ndikuti ndifulumire ndi kulowa mu ili mofulumira kwenikweni.

<sup>226</sup> “Kodi mpingo umene unafa mu nthawi ya chisautso (mukuona?) udzakhala mu chiukitsiro?” Chiukitsiro chachiwiri, chiukitsiro chachiwiri.

<sup>227</sup> “Kodi nawonso adzayembekezera mpaka chiukitsiro cha opandaumulungu?” Olungama ndi osalungama adzaukitsidwa pa nthawi yofanana.

<sup>228</sup> “Kodi iwo adzakhalanso moyo mu nthawi ya Zakachikwi?” Ayi! Ndipo akufa onse sanakhale moyo mpaka kutha kwa zaka chikwi. Tsopano, ilo ndi lalifupi kwambiri, koma ine ndikutsimikiza. . .

**358. Kodi Paulo akutanthauza chiani pamene akuti kumasulidwa ndi ufulu mwa Khristu? Ndi njira yanji imene ili kumasulidwa kwa lamulo?**

<sup>229</sup> Chabwino, inu simuli omangidwa mwa lamulo. Titi, mwa chitsanzo, apa pali chinthu chomwecho; ine ndifotokoza mwa chilengedwe, mwamsanga. Mwa chitsanzo, kunja kuno amanena kuti, muzipita pa msewu, mailosi sate pa ora ndi liwiro lonse limene inu mungamapite nalo. Chabwino tsopano. Tsopano ngati ine ndingamapite chotsika ndi msewu mailosi forte pa ora, ine ndiri wotsutsidwa ndi lamulo. Koma ngati ine ndingamapite chotsika ndi msewu ndiri wotsutsidwa mailosi sate okha pa ora, ine sindiri pansu pa lamulo. Mukuona? Kumeneko ndiko kumasulidwa mwa Khristu (mukuona?), chinthu chomwecho

<sup>230</sup> Sindinu omangidwa mwa lamulo utali wonse. . . Ngati ine sindimaba, kunama, kusuta, kuchita chigololo, chirichonse cha zinthu zimenezo apo, ine sindiri womangidwa mwa lamulo ayi. Mukuona? Ine ndine womasulidwa kwa lamulo; ine ndiri mwa Khristu.

**359. Kodi inu mumamverera bwanji za kuchepetsa kubala?**

<sup>231</sup> Ine ndinali nazo zina za izo pa zokambirana mmawa uwu. Ine kulibwino ndiyankhule nanu mwa nokha—ndi inu pa zinthu zimenezo (mukuona?), pa zinthu zimenezo apo, chifukwa pali mawu ndi zinthu zimene ine ndiyenera kuzinena, zimene ine. . . Ine kulibwino ndizinene izo ngati mwamuna ndi mkazake. . .

<sup>232</sup> Ndipo pali kuthekera kwa izo kukhala zikuchitidwa mu njira yolondola. Ine ndikhoza kuzinenanso izo mwawamba. Alipo masiku ochuluka kwambiri mu moyo wa mkazi pamene

iyе samakhala wachonde. Inu mukumvetsa? Chabwino. Chifukwa. . .

<sup>233</sup> Tsopano, pali nthawizina m—mwana akanati amuphe mkazi; ngati iye akanati akhale ndi mwana akanati amuphe iye. Inu mukufuna kuti musamalitsa zimenezo aponso. Mukuona? Chotero ingokhalani osamalira kwenikweni za izo. Mukuona? Onani, uko ndi kubweretsa moyo, chotero ndi zimene inu munaikidwira pansi pano kuti muzichita.

<sup>234</sup> Ngati mkazi wanu ali wodwalika, ndipo wina, mwana, angati amuphe iye, i—i—ine sindingati ndichite zimenezi. Ine sindikuganiza kuti Ambuye akufuna kuti inu muchite zimenezo. Ndipo i—inu mubwere kwa ine panokha pa zinthu zimenezo; tikakhale nazo izo pa zokambirana zapadera. Mundirole ine ndiyankhule nanu panokha (inu mukuona?) ndipo ine ndingathe kumverera. . .

<sup>235</sup> Onani, aliyense payekha, ine ndikhoza kudziwa ngati iwo akunama kwa ine kapena ayi. Mukuona? Iwo amandiiza ine zinthu zosiyana. Ine ndikadakonda kukuwonani inu basi. . . Mukuona? Chifukwa iwe ukaziyyika izo poyera ngati chonchi, iwe sumadziwa. Ndi chifukwa apo ali payekha ndi zinthu monga izo; ine ndikhoza kuzidziwa izo, ngati iwo akunena zoono kapena ayi. Mukuona?

**360. Chifukwa ch—chifukwa chiani Satana ati adzamasulidwe kanyengo kakang’ono zitatha zaka chikwi za Chivumbulutso 20 ndi 3, ndi Chivumbulutso 20:27?**

<sup>236</sup> Chifukwa chiani iye ati adzamasulidwe? Ndi kuti apite akasonkhanitse anthu ake pa chiukitsiro chachiwiri, chifukwa Satana ayenera kuti alandire chi—chiweruzo nayenso. Mukuona? Iye ayenera kuti atsutsidwe.

O mai, ili ndi—bukhu lodzaza ndi izo. Ine sindikukhulupirira. . .Ndipo apa palonso kalata yodzaza ndi izo. Ndiroleni ine nditenge ena kwenikweni, kwenikweni, mofulumira apa tsopano.

**361. M’bale Branham, chonde longosolani Machitidwe 9 ndime 7 ndi Machitidwe 20—Machitidwe ndime ya 22. (Kodi inu mungandipezere pamenepo ine, M’bale Neville.) Chonde longosolani Machitidwe 9 ndime 7.**

<sup>237</sup> Tsopano, pamene iye akupapeza pamenepo, ine ndiwone ngati ine ndingathe kutenga linalake mofulumira kumene. Kodi inu mwayamba? Ine ndikudziwa inu muli.

**Chonde longosolani chinsinsi cha kusinthika kwa Mkwatibwi. Momwe izo ziti zidzachitikire ndiponso kuti, malo, akupitako Mkwatibwi.** Kodi amenewo si mafunso okondeka? Awo ndi abwino kwenikweni. Ine ndingatati ndingoima pano tsiku lonse. . .

[M'bale Branham ayankha funso 361—Mkonzi.] Miniti yokha tsopano, nd—ndime...Machitidwe 9 ndime 7 (zikomo inu, M'bale Neville)—9 ndime 7:

*Ndipo anthu amene ankayenda naye anaima mwakakasi, pakumva liwu, ndi kusamuwona munthu.*

<sup>238</sup> Tsopano, ine ndikudziwa pamene inu mukupita. Mukuona? Tsopano, malo otsatira ananena kuti iwo...mosephanitsa. Tsopano, i—ine sindikudziwa zimene zinachitika pamenepo. Ine basi sindingathe kukuuzani inu, chifukwa malo otsatirawo iwo anamva. Ena, iwo sanaziwone izo, ndipo malo otsatirawo, iwo anaziwona izo ndipo sanazimve izo. Ndi angati amene anayamba aziwona kale izo mu Baibulo? Ine ndinatero, ndipo ine sindingathe kuzifotozoza izo. Mukuona? I...Ambuye adzasowa kuti awululire izo kwa ine. I—ine ndinakuuzani inu kanthawi kapitako, ine ndiyenera kukhala woonamtima ndi inu. Mukuona? Ine sindikudziwa. Ine ndikupepesa. Ngati i—ngati ine sindingathe kufotozoza izo, ine ndikhala woonamtima mokwanira kuti ndikuuzeni inu ine sindingathe. Koma i—ine sindizigunda izo p—pamene ine sindiri kuzidziwa izo.

<sup>239</sup> Ine sindingathe kulongosola zimenezo, pakuti malo amodzi anati iwo anakuwona Kuwala ndipo sanalimve Liwu, kapena chinachake chotero; ndipo pa malo otsatira, iwo anawona... analimva Liwulo ndipo sanakuwona Kuwalako. Ine sindingathe kulongosola izo. Mukuona? I—ine sindikudziwa zimene zinachitika, ndipo ine sindidziwa mpaka Ambuye atachiululira icho kwa ine; mosachuluka kuposa momwe ine sindikanatha kukuuzani inu za chikwati ndi chilekano. Ine sindinali kudziwa mpaka Iye ataululira izo kwa ine.

<sup>240</sup> Ndipo ngakhale mmawa uno, Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi akudziwa kuti izi ndi zoono, mmawa uno Iye anatsirizitsa chinthu chonsecho, kundiuza ine za chikwati ndi chilekano. Ndiko kulondola. Ndicho chifukwa ine ndikuti, ndiroleni ine ndizitengere izo zonse palimodzi. Ndifufuze...

<sup>241</sup> Pamene chimodzi cha zinthu izo monga mbewu ya serpenti, pamene icho chinaperekedwa kwa ine, i—ine sindinkatha kuchiwona icho, palibe; koma ine ndinangopitirira kumachitsatira icho, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa...Ndiye nkuchita kupita kutali komwe kwa wekha, ndiyeno Mzimu Woyera nkuyamba kuzitsewula izo apo. Tsopano, ine ndikufuna winawake ayesere kuzitsutsa izo tsopano. Mukuona? Sangathe kuzichita izo.

### **362. Chonde fotokozani chinsinsi cha kusandulika kwa Mkwatibwi.**

<sup>242</sup> Kusintha basi, mukuona, matupi athu. Tsopano, tiyeni titi *athu*. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza pamene ine ndikunena izo? Ine sindikutanthauza kuti ndikhale wosinjirira.

Ine sindikutanthauza kunena kuti *athu*; ine sindikutanthauza kunena kuti mpingo uno; ine ndikutanthauza kunena kuti wokhulupirira aliyense.

<sup>243</sup> Abrahamu, Iye anali akuyembekezera mwana wolonjezedwa, amene analonjezedwa kwa iye. Ndi kulondola uko? Ndipo Mpingo ukuyembekezera Mwana wolonjezedwa. Mkwatibwi (ndi kulondola uko?), Mkwatibwi akuyembekezera Mwana wolonjezedwa.

<sup>244</sup> Mwana wolonjezedwayo asanabwere kwa Sara ndi Abrahamu, matupi awo anayenera kuti asinthidwe. Ndi kulondola uko?

<sup>245</sup> Iye anali wokalamba kwambiri kuti akhale naye mwana. Iye analibe misempha ya mkaka mu bere lake; bere lake linali litaumamo. Chiberekero chake sichinali chachonde; iye anali wosabala. Iye sakanatha kukhala naye mwana; mtima wake unali wokalamba kwambiri kuti ungapirire nako kuwawa kwa kubala. Kotero chinachitika ndi chiani? Mulungu anamusintha iye kubwerera ku mkazi wamng'ono. Ndipo Iye anamuchitira Abrahamu chinthu chofanana, chifukwa Iye anati thupi lake linali chimodzimidzi ngati wakufa. Mukuona? Ndipo Iye anachita kuwasintha thupi lawo polinga kuti alandire mwana wolonjezedwayo.

<sup>246</sup> Ndipo ife sitingati timulandire Mwana wolonjezedwa uyo kwa ife lero mu matupi awa amene ife tiri kukhalamo; matupi amenewa ali tchimo.

<sup>247</sup> Chikumbumtima choyamba ichi chimaliramulira thupi ili ndi kupenya, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva, ndipo zangotifikitsa ife popiringizika yense; ife timalingalira ndi china chirichonse. Koma thupi latsopano ilo, limene limabwera kuchokera kwa wobadwa kachiwiri uyu (osati chikumbumtima choyamba ichi, ichi chidzachokapo)...Ndi chinachake chamkatico chimene chikukhala moyo. Aliyense akumvetsa zimenezo anene, "Ameni!" [Osonkhana ayankha, "Ameni!"—Mkonzi.]

<sup>248</sup> Si zakunja izi ayi za kupenya, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva. Si zimenezo. Izo ndi zakuti zife ndipo zidzafa, koma gawo lamkati la inu, pansu mkati umu, mkatimo, ameneyo ndiye munthu amene sangathe kufa. Mukuona? Ndipo ameneyo ndi munthu amene moyo watsopanowo umayambirapo, kuchokera pa kubadwa kwatsopano uku; ndipo iko kumawumba munthu wina mu chifano cha munthu uyu yemwe inu muli, kuzungulira pa moyo umenewo. Inu mukuzimvetsa izo?

<sup>249</sup> Kotero mwakungoyankhula izo ziri mkati umu, ndipo kodi ndi chiani icho? Mawu olonjezedwa asanakhazikitsidwe maziko a dziko. Ndipo kuzungulira pamenepo, ili limangonyezimiritsa chithunzi chosatsuka; ilo linyezimiritsa chenichenicho, Mawu. Mukuona? Ndipo chinthu chomwecho chiri...Kapena,

kusinthika kwa Mkwatibwi kukhala kuli chinthu chomwecho. Mawu amene ali mwa inu, thupi lidzawonekera pozungulira Mawu amenewo, ndipo chinthu chomwecho chinachitika ndi Sara.

<sup>250</sup> Lisanati. . . Pamene thupi lokalamba lija limene iye anali nalo, thupi loyamba lija, ilo linkayenera kuti lisinthidwe polinga kuti libale mwana. Inu mukuzimvetsa zimenezo? Thupi lijali silikanatha kuchita izo. Thupi ili silingathe kuchita zimenezo, kotero ilo liyenera kuti lisinthidwe mwanjira yomweyo kuti limulandire Mwana.

**363. Kodi zidzachitika motani, ndipo ndi liti. . . ndi kuti. . . ndi kuti kumene Mkwatibwi akupita?**

<sup>251</sup> Iye akupita ku Ulemerero, Kumwamba kukakhala ndi Mgonero wa Chikwati, moimira basi monga Isaki ndi Rabeka, pamene Rabeka anapita kuti akakomane ndi Isaki. Kumbukirani Eliezara, kuimila tsopano uthenga umene unapita uko kuchokera kwa Abrahamu, Eliezara anapita uko kuti akampeze mkwatibwi kwa Khri- . . . kwa Isaki. Iye anamupeza Rabeka wokongola mu kachisisira ka madzulo, msungwana wamng'ono wa khungu loderapo, kubwera uko atasenza mtsuko wa madzi. Ndipo Eliezara anali atapemphera, anati, “Ambuye Mulungu, ndipatseni ine ulendo wabwino tsopano ndi kupambana kwa mbuye wanga, Abrahamu.”

<sup>252</sup> Ndipo iye anati, “Pita, usati umutenge iye pakati pa Afilisiti; usati umutenge iye.” Pita mpaka uku pakati pa anthu ake, kusonyezera kuti Mkwatibwi wa Khristu ndi Khristu ali pa chibale chamagazi, chifukwa Rabeka n—ndi Isaki anali asuweni.

<sup>253</sup> Ndipo chotero iwo anapita uko, ndipo Rabeka wokongola uyu anatulukira ndipo anatunga madzi; ndipo iye anapemphera; ndipo anaimwetsa ngamira ndi zina zirizonse. Ndiyeno, inu muzindikira kuti Rabeka anali. . . Kusankha kotsiriza kunayenera kubwera kwa Rabeka. Iye anawafunsa abambo ake pofuna msungwanayo; iye anawafunsa amake pofuna msungwanayo; ndipo iwo palibe mmodzi akanatha kuvomereza. Ankafuna kuti iye akhalabe kwa kanthawi. Iye anati, “Musati munditchinge ine pa ntchito yanga.”

<sup>254</sup> Ndipo Rabeka anayenera kuti apange kusankha, chifukwa iye anati, “Iye ndiye buthulo; musiyeni iye apange chisankho.”

<sup>255</sup> Ndipo mwamsanga pamene izo zinapangidwira kwa iye, mwamsanga anapanga lingaliro; iye anati, “Ine ndipita.” Ndipo iye anakwera pa ngamila ndipo anapita kuti akakomane. . . Taonani, ngamila yomweyo imene iye anaipatsa madzi inali ngamila imene inamutengera iye kupita kwa mkwati wake ndi kupambana kwake konse. Ndipo ngamila yomweyo, mphamvu yomweyo ya (chirombo chija mu Baibulo chinkaimira mphamvu). . . Ndipo Mphamvu yomweyo imene ife tikuipatsa madzi ndi mayamiko kwa iyo (Ameni! Mukuona?), madzi,

moyo, ulemerero kwa, Mawu, ndi chinthu chomwecho chimene chikutitengera ife kupita ku Dziko laulemerero kuti tikakomane naye Mkwati. Inde, bwana! Ameni!

Kuyang'anira kudza kwa tsiku la Zakachikwi;  
Pamene Ambuye athu odala ati adzabwere,  
kudzamutengera Mkwatibwi wake kutali.

<sup>256</sup> Ndipo kumbukirani, Isaki anali atachoka mu hema ndipo anali ataima panja mmunda akusinkhasinkha pa madzulo ochedwa. (Ameni!) Pamene iye anamuwona Rabeka akubwera... Ndipo iye anali asanamuwonapo iye ndipo iye anali asanamuwonapo mkaziyo, koma icho chinali chikondi pa kuwonana koyamba. Iye anagwera mchikondi naye iyeyo ndipo mwamunayo ndi mkaziyo, ndipo iye anali anali ataphimbidwa. Ameni! O, mai!

<sup>257</sup> Ndipo taonani, pamene iye anamuwona iye, mtima wake unali utadzaza kwambiri ndi chimwemwe. Iye sanali kudziwa yemwe amati akakwatiwe naye, koma mwa chikhulupiriro. Ameni! Nd—nd—ndipo kumbukirani, Yesu adzausiya Ufumu, ndipo ife sitidzakakomana naye Iye mu Ulemerero, ife ndife oti tikomane naye Iye mu mlengalenga, pakati pa miyamba ndi dziko lapansi, kumene kwatambasulidwa kuti atiwohole ife. Ndipo iye anakomana naye Rabeka pakati, pakati pa kwawo kwa mkaziyo ndi kwawo kwa iye. Ameni! Anamutengera iye kunyumba kwawo, ndipo anakamukwatira iye, ndipo anakhala wolandira kwa chirichonse chimene bambo ake anali nacho. Ameni! O, zangwiwo, zangwiwo basi. Chabwino.

**Funso: Kodi Mulungu amalekanitsa mwamuna ndi mkazake mu . . .**

<sup>258</sup> I—ine kuli bwino ndisaliwerenge ili. Onani, mukuona? Nd—ndizo . . .mwina ndingonena apo mawu. Inu mukuona? Ine ndikukudziwani inu nonse, koma i—i—izi zikujambulidwa (inu mukuona?), kotero i—ine kulibwino ndisatero. Ndi chinachake chokhudza . . .Munthu amene analemba izi, inu mukudziwa chimene izo ziri; ndipo i—ine kulibwino ndidzakuwoneni inu pa zoyankhulana zapadera. Mukuona? Ine kulibwino ndisatero . . . Ine sindikuganiza kuti zingakhale zabwino kwenikweni kuti ndiziwerenge zimenezo. Mukuona? Ziri—zonse nzabwino, munthuyo, palibe kanthu kolakwika ndi zimenezo; iwo anafunsa funso lovomerezeka, koma i—ine ndikuganiza izo zingakhale bwinoko kuti ndidzaziwone izo pa zoyankhulana zapadera. Kodi inu simukuganiza chomwecho? Basi aliyense yemwe . . . Inu mukudziwa yemwe uyo ali, aliyense yemwe inu muli.

<sup>259</sup> O, mai! O, ife tadutsa kale nthawi yathu, anthu. I—ife kulibwino kuti titseke ndi ku—kupita ku chakudya chathu. Kodi ndi nthawi yochuluka bwanji imene inu mukufuna ine kuti ndipitirize chokupiza pano? . . .chokupiza apa? [Winawake ati, “Utali wa tsiku lonse.”—Mkonzi.] O, mai, mai! Basi—

basi . . . Eya, basi . . . Mwinamwake pang'ono pokha. Ngati yense yemwe akuyenera kumapita mofulumira kumene, musati musiyere chakudya chanu chipsyerere. Koma ngati i—ngati inu . . . N—ndipo ine mwinamwake ndikakhala ndikudya uko ku Blue Boar, kapena kwa Pryor, kapena ena a malo amenewo, ndipo iwo mwina sakakuvutitsani inu. Ngati inu mungati muzipita, Mulungu akudalitseni inu; ine ndikumvetsa. Mukuona? Ndipo ine ndingotenga pafupi . . . Ine ndikuti ndiziyale izi apa pomwe, ndipo ndizo zonse zimene ine nditi ndiziyankhe. Ndiye ndi—ine ndikuti ndi . . . izi moyenera . . . Izo zikhala pafupi . . . titenga pafupi maminiti fifitini ena owonjezera, ndiye ine ndikuti ndipiteko, kuti ndichokepo.

**364. Ine ndiri ndi ana aakazi awiri okwatiwa kwa mwamuna mu d-e-a-v- . . . ndipo iwo akukhulupirira Uthenga uwu. Iwo . . . zipembedzo, (Ndiko kulondola.), ndipo iwo akukhulupirira Uthenga uwu ndipo iwo atenga maimidwe ofuna Iwo, ndipo analandira . . . Kodi iwo achite chiyani? Iwo akulandira kutsutsidwa. Kodi ife tichite chiani?**

<sup>260</sup> Gwirani maimidwe anu! Mwamtheradi. Onetsani manga anu. Ndi zimenezo; musati mugonjere kwa iwo. Ayi, bwana! Ine sindikunena kuti, musati muzipita pakati pawo, chiyanjano, kapena chinachake chonga izo, utali wonse momwe inu mungakhoze kumayanjana nawo; koma pamene iwo abwera pa kusintha zakudya, inu mukudziwa, nkunda siingathe kudya ndi khwangwala.

**365. M'bale Branham, kodi inu chonde mungalongosole Marko 13:27? Ndiponso, M'bale Branham, nanga bwanji anthu a mu Chivumbulutso 20:7 ndi 9, chiyani . . . amene akupanga nkondo motsutsana ndi oyera? Kodi iwo akuchokera kuti? Kodi padzakhala pali kutengedwera kwina monga ndi—banja la Nowa?**

<sup>261</sup> Chivumbulutso 13 kapena . . . Ayi, Marko 13:27, M'bale Neville. Chivumbulutso 20. Inu muli ndi Baibulo lanu pamenepo, M'bale Capps? Chivumbulutso 20, ndipo izo zikuwoneka ngati 7 ndi 9. Ine ndikuganiza ine, pamene iwo akupeza izo . . . Apa, iye wapapeza apo apa pomwe. Chivumbulutso, kodi apo panali chiani tspano? Marko 13:27, 13:27.

*Ndiyeno Iye adzatumiza angelo ake, ndipo . . . adzasonkhanitsa palimodzi osankhidwa ake kuchokera ku mphepo zina, ndipo adza . . . ndi madera akutali a dziko lapansi kuti adzakhale . . . ndi mpaka kumalekezera a kumwamba . . . madera a kutali a dziko lapansi mpaka ku madera akutali a kumwamba.*

<sup>262</sup> Zimenezo zikukamba za chiukitsiro, kusinthika, kupita mmwamba. Iye adzawatumiza angelo Ake kuti akasonkhanitse. Kodi inu munayamba mwaganizapo chimene angelo ali? Nhu? Atumiki. Iye adzawasonkhanitsa iwo palimodzi,

adzawasonkhanitsa iwo palimodzi (mukuona?), kuwabweretsa iwo, kuwamanga iwo palimodzi kuchokera kumadera akutali a dziko lapansi mpaka ku kumadera akutali a Kumwamba, Mawu amene anali, kukhala akuwonetseredwa padziko lapansi. Mukuona? Mukumvetsa zimenezo? Mawu ayankhulidwa kale; apa Iwo ali kuwonetseredwa. Mukuona? Chabwino, M'bale Capps. Tiyeni tiwone.

*Ndipo pamene zaka chikwi zinatha, Satana anali...  
atamasulidwa kuchokera ku ndende yake,*

263 Chabwino. Ine ndatsiriza kumene kufotokoza zimenezi, sichoncho ine, momwe iye ati adzamasulidwire kuchokera ku ndende yake pa mathero a zaka chikwi?

Chabwino, ine ndiri nalo lina pomwe pano. Miniti yokha.

**366. M'bale Branham, kodi izo zinali za Mulungu, kapena izo zinali za kupanga kwanga kwanga pamene zinthu zimene zinachitika, pamene (k-u-...) kuyesedwa... Zinali izo...** (Onani ngati inu mungathe kuwerenga izo. Ndi zolemba zabwino, koma maphunziro anga ndi osauka. Kodi akuti chiyani pamenepo? [M'bale Branham ayankhula kwa M'bale Neville—Mkonzi.] I—ine sindikukhulupirira kuti ine ndingathe kuziyankha zimenezo. M'bale Capps kapena ine sitingathe kuziwerenga... Anati,) **Kodi izo zinali...** (Kupatula i—izo zinali...ngati uyo anali namwino. Chinachake cha unamwino.) **Kodi izo zinali za Mulungu pamene ine ndinasiya unamwino, kapena uko kunali kulakwitsa kwanga?**

264 Ine sindikanati ndidziwe. Ine bola ndikaziwone zimenezo pa kukambirana kwapadera. Mukuona?

Tsopano, unamwino ndi chinthu chovomerezeka, basi monga namwino. Ine ndikanati...Tsopano, munthuyu sanati... Ine sindinaponyere zimenezo mmbuyo kuti ndingonena kuti sindiziyankha zimenezo, chifukwa zimenezo zikutanthauza mochuluka basi kwa mkazi ameneyo basi monga funso lanu likutanthauzira kwa inu kapena langa kwa ine. Mukuona? Koma tsopano, ngati ndizo—ngati izo ziri—namwino, kuti inu munangosiya kuchita unamwino chifukwa inu munkaganiza kuti inu musamagwire ntchito...Chabwino, ine ndikuganiza unamwino uyenera kumakhala mochuluka ngati zachifundo. Mukuona? Inu muziganiza za kuchita chinthu chinachake, monga dokotala.

265 Dokotala amene ali dokotala wabwino, ife tingamuthandize munthu mosalabadira kuti iye ali ndi chidutswa cha ndalama kapena ayi, dokotala weniweni. Mukuona? Ndipo ine ndikuganiza mtumiki, aliyense, kutumikira kwathu kuzikhala kwa wina ndi mzake, chifukwa zimapangitsa moyo kukhala wabwinoko pang'ono kwa wina ndi mzake.



266 I... Pamene iwo anandiuza ine kuti ndinkayenera kumatenga madola handiredi pa sabata kuchokera pa mpingo uno ngati malipiro, bwanji, izo zinali nga—ngati kuti zindiphe ine. Tsopano... Akazi a Wilson, ine ndikudziwa, ndipo mwinamwake mwana wawo, ndi iwo amene ali pano, mukukumbukira zaka zapitazo, ine ndinkalalikira pano kwa zaka seventini ndipo sindinkatenga konse khobidi mu moyo wanga. Ndalama yaing'ono iliyonse, chirichonse chimene ine ndinkapanga, ine ndinkachiyika icho umo momwe. Mukuona? Ndipo pamene iwo anandiuza ine kuti ndinkayenera kumazitenga izo npolinga kuti ndizikhala mu misonkhano iyi, izo zinkakhala ngati kuti zindiwononge ine. Mukuona? Ndithudi, ine ndikukhulupirira nzabwino, koma kwa ine ndekha (inu mukuona?), ine sindikufuna kalikonse, ndalama ayi, chinthu chokha chimene ine ndikuchifuna n—ndi wanu—ubwenzi wanu ndi kukondera kwa Mulungu kuli nafe.

267 I—ine ndimakukondani inu (mukuona?), ine ndimakukondani inu, ndipo ine ndikufuna kuti inu mukhale owona; ndipo ine ndikufuna ndikhale wona mwiniwanga. Ndipo i—ine ndikufuna kuti inu muzindikhulupirira ine; ine ndimakukhulupirirani inu. Ndipo ngati inu mubwera ndi ine ku funso, ine ndikufuna kuti ndikhale woonamtima ndi inu. Ndipo ngati i—ine ndikuuzani inu mu Dzina la Ambuye, ine ndikufuna kuti inu muzichita basi chimodzimodzi zimene ine ndinakuuzani inu. Musati muzisiyana kwa izo—npang'ono, ndiye ine ndikuganiza ife tizipitirira nazo bwino monga choncho. Mukuona? Ndiyeno, ena...

268 Ndipo chotero tsopano, ngati uli unamwino... Ndipo ine ndikuganiza ngati inu, mu mtima mwanu kuti mukhale namwino... Aliyense sangathe kukhala namwino. Namwino ndi winawake amene ali woleza mtima ndi wachifundo kwa anthu, ndipo o, ine ndikuganiza namwino weniweni... Ngati inu munayamba mwadwalapo mu chipatala, kapena chinachake, kumukuona namwino weniweni wabwino akubwera ndi kudzakupangitsa iwe kumverera bwino, kapena chinachake kapena chimzake...

269 Ine ndinali nayo opareshoni pamene ine ndinawomberedwa nthawi ijayi; ine ndinayenera kuti ndipite ku chipatala. Anali ndi namwino wachikulire wamng'ono kumeneko, ine ndinkamutcha iye “Nkhaka zokoma,” chifukwa kuti iye nthawizonse ankakhala ndi nkhaka mkamwa mwake, akudya iyo. Izo zinali nthawizonse monga choncho. Ndipo ine ndinali pafupi usinkhu wa zaka fortini zokha, ndipo ine ndinali nditawomberedwa. Ndipo iye anali chabe pafupifupi munthu wamng'ono mulimonse, ndipo iye ankatha... miyendo yowombeledwa iyo, pafupifupi yonse iyo itaphulitsidwa monga choncho, ndipo iye ankakhoza kuika chotsamira apa ndi chotsamira apo; ndipo nthawi zonse iye anali nthawizonse

akundithandiza ine. Ndipo ine nthawizonse ndinkaganiza (ine ndinali ndiri kamwana kakang'ono)—ine ndinkaganiza kuti ine ndikanakhoza kumukwatira iye, chifukwa iye anali—iye anali wachifundo kwambiri ndi wabwino kwa ine. Chabwino i... Izo... Inu mukuona, izo zimatanthauza chinachake (mukuona?) kumachita chinachake.

**367. Ine ndikufuna kuti ndifunse funso. Loyambirira lake: Kodi zovala zapogona za mkazi...** (Tsopano, tadikirani miniti yokha; ndiroleni ine ndiliwerenge ilo. [M'bale Branham awerenga funso kwa iyeyekha—Mkonzi.] Ayi, izi zikhala zabwino bwino.) **Kodi zovala zapogona za mkazi ndi zoyenera ku zovala zaamuna?**

<sup>270</sup> Anyamata, inu musandiuze ine kuti iwo sangakufunse iwe zina zokuwotcha. Ine sindikudziwa. Ine ndikuti ndingokusiyani inu kuti muchite kulingalira kwa zimenezo. Inu musamati muziyendayenda pamaso pa anthu mutavala izo; i—ine ndikudziwa zimenezo. Chotero mwanjira imeneyo izo zingakhale ziri, koma mu... pa kupita kokagona i—i—ine sindiri kudziwa. Ine ndikuti ndibwerere mmbuyo pa limenelo nalonso.

Ine ndinakuuzani inu kuti ine ndikhala woonamtima ngati ine sindiri kudziwa. Ine sindikapo maganizo anga pa za zimenezo (chabwino), kupatula ngati inu mukufuna maganizo anga anga. Ngati inu mukufuna zimenezo, ine ndikuuzani inu. Mwawona?

Tsopano kumbukirani, si zimenezo ayi...i—izi...Izi—zikhocha kukhala zolakwika mailosi milioni. Ine ndikuganiza izo zikanati zioneke bwino kukhala utavala mkanjo wausiku. K—koma ngati inu—koma ngati inu... Koma zimenezo ziri kwa inu. Tsopano, ine sindi—ine sindingati ndikuuzeni inu zimenezo, chifukwa ine sindikanati ndipeze choimira kumbuyo zimenezo. Tsopano, a—a—ameneyo ndi ine, osati Iye, kumbukirani. Mukuona?

**368. Kodi ndi kulakwa kudula nsonga za tsitsi la mkazi?**

Ine ndikukhulupirira ife tadutsa kale mu zimenezo maminiti angapo apitawo (mukuona?), kwa laling'ono... Ine ndikupenekera iwo amazitcha izo—zinthu zazing'ono izo zimene zimallengedwera monga choncho...

**369. M'bale Branham, imodzi ya matepi a Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo inu munanena kuti Yudasi anali atalungamitsidwa, atayeretsedwa. Kodi izi zinali zenizeni...** (Apa pali labwino lake)... **talongosolani... chomuchitikira, zomuchitikira zenizeni za chisomo zimene iye anazilandira? Inu munanenanso kuti Yudasi anali nalo dzina lake pa Bukhu la Moyo, ndipo komabe, ife tikudziwa kuti iye anapita ku hade ndipo anataika. Zingatheke bwanji munthu kukhala nalo dzina lawo pa Bukhu la Moyo ndipo apobe nkutaika? Kapena nchifukwa chiani**

**Mulungu amaika maina pa Bukhu la Moyo pamene Iye akudziwa kuti iwo adzataika pa mathero?**

271 Tsopano, limenelo ndi labwino, si choncho? Tsopano, ili likanakhala labwino. Tsopano, ine ndingodalira pa Ambuye kuti ndiyankhe ili, chifukwa ine ndikungopondaponda, kusanthulasanthula, maka. Yang'anani! Choyamba, mu... mipingo yathu, ine ndinanena kuti Yudasani anali nalo dzina lake pa Bukhu la Moyo. Zimenezo ndi zooni. Iye tikudziwa zimenezo, chifukwa Yesu anawauza iwo pamene onse a iwo anatumidwa kunja (Mateyu 10), kuti akatulutse ziwanda, kuti akalalikire Uthenga, ataulandira mwaulere, akaupereke mwaulere; ndipo iwo anabwererako akusangalala, chifukwa ziwanda zinali kuwamvera iwo. Ndi kulondola uko? Ndipo Yesu anawauza iwo, ndipo Iye anatchula maina awo (amene iwo anali, chiwerengero cha amene anatumidwa kunja); ndipo iwo anabwererako ndipo Yudasani Iskaroti amene ndiyenso anamupereka Iye... Mukuona? Iwo anabwererako akusangalala, chifukwa ziwanda zinali kuwamvera iwo. Tsopano, onani, katengedwe ka zinthu kanali kolakwika pamenepo. Mukuona? Inu musamati muzisangalala chifukwa ine ndiri nayo mphamvu yopangitsa chiwanda kuchoka. Mukuona? Inu musati muzichita zimenezo, inu muzisangalala chifukwa munalandira ngakhalenso chisomo chokwanira kuti munapululumutsidwa. Onani, mukuona? Inu musati muzisangalala... Umo ndi momwe anthu...

272 Kawirikawiri anthu amene ali nazo mphantho ndi anthu amene samazifuna mphantho. Mukuona? Paulo ankayesera kuti athawe kwa chinthucho, momwe anachitiranso Mose. Atsogoleri aakulu monga amenewo amayesera kuti athawe ku ntchitoyo; iwo amadziwa zimene ziri patsogolo pawo. Mulungu...

Onani, ngati inu mumutenga munthu amene nthawizonse, “O, Ambuye, ndidzazeni ine ndi mphamvu, ndipo ine ndipita kunja uko, ndipo ine ndikazitulutsa ziwanda.” Iye sangati akachite konse zimenezo. Mulungu amadziwa bwinoko kuposa kuti amdalire aliyense wonga ameneyo. Mukuona? Iye sakanati achite konse zimenezo.

273 Ndi munthu uyo amene samafuna kanthu kochita nazo izo. Inu mukuona? Ameneyo ndi munthu amene Mulungu angamutenge iye ndi kumuphunzitsa iye chinachake nthawiina. Inu mukuona?

Chotero ndiye, Yudasani anabwererako akusangalala, onse a iwo, kuti maina... Iye anati, “Musati muzisangalala chifukwa ziwanda ziri kukumverani inu, koma zisangalalani chifukwa maina anu analembedwa mu... pa Bukhu la Moyo.” Tsopano, ngati inu mutazindikira ndi kutenga Daniele nayenso. Bi... Mukuona?

Chifukwa dzina lanu liri pa Bukhu la Moyo (chifukwa ilo liri Kumwamba, dzina lanu lakhala litazindikiridwa), izo

apabe sizikutanthauza kuti inu muli opulumutsidwa. Mukuona? Inu simuli otembenezidwa, mpakana inu mutalandira Mzimu Woyera. Kumbukirani zimenezo. Inu muli kokha otembenuka mwakungoyankhula. Mukuona? Inu simuli. . .

<sup>274</sup> Ng-ngati inu mundipempha ine p-pofuna mtengo wa thundu ndipo ine nkukupatsani inu chipatso chake, mwakuyankhula inu muli nao mtengo wa thundu, mwakungoyankhula, koma iwo sunayambe kumera apobe. Ndi chifukwa chake ine ndimakhulupirira mu chitetezero monga momwe ine ndimachitiramu.

Ngati i-ngati ine nditafunsa kuona munda wa chimanga, ndipo ine nkuwona chimanga mmwamba pafupi utali chonchi, mwakungoyankhula, ine ndiri ndi munda wa chimanga. Si-icho sichinakhwime apobe, chinachake chikhoza kuchitika. Mukuona?

Tsopano, inu muli ndi njira yanu kudutsa mu kulungamitsidwa ndi kuyeretsedwa kumka ku ubatizo wa Mzimu Woyera. Koma pamene inu mwabatizidwa moona ndi Mzimu Woyera, inu muli mu Ufumu. Tsopano, inu mukuti, “M’bale Branham, kodi izo nzoona?”

<sup>275</sup> Tsopano, ine ndiribe nthawi tsopano k-kuti ndikupatseni inu Lemba; inu mukangoliyang’ana ilo pamene inu mukafika kunyumba, chifukwa ine sindikudziwa. . . malingaliro anga. Ndiyenera ndichite kuyang’ana mmbuyo umu mu konkodanse yanga kuti ndizipeze izo. Yesu anamuuza Petro, amene anali zonse atapulumsidwa ndi kuyeretsedwa. . . Iye ankakhulupirira pa Yesu, anali atayeretsedwa. Yohane Woyera 17:17, Yesu anati, “Ayeretseni iwo, Atate, kupyolera mu Choonadi; Mawu Anu ndiwo Choonadi.” Ndipo Iye ndi Mawu ali chimodzimidzi. Iwo anali atayeretsedwa, mwakungoyankhula, kupyolera mu Choonadi, Mawu, Choonadi. Ndiyeno, Yesu anamuuza Yudasi. . . k-kapena Petro usiku wa kuperekedwa, Iye anati, “Iwe ukadzakhala utatembenuka, ndiye uzidzawalimbikitsa abale ako,” iwe ukadzakhala utatembenuka.

<sup>276</sup> Mwamuna amene uja anali atamutsatira Iye kwa zaka zitatatu ndipo anali nalo dzina pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, ndipo anali atatulutsa ziwanda, ndipo ankachita ntchito zazikulu, ndipo ankachiritisa, ndipo anachita mtundu wonse wa. . . ankalalikira Mawu, ndi chirichonse, ndipo komabe sanali atatembenuka. Mwaona. . . Inu mukulondolera ku kutembenuka. Mukuona?

<sup>277</sup> Mwana amene. . . Pamene kachitidwe kachitika pakati pa-dzira ndi umuna, kapena jini. . . Koma pamene iwo. . . Mwakungoyankhula, mwana ali mmenemo pamene mchitidwewo uli kuchitidwa. Ndiye thupilo limayamba kupangika, gawo lachiwiri; koma mwanayo ayenera kuti abadwe

apa, ndiyeno iye amalandira mpweya wa moyo. Iwo sunakhale apobe mpweya wa moyo. Inu mukuti, “O, iye ali moyo!” Ayi, izo si choncho! Imeneyo ndi misempha yaing’ono ikugwedezeza, akatumba. Mukuona? Mwanayo sanalandire moyo mpaka iye atabadwa. Ndipo inu mukhoza kumadumpha ndi kugwedezeza, koma inu simuna... Onani, mukuona? Inu muyenera kuti mubadwe. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza? Chabwino.

<sup>278</sup> Tsopano, tsopano, iye anati ndiye izo zitatenga... “Inu munanena kuti Yudasani anali ndi dzina lake pa Bukhu la Moyo, ndipo komabe, ife tikudziwa kuti iye anapita ku hade ndipo anakatayika. Zingatheke bwanji ndiye munthu, kukhala nalo dzina lake pa Bukhu la Moyo ndipo apobe nkutaika?” Tsopano, ndiroleni ine ndipereke chinthu china chimodzi chaching’ono mkati umu kwa munthu wokonedwa uyu.

<sup>279</sup> Tsopano zindikirani, Baibulo linati pamene Daniele anawona... I—iye analemba Bukhu loyamba la Chivumbulutso, Daniele. Ndipo ife tikuzindikira, mu masomphenya iye anamuwona Iye akubwera kwa wanthawi Zamakedzana amene tsitsi lake linali loyera ngati ubweya wankhosa. Ndi angati akukumbukira powerenga zimenezo? Ndipo kodi inu munazindikira, Yohane mu Chivumbulutso anabwera kwa chinthu chomwecho, Chivumbulutso 1? Ndipo Iye anaima pamenepo; tsitsi Lake linali loyera ngati ubweya wankhosa, mapazi Ake ndi momwe iwo ankawonekera—wanthawi Yamakedzana. Wanthawi Yamakedzana, ndiko kuti, analibe nthawi; Iye Wamuyayayo. Ndipo Iye anabwera... Tsopano penyani! Ndipo oyera anabwera ku dziko lapansi ndipo mabuku anatsegulidwa, ndi Bukhu lina linatsegulidwa, limene linali Bukhu la Moyo, bukhu limodzi. Iwo anabwera ku chiweruzo, ndipo... Iye anabwera, ndipo limodzi ndi Iye anabwera zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi. Ndi kulondola uko? Ankatumikira kwa Iye, Mkwatibwi, Mfumukazi ndi Mfumu... .

<sup>280</sup> Ndi ndani ali Mfumukazi wanu wamng’ono mnyumbamo? Iye amatumikira chakudya kwa inu. Ndi kulondola uko? (Chimene inu mwachedwa kwa icho tsopano.) Koma pamene iye—pamne iye atumikira kwa inu. Ndizo zimene, Mkwatibwi amatumikira kwa Khristu, Mawu. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma Mawu onse.” Mukuona? Iye amatumikira Mawu kwa Mfumu, kuwonetsera lonjezo Lake la Mawu mu m’badwo umene Iye akukhalamo. Amen! Aha, ine ndinanena chinachake apo, inu simunachimvetse icho, koma... .

<sup>281</sup> Zindikirani! O, mai! Limenelo linali labwino. Mukuona? Kutumikira mu m’badwo, Mawu. Tsopano zindikirani! Ndipo Iye anabwera... Iye anabwera, ndipo zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi anabwera kwa Iye; ndipo chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo Bukhu lina linatsegulidwa limene liri Bukhu la Moyo; ndipo iwo

anaweruzidwa momwemo. Anali ndani uyu amene anabwera? Mkwatibwi amene sankayenera kuti abwere ku chiweruzo, Iye ali mfulu ku chiweruzo.

<sup>282</sup> Bukhu lina linatsegulidwa limene linali Bukhu la Moyo, ndipo iwo amene anali nalo dzina lawo pa Bukhu la Moyo ankayenera kuti aweruzidwe kuchokera mu Bukhu limenelo. Ndipo Yudasi Iskarioti ankadzinenera kuti anali wokhulupirira, ndipo iye anali nalo dzina lake litalembedwa pakati pa iwo pa Bukhu la Moyo. Kodi uko nkulondola? Iye ankadzinenera kuti ali nao Moyo Wamuyaya. Ndipo dzina lake linaikidwa pa Bukhu la Moyo. Kotero iye ayenera kuti... Bwanji, iye ayenera kuti aweruzidwe ndiye kuti awone chifukwa chimene iye anawatsutsira Mawu a Moyo ndiye, kumugulitsa pa mtengo wa zidutswa sate za siliva. Ena amadzigulitsa kuti akhale a Methodisti, Baptisti kapena chinanso chirichonse. Anagulitsa malo ake kudzichotsa mu Bukhu la Moyo. Ndipo iye adzaweruzo... iye adzayenera kuti... aime pamenepo ndi kuweruzidwa nawo amenewo, ndi Mawu. Mukuona? Nchifukwa chake Yudasi anali woti achite zimenezo. Mukuona? Yudasi ayenera kubwera ku chiweruzo. Dzina lake linali pa Bukhu la Moyo, koma izo sizikutanthauza kuti iye ali wopulumutsidwa. Iye ayenera kuti ayime nacho chiweruzo.

<sup>283</sup> Namwali wopusa adzaima apa pomwe pansu pa chomwecho—zinthu zomwezo. Zindikirani, Yesu ananena mu Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva Mawu Anga.” Ameneyo ndi iye amene angathe kuwalandira Iwo; osati iye amene angowamva Iwo akulalikidwa ndi kumapitirira nazo kumati, “Zachabechabe.” Mukuona? “Iye amene alandira Mawu Anga, Iye amene amva Mawu Anga ndi kuwakhulupirira (osati kudzipangitsa kukhulupirira, koma kukhulupirira moonu) pa Iye amene anandituma Ine (amene anali Mawu) *ali nawo* Moyo wosatha ndipo sadzabwera ku chiweruzo; koma wa” (zochitika kale) “wachoka ku imfa nalowa ku Moyo.” Mukuona? Ndi zimenezotu.

<sup>284</sup> Chotero Yudasi anali nalo dzina lake pamenepo pa Bukhu la Moyo (uko ndi ndendende kulondola), koma iye anaweruzidwa, chifukwa kodi iye anachita chiani? Iye anagulitsa maifulu akubadwa ake.

Esau anabadwa mu banja liri ndi lonjezo la Mulungu. Mwana wamwamuna wamkulu anali nao ufulu wakubadwa. Ndi angati akudziwa zimenezo? Mwa lonjezo la Mulungu, dzina la Esau linali pa bukhu lolandira ufulu wakubadwa (ndi kulondola uko?), koma iye anasinthanitsa iwo ndi chipere cha mphoza zakuthengo, kapena nandolo. Wanjala kuti akhutitse mimba yake, chitupa chake chachakudya, iye anasinthanitsa maifulu akubadwa ake pofuna chitupa cha chakudya ndipo sanathe kupeza malo oti alapirepo.

<sup>285</sup> Azondi aja amene anapita nao...uko kuti akalizonde dzikolo, anabwera ndipo ngakhalenso kudya mphesa zimene Yoswa ndi Kalebu anabweretsa pobwerera. Ndipo komabe, kodi iwo anachita chiani? Anagulitsa maufulu akubadwa kwawo.

<sup>286</sup> Yesu anati, kapena Paulo poyankhula ndi kudzoza kwa Khristu mu Ahebri mutu wa 6: “Pakuti ndi kosatheka kwa iwo amene anayamba awunikiridwapo, ndipo anapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera, ndipo analawapo za Mphamvu ya dziko likudzalo; ngati iwo ati adzagwere kwina, kuti adzikonzenso okha kachiwiri mwa kulapa, pakuwona kuti iwo akupachikira kwa iwookha Mwana wa Mulungu, ndi kuwerengera Magazi a pangano, amene iwo anayeretsedwa nawo, chinthu chosayera, ndipo achita chonyazitsa ku ntchito za chisomo...” Ndi kosatheka kwa munthu ameneyo kuti abwerere konse.

<sup>287</sup> Iwo, wina aliyense kupatula Yoswa ndi Kalebu, anafa ndipo anawonongeka mu chipululu chija, komabe iwo anali okhulupirira, komabe maina awo anali pa mabuku.

<sup>288</sup> Ndipo apa, Paulo akuyankhula, ngati munthu afika konse pa malo okuti iye wapulumutsidwa, ndi kuyeretsedwa (Magazi amayeretsa; Ahebri 13:12 ndi 13 amati Magazi amayeretsa), ndiyeno nkubwera mpaka pa chipata cha ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo chifukwa cha kutchuka kapena chipembedzo nkukana kuti ayende mwa Iwo, anati, “Munthu ameneyo wataika ndipo sangati apulumutsidwe konse” (mukuona?); pakuti iye wachita chonyozetsa ngakhale ku ntchito zomwe za chisomo zimene zinamuitana iye mpaka pa malo amenewo ndi kusonyeza izo kwa iye, ndiyeno nkupotoloka apo, kuyenda nkuchoka kwa izo. Iye akuwawerengera Magazi a pangano amene iye anapachikidwira...Khristu anapachikidwira ngati chinthu chosayera. Chifukwa Magazi amene anamupulumutsa iye, ndi kumulumamitsa iye, ndi kumuyeretsa iye anamufikitsa iye mpaka ku ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndiyeno nkuyenda kuchokapo ndi kuwasiya iwo...

<sup>289</sup> Tsopano, penyani ndondomeko imeneyo. Ine ndikutenga nthawi yambiri, koma penyani! Yudasu Iskarioti anatsatira mkwakwalala womwewo. Iye analungamitsidwa pa kukhulupirira pa Ambuye Yesu ndipo kenako pomulandira Iye ngati Mpulumutsi wake. Iye anayeretsedwa ndi kumupatsa mphamvu kuti azitulutsa mizimu; kuika dzina lake pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Koma pamene izo zinafika ku Pentekoste ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, chidzalo cha Mawu, iye anasonyeza mangamanga ake. Izo ndizo ndendende zimene azondi aku Kenani anachita; izo ndizo ndendende zimene Esau anachita.

<sup>290</sup> Izo ndizo ndendende zimene Satana anachita kwa Eva mmunda wa Edeni: “Ndithudi Mulungu sadza...”

Koma iye anati, “Mulungu anati. . .”

Iye anati, “Eya, ine ndikudziwa iwo amanena izo; ine ndikudziwa iwo amanena *izi*, koma ndithudi. . .” Mukuona, chinthu chofanana kudutsa mu njira yonse, ndipo ndi momwe ziriri lero.

<sup>291</sup> Mpingo watsatira kupyola mu Kukulungamitsidwa, Marteni Lutera; kupyola mu Kuyeretsedwa, Wesile. Koma iwo, pamene iwo ukufika ku nthawi ya ubatizo wa Mzimu Woyera, iwo amaonetsa mitundu yao; iwo samafuna kanthu kochita nawo Iwo. A Nazerini, A Pilgrim Holiness, a Church of God, onse awo uko amene amakhulupirira mu kuyeretsedwa, inu simungati muloze chala kwa izo; ndi choonadi. Koma pamene izo zifika pa mzere wammalire, kubwera kumene mpaka pa malo amenewo kuti alandire Mzimu Woyera wa kubadwa kwatsopano, ndiye kodi mdierekezi amachita chiani? Amabwera apo ndi kuyesera kuti achipotokole icho mozunguza. O, iye. . . iye angachite chirichonse chimene chiri mu mphamvu yake yodziwika kuti awachotse anthu kumeneko.

<sup>292</sup> Iwo anabweretsapo icho, ndi kuti, “Iwe uyenera kuti uyankhule ndi malirime. Iwe uyenera kuti ukhale ndi chomverera. Iwe uyenera kuti uzichita *izi*.” Iwe uyenera kuti ubadwire mu iwo. Musati muzimulola winawake azikuuzani inu kuti kuyeretsedwa ndi Mzimu Woyera ziri chinthu chimodzimodzi, chifukwa izo siziri choncho! Ndithudi si ziri!

Mvetserani pa wa Nazereni uyu kumbuyo uku akufuula, “Izo si ziri.” Mukuona? Iye akudziwa kuti pali kusiyana mu izo, chifukwa izo ndithudi ziri. M’bale Capps, m’bale wathu wochirimika. Mukuona?

<sup>293</sup> Zedi, Nazereni. . . Palibe munthu wina amene angati anene mawu otsutsa anthu abwino achipembedzo awo; iwo ndi abwino basi momwe iwo angakhalire. Mpingo wa Mulungu, Nazereni, Free Methodisti, anthu amenewo ndi enieni, koma pamene izo zifika mpaka ku ntchito za Mzimu, iwo amati, “O, o, ameneyo ndi mdierekezi.” Ndipo kodi iwo amachita chiani pamene? Kuchitira mwano Mzimu Woyera. Pamene iwo achita zimenezo. . .

<sup>294</sup> Tsopano, kodi kuchitira mwano Mzimu Woyera ndi chiani? Apo palibe chikhululukiro. Kodi uko nkulondola? “Iye amene anayamba wawunikiridwapo, anapangidwa kugawana nawo, ndipo analawa za mphatso zakumwamba.” Kug-. . . Analawa—analawa za chiyeretso cha Mulungu: anayeretsedwa ku ndudu, ndi akazi auve, ndi mitundu yonse ya moyo monga choncho. “Ndipo analawa za zinthu zakumwamba.” Kuti awone kuti iwo ayenda mpaka ku mzere wa mmalire uwo monga azondi aja anachitira amene anadya gawo la mphesazo. Koma kodi iwo anayenera kuti achite chiani? Iwo anali oti aswe chipembedzo chawo kuti abwere mu ichi. Mukuona? Mukuti. . . Mukuona?



“Analawa za mphatso zakumwamba; powona kuti iwo akumupachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu katsopano; ndi kuwawerengera Magazi a pangano amene iwo anayeretsedwa nawo ngati chinthu chosayera.”

<sup>295</sup> Kuyeretsedwa ndi pamene dzina lako limapita pa bukhu ngati wokhulupirira. Mawu ako... Dzina lako limalembedwa mwa Magazi Ake. Mukuona? Kuyeretsedwa kumachita zimenezo; ndipo iwe umabwera pamwamba, pamene Iye wakudalira iwe mpaka utali woterewu, ndiyeno nkubwera apo... Iwo amati, “Chabwino, kodi Iye angazidziwe zimenezo?”

<sup>296</sup> Inde, Iye anazidziwa izo. Iye anadziwa kuti inu simukanati mudzachite izo pa chiyambi. Iye ankadziwa kuti Yudasī sakanadzachita izo. Iye ankamudziwa iye kuchokera pa chiyambi; iye anali mwana wachitaiko. Koma zinthu zimenezo ziyenera kuti zizikwaniritsidwa. Mukuona? Mawu ayenera kuti azikwaniritsidwa, onse, kupyolera mu zoimira ndi mithunzi. O, mai! Ife tikanakhoza kukhala pamenepo kwa maora.

**370. M’bale Branham, pamene inu munapereka uthenga pa masabata sevente a mpingo...masabata sevente (Ndikhululukireni ine.) a Daniele, ine ndikhulupirira kuti inu munanena kuti lathunthu—sabata lotsiriza lathunthu kapena zaka zotsiriza seveni zidzayambika pamenepo Mkwatibwi atatengedwa mu Mkwatulo.**

<sup>297</sup> Ayi, ayi, ayi, ayi, ayi, uu, uu, uu! Inu muzinamva izo molakwika (mukuona?), osati masabata seveni athunthu. S—sabata linayambika pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi. Iye anati, “Mesiya, Kalonga, adzabwera ndipo adzanenera, ndipo mkati mwa masabata seveni, Iye adzadulidwapo.” Ndipo Yesu analalikira ndendende zaka 3½, limene liri theka la masabata sevente, masiku seveni, sabata—masiku a sabata. Mukuona? Ndipo pali zaka 3½ zimene zatsalira.

<sup>298</sup> Tsopano, pamene Mose ndi Eliya akubwera pa dziko lapansi, chimene chiri Chivumbulutso ndi Zakariya... (M’bale Coomer funso lanu—lanu ndi la M’longo Coomer apo linali chimodzimodzi.) Tsopano, pamene iwo... Pamene Zakariya 4 ndi Chivumbulutso 11, mitengo iwiri ya azitona iyo ndi zina zotero, amene ali Mose ndi Eliya, pamene iwo abwerapo pa dziko lapansi iwo akunenera masiku 1,264. Ndi chiani chimenecho? Ndendende zaka 3½. Izo zinali ndendende chinthu chomwecho. Osati... Mukuona? Yense yemwe munthu wokonedwa uyu ali. Mokongola, kwambiri mbiri, walembe—walembe pa pepala lokhala ndi mutu wa chipembedzo utalembedwa—mizere apa ndi zinthu, ndipo ndi zabwino kwambiri. Ndipo ilo ndi funso labwino kwambiri, koma (mukuona?) inu simunamvetsetse izo, basi zimene ine ndinanena. Ine sindinayambe ndakhulupirira kuti masabata sevente onsewo akanadzakhala cha kuno. Mesiya

anadulidwa. Ndi angati akukumbukira zimenezo mu kulalikira komwe kuno? Ndithudi! Mukuona? Masabata seveni.

**371. Kuyambira pamenepo zikuwoneka ngati zaka zitatu ndi theka limodzi zoyambirira zinakwaniritsidwa mu nthawi ya utumiki** (Chabwino, inu apa muli nazo apa pomwe.) **wa—wa Yesu, koma kafotokozedweko “mkati mwa masabata” kakuwoneka kuti akugwiritsidwira ntchito kwa wotsutsakhristu yekha pakuswa pangano lake ndi . . .** (Ayi, wotsutsakhristu uyo akuswa pangano lake pa mapeto a zaka zitatu ndi theka zotsiriza. Mukuona?) **Momwe ine ndinamvetsetsera tepi ya Daniele, masabata oyambirira sikisite-naini anatha pamene Yesu anakwera akulowa mu Yerusalemu A.D. 30, kotero kuti zaka zitatu ndi theka za utumiki Wake zikanati zikhale limodzi mu masabata sikisite-naini; ndipo masabata athunthu otsirizira—ndipo sabata lathunthu lomalizira kapena zaka seveni zikanati zikwaniritsidwebe ndipo zikanati ziyambire pa mkwatulo. Chonde talongosolelani izi kwa ine.**

<sup>299</sup> Inu mukudziwa, m'bale, mlongo, yense yemwe ali amene wafunsa funso ili. Labwino kwambiri (mwaona?), koma ine ndikukhulupirira kuti inu mwasokonezeka pang'ono pa zimene ine ndinanena. Mukuona? Tsopano, a . . . Pamene Yesu anabwera mu Yerusalemu (kumeneko ndi ndendende kulondola), amenewo anali mapeto a . . . Mukuona? Iye anapita molunjika kumene umo kuchokera pamenepo ndipo anakapachikidwa. Mukuona? Ndipo I—Iye ananenera kumene theka la masabata sevente awo limene ili 3½. Tsopano, Iye anadulidwapo, ndipo moyo Wake unapangidwa kukhala nsembe. Ndipo tsopano, apo pakanabwera ndiye . . . Mu masiku otsiriza ano, pali zaka 3½ zolonjezedwa apobe kwa—Ayuda. Ndipo . . . mu nthawi iyi panali kusonkhanitsa kwa oyera kwa mkwatulo, Mpingo.

<sup>300</sup> Tsopano, ine sinditi nditenge zonse izi nkutsiriza, M'bale—M'bale, Mlongo.

**372. Chonde kodi inu mungalongosole Akorinto Woyamba, mutu wa 7 ndime 1 ndi 9?** (Pezani izo, M'bale Neville, Akorinto Woyamba, mutu 7, ndime 1, tsopano.)

**373. Ndipo kodi wokhulupirira woona aliyense azidzachita ntchito zimene Yesu ananena, momwe zanenedwera mu Yohane Woyera 14:12** (Osati ndendende. Ayi!): **kuchiritsa odwala, kutulutsa ziwanda, kuukitsa akufa** (ine sindikuganiza kuti zimenezo ziri mu Yohane Woyera 14, koma zonse ziri bwino. Izo ndi Mariko 16.), **ka—kapena ziri . . . kodi izi ziri kwa Eliya yekha? Kodi wokhulupirira azichita zonse izo . . . za izi . . . azichita kwenikweni . . . amene akukhulupirira kwenikweni? Ndipo ngati iye ali wokhulupirira weniweni, kodi iye aziaukitsa akufa ndi kumachita zozizwitsa zazikulu?**

<sup>301</sup> Tsopano, zimenezo ziri zapakati pa okhulupirira. Mukuona? Munthu aliyense samakhala nazo mphatso zimenezo, ndipo sizikutanthauza kuti munthu mmodzi yekha azichita izo; pakhala pali magulu a anthu. Monga mwa chitsanzo, bwanji ng—ngati ife tikanakhala naye msungwana wamng’ono muno mu mpingo, kapena mnyamata wamng’ono, kapena winawake amene ife timamukonda mwabwino kwenikweni, ndipo moyo ukanachoka mwa iwo. Mpingo wonse ukanabwera palimodzi, ndipo iwo angapite kukapemphera ndi kusala: “Ambuye, chitirani chifundo pa mwana ameneyo.” Mukuona? Mulungu akanakhoza kumuukitsa iye apo.

<sup>302</sup> Ndi angati amene anawerengapo apo *Nicaea Fathers* ndi iwo? Inu mukudziwa, umu ndi momwe iwo ankachitira izo mu mpingo woyambirirawo. Iwo onse ankabwera palimodzi, inu mukudziwa, ndipo ngakhale kumuukitsa m’busa wawo nthawizina ndi ena osiyana monga choncho, ngati Mulungu anawona kuyenera koti achite izo; koma iwo ankachita izo.

**374. Ngati mpingo uli wopulumutsidwa ngakhale iwo sali kupita mu mkwatulo, momwe ine ndikukhulupirira kuti inu munaphunzitsa, iwo uyenera kuti udutse mu chisautso kuti ukayeretsedwe. Koma nanga bwanji awa amene anafa, iwo adzayeretedwa bwanji?**

<sup>303</sup> Chabwino. Iwo amene ali nazo izo. . . Mkwatibwi sakusowa kuyeretsedwa; Iye wapangidwa ungwiro kale. Ndipo iwo amene ali—a—anafa mmbuyo umu, awa amene akudutsa umu. . . Mukuona? Iwo sanalandire konse Kuwala kumene mipingo iyi pamwamba apa yalandira; iwo anakhala moyo pansu pa Kulungamitsidwa kwawo, Kuyeretsedwa, zina zotero monga izo. Iwo anakhala moyo kwa Kuwala kumene iwo anali nako, mwinamwake mwa—mwa njira imene iwo anavutikira, ndi chirichonse chimene iwo anadutsamo nacho, ndi kuzunzika kwawo. . . Koma tsopano, mu nthawi ya kukwatulidwa iyi monga chonchi (mukuona?), apo padzayenera kubwera nthawi tsopano imene mkwatibwi uyu ati (amene akukana gawo la Mutu wa Mkwatibwi) adzayenera kuti adzavutike chifukwa cha kukana kwawo, chifukwa Uthenga unali usanapangitsidwe kumveka kwa iwo mmbuyo umu, momwe iwo wapangitsidwira kumveka kwa inu lero. Mukuona? Inu mukuwuona iwo momveka. Inu mwakhala nazo kale zaka zonse izo ndi zitsanzo, Zisindikizo kutsegulidwa, M’badwo wa Mpingo kuikidwa apo, ndi chirichonse monga choncho. Izo ziri zomveka kwambiri basi inu simungathe kuziphonya zimenezo. Mukuona? Ndiyeno, ngati inu muzikana kwathunthu zimenezo, pali chinthu chimodzi chokha mungachite, kuvutika chifukwa cha izo.

<sup>304</sup> Kodi inu mwapeza apo M’bale Neville? Kodi izo zikukamba za chiani? Ine basi. . . ine kulibwino ndizipita tsopano, chifukwa tikufika pochedwa kwambiri. Inu mukuona? Ndiri. . . Seveni—seveni, naini. . . Tiyeni tiwone.

*Koma ngati iwo sangadzigwire, asiyeni iwo akwatire:  
pakuti kuli bwinoko kuti akwatire kusiyana ndi  
kutenthedwa.*

<sup>305</sup> Chabwino. Izo ndi za makhalidwe oyipa chabe. Mmaloti moti mwamuna, mnyamata, msungwana, kapena chinachake kapena chimzake pamene iwo akuyenda limodzi n—ndipo iwo akudziwa kuti iwo akuyenera kukwatirana, pitirirani nazo ndi kukwatirana. Ine ndikuganiza i—inu mungathe kumvetsa chimene ine ndikutanthauza, si choncho inu? Mukuona? Musati muzingokhala moyo wawung’ono wauve kumeneko, chifukwa izo si zoyenera. Inu mukuona? Ameneyo ndi mlongo wanu mwa ganizo lina, pamene ngati inu muli Mkhristu. Tsopano, ngati liri dziko, ilo ndi dziko: garu amadya garu. Koma msungwana uyu amene inu mukuyenda naye, ameneyo ndi mlongo wanu nayenso. Ameneyo adzakhala mayi wa a—ana anu amene ati adzabwere. Musati muzikhala kamoyo kauve pa iye, sonyezani kuti inu ndinu njonda ya Chikhristu yeniyeni. Zikakhalani moyo momwe njonda ya Chikhristu imayenera kumakhalira. Mukuona? Ndipo muzimuchitira iye mlongo wanu, ndipo pamene inu mudzakwatirana, muzidzamuchitirabe iye mwanjira imeneyo.

<sup>306</sup> Ine ndikhoza kuliyanika ili pakali pano. Ine sindimakhulupirira mu makhalidwe onyansa pakati pa anthu Achipentekoste, anthu achiyero, ngakhale ngati iwo ali okwatirana. Ine sindimakhulupirira mu zimenezo. Ayi, bwana! Zina za zinthu zauve izi i—izo ziri zoipa kwambiri. . . Ine ndimalowa muno nthawizina pa zimenezi. . . Osati mmawa uno tsopano, ayi, ine sindikunena zimenezo. Koma ine ndikutanthauza pa nthawi zimene ine ndimakhala ndiri mu California ndi malo osiyana onga amenewo. Ine ndimakomana nawo atumiki kumeneko, kumene pa kuzindikira za mumtima, ine ndimamverera ngati ine ndikanangowatembenezira iwo pa bondo langa ndi kuwapatsa iwo “kukondoweza pang’ono kwa chikwapu cha Uthenga.” Inde, bwana! Mai, kumuwona mwamuna amene amayesera kuti amutenge mkazi wake wamng’ono, ndi zanyasi, zauve, zimene ziri. . . Inu mukumvetsa zimene ine ndikutanthauza. Ine ndikuganiza kuti inu mukuyenera kumadzichitira nokha manyazi ngati munthu wa Mulungu kuti. . . Inu mungokhala mwamunake; khalani wokomamtima. Zimulemekezani iye momwe inu nthawizonse munkamulemekezera iye. Musati muzikhala ndi chidwi kwa izi, zina mwa izi. . . mabuku azosagonana, kapena zopandapake izi mu mabuku azogonana awa, ndi zinthu zimene inu mumawerenga za izo, ndi zonse za zinthu izi, ndi chirichonse monga icho. Chotsani zinthu zauve izo mu malingaliro anu.

<sup>307</sup> Baibulo linati musalole zoyankhula zauve zimodzi pakati panu pamene inu mukuti ndinu achiyero. Muzimuchitira dona wamng’ono uyo ngati iye ndi wokomamtima wanu wamng’ono. Ngati iye ali usinkhu wa zaka sikite, inu mudzakhale

muli chimodzimidzi basi. Inu mukhale bwenzi lachimuna lokhazikika; kumbukirani, inu muli.

Inu musati muziyesera chirichonse cha zinthu zatsopano izi, ndipo ine ndikudziwa zimene ine ndikunena. . . Ndipo inu mungokhala mwamunake, m'bale weniweni, Mkhristu weniweni.

Ine ndikudziwa izo zikumveka ngati. . . Koma. . . Inu ndinu ana anga. Ine ndiri nawo ufulu wa kunena zimene ine ndikufuna kwa inu. Inu mukuona? Inu ndinu ana anga; inu muzikhala moyenera.

<sup>308</sup> Ndipo inu akazi, muzikakhala mwanjira yoyenera kwa amunanu. Ndipo inu amunawo, muzikakhala moyenera kwa inu. . . kw—kw—kwa akazanu. Khalani kwenikweni abwino ndi kulemekezana wina ndi mzake basi ndi. . . Ndipo ch—chijanano chanu chapabanja ndi zina zotero monga izo, mulole izo zingokhala molemekezeka, ndi mwaumulungu, ndi mogwirizana pakati panu ndi chirichonse momwe izo zingakhalire ziri. Musati muzikankhana konse, ndi kukokana, n—ndi kukhala wauve ndi wazonyansa.

<sup>309</sup> Muzimvetsetsana, kuyankhula naye mkazi wanu. Ng—ngati mchitidwe wina uli kwa inu ndi mchitidwe wina kwa iye, yankhulani naye iye. I—inu muziyesera kuchita chinthu mofanana kwa mwamunayo, mlongo. Ndipo chimodzimidzi. . . Muzimvetsetsana wina ndi mzake ndi kukhala—kukhala njonda ya Chikhristu yeniyeni ndi madona enieni a Chikhristu, nd—ndipo m'bale ndi mlongo wina ndi mzake. Nthawizonse muzikumbukira, inu ndinu ana a Mulungu, ndipo ndinu ochokera ku Banja Lachifumu. Inu ndinu magazi achifumu; palibe magazi abwinoko mu dziko kuposa anuwo. Ndipo uko nkulondola! Ndipo magazi achifumu amadziwonetsa okha. Ndicho chimene iwo ali, iwo ndi achifumu. Onse amene mukukhulupirira zimenezo itini, “Ameni!” [Osonkhana ayankha “Ameni!”—Mkonzi.] Inde, bwana! Zisonyezani chimene inu muli. I. . . i. . . ine ndine mwana wa Mfumu, ine ndine mwana wa Mfumu. Mkazi wanga ndi mwana wamkazi wa Mfumu. Ine ndingati ndizichita naye motani mwana wamkazi wa Mfumu uyo? Iyeyo angati azichita naye motani mwana wamwamuna wa Mfumu uyo? Mukuona zimene ine ndikutanthauza? Mukhale enieni moon.

**375. Kodi padzakhala pali kusuntha kwa Mzimu Woyera, zizindikiro, ndi zodabwitsa, ndi zozizwitsa zikuchitidwa ndi Mkwatibwi iye asanachotsedwepo, kapena kodi ife tikungodikirira kuwonekera Kwake?**

<sup>310</sup> Ine ndikuti nditsekere pa limenelo, ine ndikuganiza, chifukwa ine ndangokhala nazo zochuluka kwambiri apa zoti ndifike kwa izo. Ndipo tiri kufika pochedwa kwenikweni. Ali maminiti twente isanafike wani tsopano, ndipo ine ndiri

nalo pafupi sate kapena forte a iwo mwinamwake pano, mwinamwake. Ine ndiyankha izi mwa kupambana kwa nthawi yanga. I . . . ine ndingotenga maminiti atatu otsatirawa. Ine ndidzatenga izi pamene ine ndingathe. Mukuona? Ine sindikudziwa liti limene ine ndidzathe kuwatenga iwo; ine ndidzachita mwa kupambana kumene ine ndingathe. Kodi inu mukukomedwa nawo? I . . . Izo zikundithandiza ine apanso. Mukuona?

Kubwera kuno ndi kudzawatenga iwo munga chonchi, iwe usanayang'ane nkomwe mwa iwo (inu mukuona?), iwe umapezamo zinthu zina zimene iwe sungathe kuziyankha, n—ndipo i—ine ndinali mu ziyembekezo kuti ine ndiwatenga iwo . . . Ine ndikudziwa pali limodzi mkati umu lokamba za mbewu ya serpenti. Ine ndimafuna kuti ndilitenge ilo moyipa kwambiri; ine ndimafuna kuti ndifotokoze izo. Mukuona? Koma ine ndikuganiza ine ndinangoliphonya ilo, kotero ine ndingokhala nao . . . Mwinamwake Ambuye sakufuna kuti izo zichitike mwanjira imeneyo, koma ilo linali pa mbewu ya serpenti. Kuwopa kuti winawake pa tape imeneyo akanati apite ndi kumakati, “Chabwino, iye anachita, iye analilambalala ilo.” Ndi angati amene ati apirire maminiti awiri ena pa ilo? Nhu? Chabwino.

<sup>311</sup> Chabwino dikirani, ndiroleni ine ndilipeze ili poyamba. Tiyeni tiwone! “Kodi—a . . .” Ayi. Funso ili apa liri chonchi: “Kodi padzakhala zozizwitsa zikuchitidwa ndi Mkwatibwi?” Inde, bwana! Izo zikuchitidwa pakali pano. Uko nkulondola! Mukuona? Koma musati muziyang'anira chinachake chachikulu chomwe . . . kapena kubweretsa miyamba ndi kutseka miyamba, iyo nkusavumba. Izo zipita kwa—Ayuda tsopano. Mukuona? Izo si zikunena za izi konse; ameneyo ndi Mose ndi Eliya kwa Ayuda, osati kwa Mpingo uwu konse. Kawerengeni mitu itatu yoyambirira ya Chivumbulutso; inu mupeza chimene Mpingo uli apo pomwe. Izo zonse ndi za Mpingo. Ndipo pamene iwo ubwerera ndi Mkwatibwi, pamene iye azibwerera ndi . . . Werengani . . . Ngati inu mukufuna kuti mudziwe za Mpingo, chimene chiri cha kwa Iwo, werengani Chivumbulutso mitu itatu yoyambirira, ndiyeno pitani ku mutu wa 19 ndi kuyamba kuwerenga kuchokera pamenepo. Ndiye inu mukampeza Mkwatibwi. Zina zonse za izo ziri mwa Ayuda kumeneko.

<sup>312</sup> Tsopano, ku mbewu ya serpenti. Ine sindikutha kulipeza ilo mkati umu, chifukwa (inu mukuona?) ndi mulu waukulu basi wa iwo. Koma munthuyo anati, “Ngati serpenti—ngati mbewu ya serpenti (mukuona?) . . . Mkazi, iye . . . iye analandira mwana kuchokera kwa Ambuye, iye ananena choncho.”

Chabwino, ine ndikukhulupirira Lamlungu lapitalo, ine ndinalongosola momwe iye anamupeza iye kuchokera kwa Ambuye. Ngati iye anamupeza iye konse, iye anamupeza uyo

kuchokera kwa Ambuye (mukuona?), chifukwa anayenera kuti abwere kuchokera kwa Ambuye. Chifukwa lamulo la Mulungu liri nalo . . . Ilo li . . . ilo limamumvera Mulungu. Ndendende.

<sup>313</sup> Iye analamulira kuti dzuwa liziwala, ndipo dzuwa limawala. Iye analamulira kuti mvula izigwera pa olungama ndi osalungama; iyo imachita zimenezo. Ndipo mbewu zobzalidwa mmunda uliwonse, ngakhale izo ziri zabwino kapena zoipa, zidzatulukira apo; izo ndi mbewu. Ndipo ngati mbewu ibzalidwa, ziribe kanthu . . .

Ndipo njira yokha serpenti iyi ikanati ibzalire mbewuyo, iye anali chinyama chokha chapafupi kwa munthu wokhalapo. Pakuti mu kasinthidwe ka mtundu wa anthu, pamene munthu . . . Mulungu anafungatira pa dziko lapansi . . . Ndipo Iye anayamba kubalapo mbalame, ndi . . . kuchokera pa mbalame Iye anabwera ku zinthu zosiyana, kenako chimpanzi, ndipo kuchokera pa chimpanzi mpaka kwa serpenti.

<sup>314</sup> Tsopano, Iye anamusintha serpenti uyo mwa njira yotero (zimene zinkayenera kuti zichitidwe) zimene zikanati zisokoneze kam'badwo kano, amene akuyesera kuti apeze fupa limene limawoneka ngati mtundu wina wa chinyama chimene chinali gawo lina munthu ndi gawo lina chinyama, kuti ati apo ndi pamene munthu . . . Iwo azitaya izo kuchokera kwa chimpanzi; kungoti chimpanzi chiribe luntha. Chimpanzi chiribe solo; iye sangathe kuganiza. Iye ali basi . . . I—iye angathe . . . Basi p—phokoso, ndipo iye angathe . . . Kavalu, “gii,” “hoo,” kapena chinachake chonga izo. Garu, “Bwera kuno, Fido, chita tsenga. Lumpha apo!” Ndi kuyika zotchinga ndi zinthu monga choncho, iwo amachita zimenezo mwa kutengeka, mwakumva, ndi zinthu monga choncho, chochitapo; koma kuti aganize ndi kumvetsetsa, iwo sangathe. Iwo samadziwa kuti ali amaliseche, iwo samadziwa wamphongo ndi wamkazi, kusiyana kwake, monga choncho. Iwo alibe malamulo a zoterozo . . . ? . . . Mukuona? Iwo sangathe kuchita zimenezo. Munthu wokhalapo ndi iye yekha.

Ndipo wina wotsatira kwa munthu wokhalapo anali serpenti. Baibulo linati iye anali wochenjera kwambiri mwa zinyama zonse za kutchire. Wanzerupo, i—iye—iye anali pafupifupi kukhala nayo solo. Iye anali nawo malo a solo, koma kodi iye anachita chiani? Iye anadzigulitsa kwa Satana kuti amunyenge Mulungu, kuyesera kutero. Ndi angati akumvetsa zimenezi tsopano mpaka apo?

<sup>315</sup> Satana, serpenti, pafupifupi anali nayo solo. Mulungu ankadziwa kuti iwo akanati azidzawafunafuna mafupa amenewo, ndipo palibe fupa mwa njoka limene limawoneka ngati la munthu. Iye anali . . . Limenelo ndiye themberero lake. Iye ankaima pa mapazi ake basi monga munthu.

316 Zindikirani, ndiye mbewu imeneyo, imene inali yapafupi ndi mbewu ya munthu. . . Satana mwiniwake, mzimu, ankadziwa kuti imeneyo inali mbewu yokha imene ikanamupatsa mimba mkaziyo, chifukwa chimpanzi sichikanati chichite izo. Iwo azisakaniza izo ndi china chirichonse; iyo siingachite kuchita zimenezo. Koma iye ankadziwa kuti nyongolosi ya moyo imene inali mwa chimpanzi siikanati ibwere ku munda wa dzira la mkazi; koma iye ankadziwa kuti mbewu ya serpenti ikanati idzachite izo, chotero iye anachita naye serpenti.

317 Ndipo Adamu anali asanadziwe nkomwe kuti kachitidwe aka kakanati kachitike. Mukuona? Iye anapangidwa ali mkazi. Ndithudi, iye akanati adzafike kwa izo mtsogolo; koma inu mukuona, kuchita kwa mwayekha kwa Mulungu kuti adziwonetsere Iyeyekha ngati Mpulumutsi n—ndi zina zotero, monga ine ndafotokozera nthawi zambiri. Koma Satana ankadziwa izi, pakuti iye anabwera kwa iye mumawonekedwe a serpenti iyi, imene inali chinyama, ndipo—chinyama; ndipo anabwera kwa mkaziyo. Ndipo anakhala napo pakati ndi Satana poyamba.

318 Ndipo ngati inu mungazindikire, apo panali kuchita kuwiri kokha, ndipo apo panali ana atatu amene anabadwa. Kafufuzeni Lemba. Iye anabala mapasa. Mmodzi wa iwo anali mbewu ya serpenti; winayo anali Abele. Mkaziyo anamunyenga mwamuna wake ndipo anamuza. . . Mukuona? Ndiye iye anamusonyeza mwamuna wakeyo chimene icho chinali, ndiyeno iye anakhalanso ndi mkaziyo, ndipo iye anabala mwana uyu. Ndipo ine ndikufuna inu. . . kuti tisonyeze kuti iye anakhala napo pakati pa mapasa a awiri osiyana. . . Iye anali. . . Ameneyo ndi mkazi wanamwali.

319 Iwo ali, mukuona, iwo ali amphamvu. Monga yang'anani apa. Abrahamu anakwatira mlongo wake yemwe. Bwanji, ngati mwamuna angakwatire mlongo wake lero, ana ake akanati akhale zitsiru. Mukuona? Koma munthu. . . Ndipo apa Yakobo. . . k—kapena Isaki anakwatira Rabeka amene anali msuwani wake yemwe, msuwani wa magazi ake pamenepo, ubale wa magazi, mwaona, mwana wa achimwene ake a Abrahamu.

320 Zindikirani, zindikirani tsopano, pa ichi, onani, apo pali. . . mtundu wa anthu unali wamphamvu kwambiri. Tsopano, ngati inu mungazindikire nthawizonse akhala ali mapasa njira yonseyo. Uko kunali. . . Kaini ndi Abele anali mapasa, ndipo Esau ndi Yakobo anali mapasa. Yesu ndi Yudasi anachokera ku mtundu wofanana ndi mu mpingo wofanana. Ndipo. . . Ngakhale Mzimu Woyera ndi wotsutsakristu ali woti angakhale mapasa, “Apafupi kwambiri kuti akanati anyenge Osankhidwa omwe ngati nkotheke.” Kodi mwazimva zimenezo? Chabwino.

321 Tsopano kuti titsimikizire ichi, ine ndikufuna kuti inu mutenge Yuda. . . ine ndikukhulupirira ndime ya 17, kapena



ndime ya 14 ya Yuda ndipo anati...Tsopano, tsopano, zindikirani ichi. Tsopano, ine nditseka. Zindikirani. Kuti ndidulepo chinthu chonsechi kuti tichipangitse icho bwino, malo oyamba Iye anati, “Ine ndiika udani pakati pa mbewu yako ndi mbewu ya mkaziyo.” Mukuona? Tsopano, mkazi alibe mbewu. Chotero, momwe iye anaizepera mbewu iyi inali mbewu ya Satana. Kaini anali mwana wa Satana. Mkaziyo analibe mbewu, chotero iye anailandira iyo kupyolera mu kugonana. Ndipo pamene iye anachita izo, iyo inapatsidwa kwa iye ndi mdani wa Mulungu. Ndiyeno, pamene Mulungu anamupatsa iye Mbewu, Iyo inalibe kugonana konse mwa Iyo. Inu mukuzimvetisa izi? Mkazi wamunsinga ndi mwana wake anaponyedwera kunja, chifukwa iwo sakanadzakhala olandira nao limodzi ndi mkazi waufulu ndi mwana wake.

<sup>322</sup> Ndipo zindikirani, ndiye iye anapatsidwa Mbewu imene inali Khristu. Popanda dzira lake...Tsopano, Aprotestanti amafuna kuti akhulupirire kuti awo anali magazi opereka moyo obadwira mwa namwali, awo anali Magazi a Mulungu ochita kulengedwa mmene munali nyongolosiyo, koma amati ilo linali dzira lake. Ayi, bwana! Dzira limenelo silingati libwere mmusi kudzera mu chubu icho kukalowa mu chiberekero kupatula ngati pakanakhala kugirigishika. Ndiye inu mukumuika Mulungu limodzi nao, m—Mzimu, kuchita zogonana ndi mkazi. Kodi zimenezo zingachitike motani? Icho chinali chinthu chochita kulengedwa cha Mulungu mu zonse, zonsezo dzira ndi nyongolosi.

<sup>323</sup> Ndipo Iye anali Mwana wa Mulungu, osati mwana wa Maria, pakuti Iye sanamutchepe konse iye kuti amake. “Mkazi,” Iye ankamutcha iye, osati amayi. Iye sanali amayi Ake. Iye anali Mwana wa Mulungu, ndipo Mulungu ndi Mmodzi. Mukumvetisa zimenezo?

<sup>324</sup> Tsopano, chinthu china kuti titsimikizire izi ndi kuzikhomerera izo apa, pamene ngati wina aliyense atati azitsutsana ndi inu, bwererani umu mu Bukhu la Yuda, ine ndikuganiza ndi ndime ya 17 (ndime ya 14 kapena ya 17), iye anati, “Tsopano, Enoki . . .” Inu mukufuna kuti ine ndiwerenge izo? Kodi inu muli nayo nthawi yochuluka chotero? T—tiyeni . . . ndiyeno ine ndipeza . . . Ndiye ine ndidziwa, chifukwa tepiyo apa ikupitirira, ndipo i—ife tikhoza kusokonezeka izo m—mu izi tsopano. Ndiroleni ine ndiwone ngati izi . . . ndime ya 14:

*. . . Enoki nayenso, wachisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Adamu, ananenera za zinthu izi, kuti, Taonani, Ambuye akudza limodzi naye zikwi makumi za oyera.*

<sup>325</sup> Tsopano, bwererani ku mutu wa 5 (ine ndikuganiza apo pali) wa Genesis, ndiyeno mupitenso, uko mu Bukhu la Luka (ndikukhumba ine ndikanapapeza apo; ine ndinazilemba izo zonse apa, ngati ine ndikanatha kupapeza apo mkati) ndipo inu

muzipeza izo mu obadwapo, palibe paliponse mu Baibulo... Ngati...Penyani! Ngati Nowa...Ngati Enoki ali wachisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Adamu, Baibulo linati, “Adamu ndipo kenako mwana wake Seti,” chifukwa Kaini sanali mbewu ya Adamu. Apo akuti Adamu anabala Seti, ndipo Seti anabala...Yaredi; Yaredi anabala, ulendo wonse mpaka kwa Enoki; ndipo Enoki anali wachisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Adamu. Palibe pamene ilo likuyankhula konse kuti Kaini anali kutengedwa konse kuti ali chirichonse mu obadwapo a Mulungu.

<sup>326</sup> Tsopano, tangoyang’anani ndi kupeza ngati izo ziri chomwecho kapena ayi; fufuzani izo. Ndipo Luka akubwera apo ndipo akutchula iwo apo pomwe mobwereza, ndipo akulemba apo kuchokera kwa Adamu. Palibe nthawi imodzi pamene Kaini akutchulidwa konse mu chinthu chonsecho. Ndipo ngati Enoki (mukuona?) anali wachisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Adamu, Kaini anabwera kuchokera pati? Chifukwa Baibulo linanena kuti, mu obadwapo, kuti Adamu anabala mwana wake, Seti. Ndipo Seti anabala Yaredi, ndipo Yaredi anabala *Wakuti-ndi-wakuti*, mpaka pansi; ndipo palibe nthawi imodzi pamene Kaini anatchulidwa konse. Ndiye iye sangati akhale ali mwana wa Adamu. Chotero iye anayenera kukhala ali mwana wa serpenti, ndipo iye sakanati akhale mwana popanda kugonana. Amenii! Ngati iye sanali, iye anali wobadwa kwa namwali, ndiye iye akanakhala ali mwana wa Mulungu. Ine ndikufuna iwo achoke mu zimenezo nthawi imodzi.

<sup>327</sup> Tsopano, Mulungu yemweyo amene anawulula zimenezo, ali Mulungu yemweyo amene anandiuza ine za chikwati ndi chilekano chanu. Pamene Iye anena zinthu zimenezo, M’bale wanga, Mlongo...Ine ndine m’bale wanu, mwamuna. Koma pamene Iye anena zimenezo, ndipo izo zimakhudza pansi mkati umu, ine sindingathe kulongosola izo kwa inu. Palibe chosowekera kuti ine ndiziyesera kuchita zimenezo, chifukwa ine sindikanatha. Koma izo sizinayambe nthawi imodzi zakhala ziri zolakwika. Ngakhale, ine sindikanatha kuziwona izo inemwini konse, ine sindikanatha kuziwona izo, koma ine ndinangogwiritsitsa mopitirira kwa izo; ndiyeno Iye anayamba kuziwulula izo, ndiye ine basi—izo zimangondigwetsa ine. Apo izo zinali apo pomwe, ndipo ine sindinali kuziwona izo. M—maphunziro anu alambalalidwa, ndipo zoganizapo zanu zalambalalidwa, ndi china chirichonse; choteronso Kaini analambalalidwa.

Tsopano, ngati ife tikanakhala nayo nthawi kuti tibwerere mmbuyo mu Genesis ndi kukayamba kuwerenga...Tiyeni tiwone ngati ine ndikanatha ndingozitenga izo ndi kuzipeza izo mmbuyo umu. Ine sindikudziwa mwa kutsimikiza ng—ngati ine ndingathe kapena ayi. Akazi a Woods, kodi inu mukukumbukira pamene ine ndinali kukusonyezani inu izo

tsiku lina? Basi zimene. . . Kodi umenewo unali mutu wa 5? Wa 5, a, ha. Chabwino.

*Ili ndi bukhu la obadwapo a Adamu. Mu masiku amene Mulungu anamulenga munthu, mu mafananidwe a Mulungu anamulenga. . . iye;*

*Mwamuna ndi mkazi anawalenga iye iwo; ndipo anawadalitsa iwo, ndipo anawatcha dzina lawo Adamu, mu tsiku limene iwo analengedwa.*

*Ndipo Adamu anakhala zaka zana ndi zaka makumi atatu, ndipo anabala. . . ana aamuna—ndipo anabala— anabala mwana mwa mafananidwe ake omwe, nd— ndipo motengera thunthu lake lomwe; ndipo iye anamutcha iye dzina lake. . . (Kaini? Ha-ha-ha-ha-ha! Kodi iye anamutcha dzina lake chiyani? Ali—alikuti mwana woyamba kubadwa amene anali nao maufulu akubadwa pamenepo? Sanayambe amutchula nkomwe iye. Seti anali mawna wake.)*

<sup>328</sup> Tsopano, ife tikubwera mpaka apa tsopano ndipo ife tikupeza pamene izo zinanenedwa. . . Ndipo Eva anapatsidwa mwana wamwamuna, chifukwa Kaini anamupha Abele. Tsopano zindikirani pamene ife tirikupitirira nazo. Adamu ndi masiku kuleng. . .

*Ndipo Adamu anakhala moyo zaka zana ndi atat— anakhala moyo zaka zana ndi makumi atatu, ndipo anabala mwana wamwamuna— anabala mwana wamwamuna monga mwa mafananidwe ake, motengera thunthu lake; ndipo anamutcha dzina lake Seti:*

*Nd—ndipo masiku a Adamu iye atatha. . . atabala Seti anali mazana asanu ndi atatu ndi. . . zaka: ndipo iye anabala ana aamuna ndi aakazi:*

*Ndipo masiku onse a Adamu alimoyo anali mazana asanu ndi anai ndi—ndi makumi atatu ndipo. . . zaka: ndipo iye anafa.*

*Ndipo Seti anakhala moyo. . . zaka zana ndi zisanu, ndipo anabala Enosi: . . . (Ndipo kuchokera apo kutsika mpaka izo zikupitirirabe mmusi, ndipo iye ali wachisanu ndi chiwiri, Enoki ali wachisanu ndi chiwiri kuchokera kwa Adamu.)*

Tsopano, ine sindikukumbukira basi pati mu Luka. Kodi inu muli napo mutalembapo nanunso, Akazi a Woods? Iye ndi ine. . . Ine ndimamuwonetsa iye zimenezo tsiku lina uko mu. . . Mukuti chiani? [M'bale Branham akambirana ndi Mlongo Woods—Mkonzi.] Ine ndikukhulupirira kuti inu mukulondola, Mlongo Woods. Ife tinapalemba apo uko mu bukhu lake, kumene ife tinali, Baibulo lake, kumene ine ndinali kumusonyeza. Ndi izi apa, eya, mafuko. Chabwino.

329 Tsopano, ife tizindikira apa . . . Mu mutu wa 3 wa Luka ife tikupeza chinthu chomwecho. “. . . ana amene ndi ena otero . . . ndi Nowa, amene anali wa Lameki, amenenso anali ana a Metusela, amene analinso mwana wa Enoki, amene anali mwana wa Yaredi, amene anali mwana wa Maleleeli, amene anali mwana wa Kanani, amene anali mwana wa Enosi, amene anali mwana wa Seti, amene anali mwana wa Adamu, amene anali mwana wa Mulungu.” Kodi Kaini anabwera umo pati? Kodi Kaini ali pati, woyamba kubadwa? Ufulu wa kubadwa pa iye; iye anachokera kuti? Iye anali mbewu ya Satana, ndipo osati ya Mulungu. Sanali wa Adamu, ngakhalenso chifukwa dzina la mwana wa Adamu lina—linali Seti. Kaini, mbewu ya serpenti, anamupha mwana wake woyamba amene anali choimira ndi mthunzi wa serpenti aponso kupha mwana wake winayo, Yesu. Ndipo Seti anatenga malo ake mwa obadwapo, amene ankanathauza chiukitsiro, kuti obadwapo a Mulungu akanati adzatengedwere patsogolo kwathunthu.

330 Ine ndikufuna kuti ndimuwone winawake amuike iye mmenemo tsopano ndi kuti iye sanali mbewu ya serpenti. Iye sanazindikiridwe mu obadwapo a Mulungu, kapena ngakhalenso mu obadwapo a mtundu wa anthu, obadwapo a Adamu, aliwonse a onse a iwo. Ndi kulondola uko? Ndi angati akukhulupirira zimenezo, munene, “Ameni!” [Osonkhana ayankha, “Ameni!”—Mkonzi.] Zedi. Iye sanali; iye anali mbewu ya serpenti ndipo osati mbewu ya Adamu!

331 Mkaziyo anati ameneyo anali mwana wa Adamu. Iye sanali mwana wa Adamu. Iye anati, “Ine ndamupeza iye kuchokera kwa Mulungu.” Ndipo iye ankayenera kuti atero, iyo inali mbewu. Iyo inali mbewu, koma iyo inali mbewu ya serpenti. Mukuona?

332 Ndipo Iye anachita kubwereranso mwa namwali ndiye polinga kuti adzayeretsepo mchitidwe wogonana uwo umene unali utachitidwa. Adamu anaikidwa pansu pano, koma iye an—iye anali asanzipeze kuti iye anali woti akhala bambo. Inu mukumvetisa zimene ine ndikutanthauza. Satana podziwa izi, iye anafika kwa Eva Adamu asanafikepo pamenepo. Ndipo apo ndi pamene chinthu chonse chagona lero. Ndipo m’bale, icho ndi chimene chikupangitsa chikwati ndi chilekano ndi china chirichonse kukhala zokanganira zotero momwe izo ziriri lero. Izo ndi zomvetisa chisoni kwambiri. Mukuona? Koma i . . . Mulungu wakonzana njira, kwa yemwe ife tiri othokoza kwambiri.

333 Kodi inu mukumukonda Iye? Kodi Iye si wodabwitsa? Tsopano, kodi mbewu ya serpenti ndi yolondola? Ine ndimaganiza mwina winawake pa tepi akanati . . . akhoza kuganiza kuti ine ndimaopa kuligunda ilo. Inu mukuona? Kotero iwo akanati, “Mwakuti, iye anazilambalala izo kawiri. Iye akuwopa basi kuti agwire pa izo.” Ife sitiri a zimenezo. Utali wonse Ambuye ali mu izo, izo zonse ndi zabwino.

Inu mukudziwa chiani? Momwe ine ndinanenera, kuti mphungu nthawi ija ine ndinkaiwona, ikusisita mapiko ake, inu mukudziwa. Ine ndinaganiza, “Kodi iwe sukuchita mantha ndi ine?” Ine ndinali nayo mfuti yanga ili pamenepo; ine ndinati, “Ine ndikanakhoza kukuwombera iwe.” Iye amadziwa kuti ine sindikadakhoza kumuwombera iye; ine ndinali kutali kwambiri ndi mfuti imeneyo. Ine ndinati, “Kodi iwe ukuchita mantha?” Iye anangophethiritsa maso ake aakuluwo ndipo anayang’ana pa ine. Kagologolo kakang’ono katakhala pamenepo kakuti, “Che, che, che, che, che; ine ndidzakukhadzula iwe mzidutswa, kukukhadzulira iwe mzidutswa!” Iye sanali kupereka chidwi kwa gologolo uyo, koma iye anatopa ndi kumvetsera pa iye. Kotero patapita kanthawi, iye anangopanga kukupiza kumodzi kwakukulu, anapita kwina monga choncho, ndipo anangotambasula mapiko ake. Ndipo iye ankadziwa kupendeketsa kwake mapiko amenewo, anangowuluka mpaka kosawonekanso. Mukuona? Ine ndinangomuwona iye akukhala pansu kanthu kakang’ono ngati choncho, kachidutswa kakang’ono basi.

<sup>334</sup> M’bale Fred, ine ndikukhulupiira ine ndinakusonyeza inu. Ine ndinamuwona M’bale Fred kumbuyo uko tsopano, pamene iye anafuula “Ameni!” kanthawi kapitako. I—ine ndikukhulupirira ine ndinakuwonetsani inu pamalo pamenepo kuntunda uko, ndi M’bale Woods, kulikonse kumene inu muli, komwe uko mmapiri pamwamba apo, kumene izo zinachitikira. Ine ndinaiwona mphungu imeneyo. I . . . Iye anakakamizidwira pansu mu mkuntho umenewo, ndipo ine ndinali nditaima kumbuyo kwa mtengo umenewu.

<sup>335</sup> Tinali kusaka mbawala (ndipo kenako mochedwerapo pang’ono), ndipo umu munali mu Okotobala, ndi chisanu ndi zinthu. M’bale uyu apa anali kuntunda kumeneko kulakatika masamba kwapitaku limodzi nafe, M’bale John ndi iwo, pamwamba pomwe pa Corral Peak ndiko kumene izo zinali.

<sup>336</sup> Ine ndinayima pamenepo, ndipo ine ndinaima paseli pa mtengo uwu. Chisanu chiri pang’ono pokha ndi mvula ikugwa pang’ono pokha, ndipo ine ndinali nditangoima pamenepo. Mphungu imeneyo itaima pamenepo, ndipo iye anali atakamizidwira pansu. Iye anawulukira mmwamba pamenepo, yaikulu, chinthu chowoneka ngati chirombo chachikulu, chachikulu, mphungu yabulauni. Itakhala pamwamba pamenepo ndipo inkayang’ana pozungulira, ine ndinaganiza, “Chabwino . . .” I—ine ndinali nayo nthawi yabwino kwenikweni. Ine ndinali kufuula, “Ambuye alemekezeke! Aleluya!” Kuzungulira zungulira zungulira thengolo ine ndinali ndikupita, ndikufuula monga choncho. Ine ndinayang’ana pansu apo; ine ndinkakhoza kumva nkhandwe yokalamba iyo ikufuula. Inu mukudziwa momwe izo zimafuulira.

337 Chaka chatha kumusi uko, pamene...basi isanayambe kuti izivumba, izo zinkayamba kufuula; iyo inali nkhandwe yaing'ono, inu mukudziwa. Ine ndimangokonda kuzimva izo.

338 Ndiye ine ndimakhoza kumva mbawala kutali uku, “Whiiiioo,” momwe iye amachitira. Ndipo kutali cha uku mzake kumuyankha iye. (Sabata yamawa, sabata pambuyo pa sabata, ine ndikhala ndikuzisaka izo, Ambuye akalola.) Kotero ndiye, kuzimva zimenezo cha kumeneko, o, ndi zaumulungu basi kukhala uli kuntunda kumeneko. O, i—ine basi...U—uko ndi kukachisi wanga kuntunda uko kumene ine ndimayankhula kwa Iye, ndiyeno nkubwera kumusi kuno ndi kudzayankhula kwa inu. Mukuona?

339 Ndipo mmwamba umo, o, ndi kodabwitsa kwambiri, kungomasuka basi. Nditangoima pamenepo, ine ndinaganiza, “O, Mulungu...” Ine ndinayang'ana, ndiye mvula inayamba kugwa, ndipo zobiriwira nthawizonse zinachita chisanu pa izo, ndipo utawaleza unasesa pamwamba pake kuchokera ku Corral Peak mpaka ku Sheep Mountain, pamwambapo njira *imeneyo*, kudutsa njira *imeneyo*. Ndipo ine ndinaganiza, “O, Mulungu, taonani apo. Unhu,” ine ndinaganiza, “ndi Inu apa, Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza. Apa iwo ukutsika ndi apa, apo. Inu ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse, Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri, Zoyikapo Nyali Zisanu ndi ziwiri za Golide. Ndi Inu pamenepo, Mulungu, kudabwitsa kwake komwe Inu muli.”

340 Ndipo ine ndinali ndikungofuula, ine ndinaikhazika mfuti yanga pansu; ine ndinali kuzungulira mtengo ndikufuula, “Ulemerero kwa Mulungu! Ambuye alemekezeke,” kuzungulira zungulira mtengowo monga choncho. Ine ndinali ndi nthawi yaikulu pamwamba apo mwandekha, Ambuye yekha ndi ine, inu mukudziwa.

341 Ndipo patapita kanthawi mphungu imeneyo inatulukira kuchokera mu tchire lambiri ilo ndipo iyo inkangoyang'ana pa ine. Ine ndinaganiza, “Chabwino, iwe sukuzikonda zimenezo?” Ine ndinati, “Mnyamata wokalambawe, ine ndikumupembedza Mulungu yemweyo amene anakupanga iwe.” Mukuona? Iye anangophethitsira maso ake aakulu kwambiri owoneka-motuwawo ndipo anayang'ana pozungulira inepo, ndi ine ndikufuula monga choncho.

342 Kagologolo kakang'ono, kokalamba ka mu paini (aliyense amene anayamba wasaka mu mapiri, i—iyeyo ndi wapolisi wa mu nkhalango), ndipo iye analumphira pamenepo (kanthu kokalamba kakang'ono, si kakakulu mokwanira kuti kangakhoze kuchita kanthu, koma o, phokoso lakelo)—ndipo analumphira pamwamba pamenepo, akulumphira mmwambandi-pansi, inu mukudziwa, “Ya, ya, ya, ya, ya, ya—ya, ya, ya, ya, ya, ya,” basi kumapitirira nazo monga choncho.

<sup>343</sup> Ndipo mphungu imeneyo inali kumuyang'ana iye; iyo inkakhoza kuyang'ana pa ine. Ine ndinaganiza, "Mai, Ambuye, chabwino, bwanji Inu mwandileketsa ine pa chinachake monga chimenecho?" Mukuona? Ine ndinati, "Chifukwa, Inu mukudziwa, ine ndinali ndikukupembedzani Inu. Inu mukufuna kuti ine ndiwone chinachake pa mphungu imeneyo?" Ine ndinati, "Ine ndimuphonzira iye, kapena kodi ndi pa gologolo wa mu painiyo?" Ine ndinaima pamenepo ndipo ndinkayang'ana iwo; ine ndinaganiza, "Ine ndimuphonzire iye mochepa pang'ono pokha." Ine ndinati, "Chinthu chimodzi ine ndinamuzindikira iye, iye sanali wamantha." Ine ndikukonda zimenezo, alibe mantha. Iye anaima pamenepo mbalame yaikulu kwambiri iyo; ine ndinati, "Iwe ukudziwa chiani?" (Mfuti yanga inali itaikidwa motsamira mtengo.) Ine ndinati, "Iwe ukudziwa ine ndikhoza kukuwombera iwe?" Iye ankadziwa bwinoko kuposa zimenezo; iye ankadziwa chinthu chimodzi: Ine sindikanatha kuchita zimenezo; ine ndinamuyamikira iye mochuluka kwambiri. Mukuona? Apo iye anali ataima pamenepo, osachita mantha mpang'ono.

<sup>344</sup> Ndipo ine ndinaganiza, "Ine ndikhoza kukuwombera iwe." Tsopano, ine ndinali nditamuwona iye; iye amakhoza kuyang'ana yang'ana mozungulira pa ine monga choncho. Ndipo iye anapitirira kuwapanga mapiko ake, inu mukudziwa, kupita mmbuyo. Inu mukudziwa momwe iwo amachitira monga choncho, mapiko awo, inu mukudziwa. Mapiko aakulu kwambiri pafupi kutalika *chonchi*, inu mukudziwa, ndipo iye anali chinthu chachikulu. Iye anali atakhala pamenepo, ndipo ine ndinkamuyang'ana iye. (Izo zinali mmbuyo momwe ine ndisanazidziwe zinthu izi; izi zinali zaka ndi zaka zapitazo, mwinamwake zaka twente zapitapo.)

<sup>345</sup> Ndipo ine ndinkamuyang'ana iye. Patapita kanthawi, ine ndinamuwona iye; ine ndinaganiza, "Akutani iye—akutani iye. . . Iye sakuchita mantha, kotero ine ndikuyamikira zimenezo. Koma nchiani chiri chaumulungu kwambiri pa mphungu yokalamba iyo?" Powona waukulu kwambiri uwo, mlomo wangowe ukutuluka monga choncho, ndi maso aakulu awo, ine ndinaganiza, "Mnyamata, iyeyu ndi mbalame yenyeni."

<sup>346</sup> Tsopano, palibe wina. . . Mphamba, ngati iye angayesere kuti amutsatire iye, iye angachite angaphwasuke. Palibe kalikonse kangathe kumutsatira iye. Ayi, ayi! Izo zingatengere ndege kuti ichite zimenezo. Inde, bwana! Palibe mbalame ingathe kumutsatira iye, kotero, iye amapita pamwamba kwambiri. Ndiyeno, iye ali nao maso; iye angathe kuyang'ana mpaka pansa pa nthaka aponso, iye ali kale mmwamba umo, kuwona kutali komwe.

<sup>347</sup> Tsopano, Yehova anawafanizitsira aneneri Ake kwa mphungu (inu mukuona?); Iye amakhoza kuwanyamulira

iwo mmwamba monga choncho. Iwo amayenera kuti akhale opangidwa mwapadera. Tiyeni tiwone. Okonzedweratu, obadwira cholinga chimenecho (mukuona?), kumanyamulidwira mmwamba monga choncho. Ndiyeno inu... Ndi cha ubwino wanji iwe kupita mmwamba umo ngati iwe sungathe kuwona kumene iwe uli? Mukuona? Ndi cha ntchito yanji kukafika mmwamba umo ngati iwe sukudziwa chimene iwe ukuchita? Mwaona, mukuona?

<sup>348</sup> Ndi cha ntchito yanji kumalumphira mmwamba-ndi-pansi, ukufuula ndi kuyankhula mu malirime, ngati iwe sukudziwa kuti zonsezo ndi zachiani? Mwaona, mukuona? Iwe uyenera kuti uzizimvetsa pamene iwe uli mmenemo. Mukuona?

<sup>349</sup> Kotero ndiye, ine ndinamuyang'ana iye, inu mukudziwa, pamene iye ankasuntha cha pamenepo. Ine ndinapitirira... ine ndinkangomuyamikira iye; iye anali mbalame yokongola chotero. Ndipo komabe, iye mwinamwake akanadya ina ya nyama yanga ya gwape ndi zinthu zimene ine ndiri... ine ndinamuyang'ana iye, ndipo patapita kanthawi ine ndinaganiza, "Iwe ukudziwa, chiani—kodi iye akuti..."

<sup>350</sup> Patapita kanthawi iye anafika potopa. Ine sindikuganiza kuti iye anatopa ndi kuyang'ana pa ine, koma ine ndikuganiza iye anali atatopa kumvetsera kwa kagologolo kokalamba kakang'ono ako atakhala pamenepo. Inu mukudziwa, ife tiri nawo ochuluka kwambiri a iwo mu msasa lero. Inu mukudziwa? Mukuona? "Che, che, che! Masiku a zozizwitsa anatha! Palibe chinthu chotero ngati machiritso auzimu. Palibe zinthu zimenezi panonso!" Mukuona? Kagologolo kokalamba kakang'ono kamene kakhala pa chitsa chimenecho. "Iwe uyenera kukhala wa mu *ichi*. Ife—nd—ifefe ndi..." Mukuona? Atakhala pamenepo basi akupanga phokoso chokweza-ndi-chotsika. O, iye anali akututuma, iye anali akunjenjemera molimbika kwambiri.

<sup>351</sup> Iye anafika potopa ndi kumvetsera kwa izo, ndipo iye anangopanga kulumpha kumodzi kwakukulu, kwamphamvu, ndipo anagwedeza basi nthambi imeneyo pamene iye anali atakhalapo, monga choncho. Nthambiyo inagwedezeka, monga choncho, ndipo iye anapita kwina pamenepo. Mwaona, iye anakupiza mapiko ake ndipo anangochokapo kudutsa mu mitengo imeneyo uko. Ndipo pamene iye anatero, ine ndinamuzindikira iye. Mukuona? Iye sanali wamantha, chifukwa iye ankakhoza kumverera kukhalapo kwa mapiko ake opatsidwa ndi Mulungu. Iye ankadziwa kuti mapiko amenewo akanakhoza kumunyamulira iye kutali kuchoka ku chowopsya cha mtundu uliwonse. Mukuona?

<sup>352</sup> Ndipo kotero, umo ndi momwe ife tikufuna kuti tizimverera. Awa ndi Mawu, ndipo Iye amene anawalemba Mawu ndiwo Mapingo anga. Ine sindimachita nawo mantha Mawu; Iwo



azikunyamulirani inu kudutsa vuto la mtundu uliwonse limene liripo. Iwo ndi Lupanga limene lingadule njira Yake molunjika kumene nkudutsa. Musati inu muzidandaula konse ndi zimenezo. Mukuona?

<sup>353</sup> Ine ndinamuzindikira iye pamenepo. Iye sanali kukupiza, iye anangotambasula mapiko ake. Mukuona? Ndipo iwo, nthawi iliyonse mphepo imabwera umo, iye amangokwezedwa mmwamba, amapita mokwererapo ndi mokwererapo.

Ine ndinaima pamenepo, ndipo ndinapinda mikono yanga, ndipo ndinayang'ana pa iye mpaka iye anangokhala kadontho kakang'ono ine sindinkatha kumuona nkomwe kenanso. Ndipo ine ndinaganiza, “Mulungu, izo ndizo” Si kuthamanga kukajowina *ichi*, ndi kuthamanga kukajowina *icho*, ndi kuchita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*, ndi kungotambasula mapiko ako (mukuona?); kudziwa momwe ungamambasulire mapiko ako a chikhulupiriro mu Mawu a Mulungu, ndi kuyandama kuchoka kwa zachabechabe zonse izi za kulongolola longolola apa ndi kulongolola longolola apo. Eya! “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera konse.”

<sup>354</sup> Tsopano, ine ndiri nawo pafupi makumi awiri a inu madzulo ano. Tsopano, inu amene muli pa...ndizo zolankhulana zapadera za madzulo ano, ndiye, inu mumuwone Billy, chifukwa ine ndikuganiza iwo ayesera kuti ayambe molawirira pang'ono basi kuti ine ndidzawatengere onsewo umo. Ngati ine ndingathe, ine ndikufuna ndimutenge aliyense wa iwo amene ali otheke kuti ine ndingamutenge. Ndipo ine ndinachita ichi, osati chifukwa...Billy samadziwa izi, onani, koma malingaliro anga anali atamangika kwambiri atatha pafupi masomphenya makumi awiri mkati umo mmawa uja, inu mukuona, mpaka izo...kapena chirichonse chimene icho chinali. Izo zimakhala ngati zimakutengera iwe mu...Ndipo Billy anati, “Bwanji inu simukupita kunja ndi kukatenga pang'ono...Mukatakasuke, kupita panja, ndi kukayankha ena a mafunso amenewo uko.”

Ndipo ine ndinati, “M'bale Neville ali ndi uthenga wake.”

Anati, “Ine ndipita kuti ndikamuze iye.” Iye anapita uko.

M'bale Neville anati, “Bwerani nazo!” Koteri ndiye, Ine ndinauka ndipo ndinabwera kunoko. Ndipo ena a iwo akuyembekezera kwa madzulo ano. Pepani ine ndakusungani inu pano mpaka 1:00 koloko, koma ine ndikhala ndiri...ndikuganiza ndiyenera kuti ndichoke nkucha, chotero kuti ndibwerere ku Arizona aponso.

<sup>355</sup> Kumbukirani, Ambuye akalola, nthawi yotsatira ine kubwerera, ine ndikufuna kuti ndidzalalikire pa, kwa inu za... kukusonyezani inu mu Lemba kulondola kwa chikwati ndi chilekano. Izi...Ndipo tsopano...Ndiyeno, ndidzangozisiya izo basi...Kungoziyala izo apo basi momwe izo ziliri kwenikweni, ndiye inu muziwona izo kuyambira pamenepo.

Kotero kufikira nthawi imeneyo, khalani olimbika mtima mwabwino; Ambuye akudalitseni inu molemera kwenikweni. Kodi ife tingaime? [Ulosi uli kuperekedwa kuchokera kwa dona mwa osonkhana—Mkonzi.] Ambuye alemekezeke.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye, (Inu muli?)  
Poti anayamba kundikonda,  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

356 Inu mukumukonda Iye? Tsopano, tiyeni tigwirane chanza wina ndi mzake, pamene ife tikuyiimba kachiwiri.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye,  
Poti anayamba kundikonda,  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

357 O, kodi izi si zodabwitsa? O, mai! Billy amafuna kuti ine ndilengeze, kuti akatha madalitso, iye ali ndi mawu oti anene kwa inu anthu pano amene mukufuna zoyankhulana zapadera izo. Inu mukuona? Iye akufuna kuti akomane nanu basi mu maminiti ochepa. Koma ine ndikumverera pakali pano, mphindi chabe ya kupembedza. Awa . . . Kodi inu simumakonda kumupembedza Iye mu Mzimu?

Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

358 O, kodi izi si zodabwitsa? O, i—ine ndikumukonda Iye. Mu mtima mwanga ine ndikumukonda Iye, ngati ine ndikuwudziwa mtima wanga. Ine ndikukhulupirira inu mukutero nanunso. Kotero palimodzi ife ndife ana Ake. Ife timakondana wina ndi mzake. Tsopano, ine sindingati ndizimukonda Iye popanda kukukondani inu. Ndipo ngati ine ndikunena kuti ine ndimamukonda Iye ndipo nkusamakukondani inu, Baibulo linati ine ndine wabodza. Mukuona? Ndipo ngati i . . . Ngati inu mukufuna k—ngati inu mumafuna kuti muzindikonda ine kapena kulikonda banja langa . . . Kusankhako kunali, kodi ine ndikufuna kuti inu muzichita chiani, muzindikonda ine kapena muzilikonda banja langa; inu muzilikonda banja langa. Ine kulibwino inu mukanamamukonda Billy Paul kuposa kundikonda ine. Ngati izo zitafika pa chiwonetsero cha mtundu umenewo, ine kunali bwino inu mukanamachita zimenezo. Ine ndikufuna kuti inu muzimvetsera kwa ine, chifukwa Billy si mtumiki. Koma ine ndikufuna kuti inu muzimvetsera kwa ine, zimene ine ndikukuuzani inu; koma pamene . . . ngati inu mukufuna kuti muzimukonda winawake, kuwakonda kwenikweni iwo, inu mungati, “Ine ndikufuna kuti maka ndizikukondani inu kapena Billy,” inu muzimukonda Billy. Mukuona? Mulungu amamverera mwanjira yomweyo pa za ife. Ndipo ife sitingati . . . Ndiye ine ndikudziwa kuti inu simungati muzimukonda Billy popanda kundikonda ine, chifukwa iyeyo

ali gawo la ine. Mukuona? Koteru ine sindingati ndizimukonda Mulungu popanda kukukondani inu, chifukwa inu ndinu gawo la Mulungu. Ndipo ife timakondana wina ndi mzake. O, ine ndikuganiza kuti izo ndi zodabwitsa kwambiri. Kodi inu simukuganiza kuti nyimbozi ziri chinachake chokongola ife titatha kukhala nazo izi, kuyankha zinthu zimenezi, pamene izo zimatiyika ife mu kupiringizika? Anha, anha, o zenizeni kwambiri.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye,  
Poti anayamba kundikonda,  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

O, iwo azidzachokera kummawa ndi . . .



*Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo*, Bukhu Lachiwiri  
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume Two)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)